

ZOCHITIKA MCHAKA CHOYAMBA CHA

LIVING WORD MISSIONS

BIBLE SCHOOL

Maphunziro awa atanthauziridwa m'chichewa kuchokera mchingerezi ndi utumiki wa:

Good News Revival Centre, P.O. Box 56, Mikolongwe, Malawi; mothandizidwa ndi:
Maranatha Publishers, P.O. Box 90168, Bangwe, Blantyre 9, Malawi; yomwe ndi gawo limodzi la utumiki wa *Good News Revival Centre*.

Abale ena anazipereka kwambiri kundithandiza ntchito yomasulirayi osaiwala mbale **Frank Mapondo** yemwe ndi mbale wa pa Computer yathu. Iyeyu wagwira ntchito yaikulu usana ndi usiku kuika mu Computer maphunziro ozamawa. Ndipo ndi pemphero langa kuti Ambuye agwiritse ntchito maphunziro amenewa kubweretsa Malawi kwa Ambuye.

Ine mtumiki mzanu chifukwa cha Yesu,

Nedson W. Milanzi.

Russ Tatro, mtsogoleri wa Living Word Missions wakhala akutumikira Ambuye ku minda ya utumiki kuyambira m'chaka cha 1985, wayambitsapo malo ophunzitsirapo mau a Mulungu m'maiko aku madzulo a Africa. Utumiki wafika kale ku maiko 11 ndi ophunzira opitirira 10, 000. Mazana a iwo amene atsiriza maphunzirowa tsopano ali kuphunzitsa choonadi cha m'Bukhu Lopatulika kwa ana a sukulu opitilira 125, 000 pa sabata iliyonse.

MAU OTSOGOLERA

Maphunziro khumi, asanu ndi limodzi (16) otsatirawa akhala akugwiritsidwa ntchito m'sukulu zophunziriramo mau a Mulungu zosiyanasiyana ku madzulo kwa Afrika (West Africa) kuyambira mchaka cha 1987. Izi ndi zochitika za m'chaka choyamba zomwe zaphunzitsa zikwi za ophunzira.

Maphunziro awa anakonzedwa kuti akhale zida zomwe ophunzira angathe kuphunzitsira gawo losankhika limodzi la maphunziro, kaya ndi mu Sande sukulu, mu mpingo, mu msonkhano waukulu, kapena mu Bible School. Gwiritsani ntchito monga umo mufunira. Mutha kugwiritsa ntchito maphunziro onse kapena gawo lochepa limene likupezeka m'maphunzirowa pofuna kudalitsa ena.

Pemphero lathu ndilo lakuti maphunziro awa agwiritsidwe ntchito polimbikitsa ofooka, kulimbikitsa omwe ataya mtima, ndikutsegulira maso akumvetsetsa ku choonadi cha mau a Mulungu.

Mu ntchito yake,

A handwritten signature in black ink that reads "Russ Tatro". The signature is written in a cursive style with a long horizontal stroke extending to the right.

Russ Tatro.

ZIPHUNZITSO ZA MBUKHU LOPATULIKA

- I. CHIPHUNZITSO NDI CHIYANI?**
- II. CHIFUKWA CHIYANI KUPHUNZIRA ZA CHIPHUNZITSO KULI KOFUNIKIRA?**
- III. MALEMBA**
- IV. AMBUYE YESU KHRISTU: CHIKHALIDWE CHAKE**
- V. MAUTUMIKI A YESU - LOPATULI KAZA MBUKHYESAYA 6:1,11:1-3)**
- VI. UTUMIKI WA LERO WA YESU KHRISTU**
- VII. UTUMIKI WA MTSOGOLO WA KHRISTU**
- VIII. CHIPULUMUTSO**
- IX. KUYERETSEDWA (KUPATULIDWA)**
- X. MPINGO**
- XI. KODI YANKHO LANU LIKHALA LOTANI?**

PANGANO (MGWIRIZANO) LA MWAZI

- I. PANGANO LA MWAZI NDI CHIYANI?**
- II. ZIFUKWA ZOLOWERA MU PANGANO LA MWAZI:**
- III. NJIRA ZOLOWERA MU PANGANO LA MWAZI:**
- IV. ZOCHITIKA (MAKWERERO) POLOWA MU PANGANO LA MWAZI**
- V. PANGANO LATHU LA MWAZI NDI MULUNGU.**
- VI. BAIBULO LIRI NDI ZIPANGANO ZIWIRI KAPENA KUTI MAPANGANO AWIRI: PANGANO LAKALE NDI LATSOPANO.**
- VII. CHOSOWA CHA MUNTHU POFUNA MPULUMUTSI**
- VIII. TILI NDI PANGANO LOPAMBANA (LABWINO LOPOSA) CHIFUKWA CHA YESU.**

IX. PANGANO LATSOPANO NDI PANGANONSO LA MWAZI CHIKHALIDWE CHA MULUNGU

- I. MAGWERO A VUMBULUTSO**
- II. ZOCHITIKA ZA MULUNGU (ZOSAKHALA ZA UMUNTHU)**
- III. ZOCHITIKA ZA MULUNGU (ZA UMUNTHU)**

IV. TANTHAUZO LAKE LAMULUNGU

**V. CHIKHALIDWE CHA MULUNGU CHIVUMBULUTSIDWA
KUPYOLERA M'MAINA AKE.**

**VI. MAINA ASANU NDI AWIRI (7) A MULUNGU OFOTOKOZA ZA
CHIOMBOLO**

VII. MAINA ENA

UDINDO (KAPITAWO) WA CHIKHRISTU

I. KUONA KOYENERA (KUMVETSETSA)

**II. MULUNGU AMAFUNITSITSA KULEMELETSA ATUMIKI AKE -
DEOTORONOMO 28**

III. ZOOPSA ZOGWIRIZANA NDI ULEMERERO

**IV. MAFUNGULO (MAKIYI) OLOWERA MU ULEMERERO WA
M'BUKHU LOPATULIKA (BAIBULO)**

**V. MALAMULO OCHITIKA AKUPEREKA NDI KULANDIRA
CHIPHUNZITSO CHA ZIWANDA**

**I. SATANA ANALI KUMWAMBA MONGA LUSIFALA (EZEKIELI
28:1-19).**

**II. SATANA NDI ZIWANDA ZAKE AKUGWIRABE NTCHITO
MPAKA LERO**

III. YESU ANAGONJETA SATANA (AKOLOSE 2:15)

**IV. NJIRA ZISANU NDI ZIWIRI (7) ZOMWE SATANA
AMAZIGWIRITSA NTCHITO POLIMBANA NAFE**

V. MAINA A SATANA

VI. MAINA A MIZIMU YOIPA

**VII. UMO M'MENE UNGATETEZEKERE MKATI KATI MWA
NKHONDO YA UZIMU**

MAU OTSOGOLERA KUKUKHALA WOPHUNZIRA

I. MAU OTSOGOLERA KUKUKHALA WOPHUNZIRA

**II. ZOLINGA PA KUPANGA ENA KUKHALA OPHUNZIRA:-
KUPITITSA MTSOGOLO UFUMU WA MULUNGU**

III. ZIMENE YESU ANAPHUNZITSA PA KUKHALA OPHUNZIRA

IV. UMO M'MENE YESU ANAKONDERA NDI UMO M'MENE

ANAYENDERA - WOPHUNZIRAKUKHAL

KUKHALA WOPHUNZIRA

I. UBWINO WA CHIPANGANO CHATSOPANO POYEREKEZA NDI CHAKALE.

II. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI MATEYU

III. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI MARKO, WOLEMBEDWA MCHAKA CHA 67-70 YESU ATABADWA

IV. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI LUKA MCHAKA CHA 62 YESU ATABADWA

V. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI YOHANE MCHAKA CHA 80-90 YESU ATABADWA

MACHIRITSO OCHOKERA KUMWAMBA

I. ADAMU NDI HAVA M'MUNDA WA EDENI.

II. MACHITIDWE A MULUNGU MU CHIPANGANO CHA KALE.

III. ANAYAMBITSA MATENDA NDANI?

IV. YESU KHRISTU MCHIRITSI

V. NJIRA ZAPAFUPI ZISANU NDI ZIWIRI ZOMWE MULUNGU AMACHIRITSIRA

VI. KUCHITA PA MAU A MULUNGU

UTUMIKI WOFALITSA UTHENGA WABWINO

I. UTUMIKI WOFALITSA UTHENGA WABWINO UFOTOKOZEDWA (LUKA 19:10)

II. ZIDA ZOGWIRITSIRA NTCHITO POFIKIRA ENA NDI UTHENGA WABWINO

III. NJIRA ZOTHANDIZA POCHITIRA UMBONI

MAUTUMIKI OCHITIKA

I. MAU OYAMBA: KUFOTOKOZA MAUTUMIKI OCHITIKA

II. KUITANA KWA MULUNGU

III. MBALI (MADERA) ZOCHITACHITA ZA UTUMIKI

IV. MAYESERO

V. ZOLIMBANA (NKHONDO)

VI. KUPAMBANA MU UTUMIKI

MAZIKO A CHIKHULUPIIRO

I. CHIKHULUPIIRO NCHIYANI? TIMACHIPEZA BWANJI CHIKHULUPIIRO?

II. UMO M'MENE TINGAKULILE MCHIKHULUPIIRO (2 ATESALONIKA 1:3)

III. ADANI A CHIKHULUPIIRO

MZIMU WOYERA

I. MZIMU WOYERA NDI NDANI?

II. UMULUNGU (ATATE, MWANA NDI MZIMU WOYERA)

III. ZIZINDIKIRO, MAKHALIDWE AKE, NDI ZINTHU ZINA ZOKHUDZANA NDI MZIMU WOYERA.

IV. MZIMU WOYERA M'KUBADWA MWATSOPANO NDI UBATIZO WA MZIMU WOYERA

V. CHIYANJANO CHA MZIMU WOYERA (ZAKARIYA 4:6; 2 AKORINTO 13:14)

MAU OYAMBIRIRA AKU UTUMIKI

I. MITUNDU ITATU YA MPHATSO

II. MPHATSO ZA UTUMIKI

III. MTUMWI

IV. MNENERI

V. MLALIKI

VI. MBUSA

VII. MPHUNZITSI

VIII. UTUMIKI WA MATHANDIZO

IX. KUTSILIZA/KUMANGIRIRA

KUMVERA

I. MAU OTSOGOLERA A KUMVERA

II. KUMVERA: MPHAMVU IMODZI YOKHA YA KU MPALADIZO (GENESIS 2:16-17; 3:11)

III. KUPHUNZIRA CHINSINSI CHA KUMVERA KWENIKWENI (AHEBRI 5:8,9)

PEMPHERO

- I. KUFUNIKA KWA PEMPHERO
- II. ZIMENE PEMPHERO SILIRI (MATEYU 6:5-8)
- III. CHIMENE PEMPHERO LIRI
- IV. ZOMWE YESU ANANENA ZA PEMPHERO
- V. ZIMENE PAULO ANANENA ZA PEMPHERO
- VI. ENA ANENA ZOTANI PEMPHERO
- VII. MAPEMPHERO MCHIPANGANO CHATSOPANO

CHILUNGAMO

- I. CHIFUKWA CHOMWE MPINGO WALEPHERERA
- II. KUBWEZERETSEDWA KWA CHILUNGAMO
- III. MITUNDU IWIRI YA CHILUNGAMO (AFILIPO 3:9).
- IV. KUYENDA MCHILUNGAMO CHAKO
- V. ZIPATSO ZA CHILUNGAMO
- VI. M'MENE MULUNGU ANATIPANGIRA IFE KUKHALA

OLUNGAMA

KUMVETSETSA ULAMULIRO

- I. KUGONJERA KU ULAMULIRO, CHOFUNIKIRA KU MOYO WOPAMBANA WA CHIKHRISTU
- II. MAULAMULIRO OKHAZIKITSIDWA NDI MULUNGU (ULAMULIRO WODZIWIKA)
- III. ULAMULIRO WOPEREKEDWA (ULAMULIRO WOSADZIWIKIRA)

ZIPHUNZITSO ZA MBUKHU LOPATULIKA

I. CHIPHUNZITSO NDI CHIYANI?

- A. Mwa tchutchuchu (mu zoonadi) chitanthauza "chinthu chophunzitsidwa" kapena "langizo (mwambo).**
- B. Kuphunzira za Mulungu ndi za chipembedzo "ndi zoonadi zenizeni za Baibulo zoikika mdongotsolo labwino."**
- C. Kusiyana pakati pa "chiphunzitso" ndi "mtundu wa chikhulupiriro."**
 - 1. Chiphunzitso ndi vumbulutso la Mulungu la choonadi monga chopezeka m'malemba.
 - 2. Mtundu wa chiphunzitso ndi zolankhula za munthu pa choonadi chimenecho monga chokhazikitsidwa mu mgwirizano (umodzi) wa chikhulupiriro (mwa chitsanzo, umodzi wa chikhulupiriro cha Atumwi).

II. CHIFUKWA CHIYANI KUPHUNZIRA ZA CHIPHUNZITSO KULI KOFUNIKIRA?

- A. Nchofunikira pa chitukuko (chikhazikitso) cha chikhaliidwe. Chomwe munthu amachimvetsa ndi kuchikhulupirira, chili ndi mphamvu m'machitidwe a chikhaliidwe chake.**
- B. Chimatchinjiriza (kuteteza) ku kulakwitsa (Mateyu 22:29; 2 Timoteo 4:2-4).**
- C. Nkoyenera kupindula kuona kwabwino kwa zoonadi za Baibulo zomwe zili zobalalika mbali zosiyanasiyana za Baibulo.**

III. MALEMBA

A. Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu (2 Timoteo 3:16).

- 1. "Mulungu - adapumira" - Liu la Chihelene loti "Theopheustos."
 - a. Monga momwe cholankhula cha munthu chimanenedwa kupyolera pakamwa pa munthu.
 - b. Monga munthu woimba akuimba chitolilo (fuluti) chake.
- 2. Zisonyezo (Maumboni)
 - a. Ulembedwe uwiri(mwa chitsanzo Marko 12:36 pamene mzimu ukunenedwa kukhala mlembi wa chomwe David analemba pa Masalimo 110).
 - b. Mulungu anawayang'anira koma sanawalembetse mau ndi mau pa zinthu izi kupatula pa zinthu zochepa zokha, monga ngati Malamulo Khumi.
 - c. Ngakhale kuti Mulungu anagwiritsa ntchito alembi a umunthu ndi pa mchitidwe wa iwo payekhapayekha, lye anawatetezera kuti asalakwe (sayenera kulakwa).
 - d. Baibulo silingosenza mau a Mulungu kokha mkati mwake, koma kuti liri mau a Mulungu.
 - e. Lemba lina liri lonse ndi louziridwa, si lingaliro lake lokha (mchitidwe wa kuuzira).

B. Yesu ankaona bwanji malemba?

- 1. Kufunikira kwa chilembo china chili chonse (Mateyu 5:18).
- 2. Timalakwa pamene sitidziwa malemba, ndime 29 (Mateyu 22:23-32).
- 3. David analemba mwa Mzimu, ndime 43 (Mateyu 22:41-46).

4. Malemba ali osatha (Mateyu 24:35).
5. Ali mzimu ndi moyo (Yohane 6:63).
6. Ali oyenera kuwamvera (Mateyu 5:19).
7. Mau akuwafanizira ndi kudya chakudya (Mateyu 4:4).

C. Atumwi ankaona bwanji malemba?

1. Paulo ndi Petro
 - a. Ouziridwa ndi opindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha mchilungamo (2 Timoteo 3:16).
 - b. Adzampanga munthu kukhala wa nzeru zofikira ku chipulumutso (2 Timoteo 3:15).
 - c. Palibe chinenero cha lembo chitanthauzidwa pa chokha (2 Petro 1:20).
 - d. Lupanga lakuthwa konsekonse la Mzimu (Aefeso 6:17).
 - e. Liyenera lemba likwaniritsidwe (Machitidwe a Atumwi 1:16).
 - f. Lemba lonenedwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 1:16)
2. Yakobo ndi Yohane.
 - a. Malembo sangonena chabe (Yakobe 4:5).
 - b. "Palibe munthu adzaonjeza kapena kuchotsera ku mau a bukhu ili, chifukwa Mulungu azamchotsera gawo lake mbukhu la moyo (Chibvumbulutso 22:18-19).

D. Kusiyanana kwake kwa Bukhu Lopatulika ndi mabukhu ena onse

1. Lolembedwa nthawi yopitirira pa zaka 1600 ndi mibadwo makumu anayi (40)
2. Lolembedwa ndi alembi opitirira makumi anayi (40) kuchokera mkusinkha kulikonse kwa moyo (mafumu, chilengedwe (ophunzira kapena kuphunzitsa za chilengedwe), alakatuli, atsogoleri a ndale, ophunzira sukulu, ndi ena otere).
3. Lolembedwa m'maiko akuluakulu atatu; Afirika, Asiya ndi Ulaya. Lolembedwa mzilankhulidwe zitatatu; chi hebri, chi aramu, ndi chihehlene.
4. Lokhala ndi maphunziro ovuta kuwamvetsetsa, olembedwa mogwirizana ndi mosalekeza.
5. Lokhala ndi umodzi wa mfundo ndi cholinga chomwe chingathe kulongotsoledwa ndi nzeru za woyang'anira m'modzi yekha, ndiye Mzimu Woyera.
6. Ndi la nthawi zosatha. Limodzi mwa mabuku akalekale koposa, ndiponso latsopano moposa ena onse.
7. Kutsimikizira kuti ndi louziridwa. Limagwira ntchito!

IV. AMBUYE YESU KHRISTU: CHIKHALIDWE CHAKE

A. Mwana wa Mulungu ndi wosiyana ndi ena onse.

1. Zivomerezo(Zitsimikiziro) za Yesu:
 - a. Wochokera kwa Mulungu (Yohane 16:28).

- b. Chidziwitso cha kwa Mulungu ndi chiyanjano (Mateyu 11:27).
- c. Kuonetsera Atate mwa lye yekha (Yohane 14:9-11).
- d. Maonekedwe a umulungu
 - 1) Wopezeka paliponse (Mateyu 18:20)
 - 2) Mphamvu yakudzutsa akufa (Yohane 5:21)
 - 3) Mphamvu yakukhululukira machimo (Marko 2:5-10).
 - 4) Mphamvu ya kuweruza munthu (Yohane 5:22).
- 2. Ulamuliro wa Khristu.
 - a. Analankhula ndi ulamuliro wa Mulungu wamphamvu zonse (Mateyu 7:24-29).
 - b. Yesu sanagwiritsepo ntchito malankhulidwe monga "Ili ndi ganizo langa," "Mwinamwache," kapena "ndikuganiza".
- 3. Kupanda ntchimo kwa Khristu - kusapezeka konse ndi maganizo kapena chivomerezo cha tchimo m'mau kapena mu tchito za Yesu (Yohane 8:46; 1 Petro 2:22).
- 4. Umboni wa ophunzira pamodzi ndi wa Yakobo mbale wake wa Yesu.
 - a. (Yohane 1:1-3, 20:28; Machitidwe a Atumwi 2:33-36).
- 5. Kuuka kwa akufa: Yekhayo amene ali wochokera kwa Mulungu angathe kugonjetsa imfa.

B. "Mau" ndilo dzina lina la Yesu (Yohane 1:1-3,14).

- 1. Liwu ndi chioneysero cha maganizo a munthu, njira zimene iye amazilumikizira ndi kuzionetsera yekha.
- 2. Yesu ndi "Mau" chifukwa amaonetsera (kuvumbulutsa) Mulungu (Ahebri 1:1-3).
- 3. Monga "Mau," Yesu ndi wamuyaya (wosatha) (Yohane 1:1, 14).
- 4. Monga "Mau", Yesu ndi m'modzi wa olenga wa dziko la kumwamba ndi lapansi ndi wogwiritsa zinthu zonse pamodzi (Yohane 1:3, Ahebri 1:3).

C. Mwana wa munthu.

- 1. Yesu anali munthu ndithu, koma analibe chikhalidwe cha uchimo (1 Petro 2:22).
- 2. Mwa thupi: Momwe Mulungu Mwana (Yesu) anakhala munthu mwa kubadwa mwa namwali.
 - a. (Yesaya 7:14; Mateyu 1:23; Luka 1:27-35).
 - b. Cholinga chokhala m'thupi.
 - 1) kuti aonetsere Mulungu kwa anthu (Yohane 1:14).
 - 2) kuti apereke chitsanzo pa makhalidwe (Yohane 13:15).
 - 3) Kuti apereke nsembe chifukwa cha machimo (Ahebri 10:1-12)
 - 4) kudzaononga ntchito za mdierekezi (1 Yohane 3:8).

5) kuti athe kukhala wa nsembe wamkulu wa chifundo ndi wokhulupirika (Ahebri 5:5-6).

c. Zitsimikizo za umunthu wake.

1) Anali ndi thupi la umunthu (Yohane 1:14; Agalatiya 4:4).

2) Anali ndi moyo wa umunthu (Mateyu 26:38) ndi mzimu (Luka 23:46). Sanali theka lina munthu ndi theka lina Mulungu, koma anali munthu wa thunthu (wangwiro) ndi Mulungu wa thunthu.

3. Anali ndi makhalidwe a umunthu.

Anamva njala (Mateyu 4:2). **Anatopa** (Yohane 4:6). **Anamva ludzu** (Yohane 19:28).

Analira (Yohane 11:35).

D. Maonedwe ABODZA okhuzana ndi chikhalidwe cha Khristu.

1. Anali woimirira wa mkulu wa olengedwa onse (mboni za Yehova, akhristu osakhulupirira za utatu mwa Mulungu m'modzi).

2. Anangoonekera kukhala ngati munthu, koma sanali munthu weniweni (Docetists).

3. Anakhala ngatiwa Mulungu pa ubatizo wake (osakhulupirira Atate Mwana ndi Mzimu ngati Mulungu m'modzi).

E. ZONADI ZAKE

1. Anali Mulungu mwa thunthu ndi munthu mwathunthu.(wokwanira)

2. Makhalidwe awiri analumikizana mwa munthu m'modzi popanda kuchita chikhalidwe cha chitatu.

3. Yesu anali wopanda tchimo (wopanda chifukwa).

V. MAUTUMIKI A YESU - MUNTHU WODZODZEDWA (YESAYA 6:1,11:1-3)

A. Mneneri (Mateyu 13:57).

1. Mneneri ndi munthu yemwe amagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuvumbulutsa ndi kupereka uthenga wake kwa munthu. Amaimirira m'malo mwa Mulungu kwa munthu.

2. Yesu anaonetsa njira yothawira cholakwa cha tchimo kwa dziko ndi kwa munthu aliyense payekha.

3. Yesu anatsutsa tchimo, analalikira chilungamo ndi kulamulira kumvera ku Mau a Mulungu.

B. WANSEMBE (Ahebri 5:1-10).

1. Wansembe ndi wopatulidwa mwa umulungu kuti aimirire munthu pamaso pa Mulungu ndi kupereka nsembe m'malo mwa munthu (Ahebri 8:3).

2. Yesu anazipereka lye yekha, nsembe, pa mtanda wa Kalvari kuti akalandilire chikhululukiro cha machimo kwa munthu.

3. Yesu ali wa moyo chikhali kupembedzera munthu (Ahebri 7:25).

C. Mfumu (1 Timoteo 6:15)

1. Mfumu amalamulira dziko lake (ufumu) ndikukhala ndi ulamuliro waukulu.
2. Ufumu wake suli wa pansu pano, wosakhazikitsidwa ndi mphamvu ya munthu. Ambiri amakana ulamuliro wake, koma tsiku liri nkuza pamene bondo liri lonse lidzapinda ndi lilime lirilonse lidzavomereza kuti lye ali Ambuye (Afilipi 2:9-11).

VI. UTUMIKI WA LERO WA YESU KHRISTU

- A. Kupempherera anthu ake (Ahebri 7:25).**
- B. Kukonza malo a kokhala kwathu ku nthawi zosatha (Yohane 14:3)**
- C. Kumanga mpingo womwe ndi thupi lake (Mateyu 16:18).**
- D. Kukhala ndi kupereka mphamvu mwa okhulupirira aliyense (Agalatiya 2:20).**
- E. Kuyankha mapemphero a anthu ake (Yohane 14:12-14).**

VII. UTUMIKI WA MTSOGOLO WA KHRISTU

- A. Akubwera kuzatenga mpingo wake mu mkwatulo (1 Atesalonika 4:13-18).**
- B. Kutsanulidwa kwa mkwiyo wa Mwana wa nkhusa pa dziko lapansi (Chibvumbulutso 6:16-17).**

VIII. CHIPULUMUTSO

A. SOTERIA ndi mau a chihelene otanthauza kumasulidwa, kutetedzera, ndi chipulumutso.

1. Kumasulidwa ku machimo, matenda, kugonjetsedwa ndi ku imfa.
2. Chipulumutso chimatenga lingaliro (ganizo) la kukhala wokonzedwa mwa thunthu.

B. Kulungamitsidwa.

1. Mau akuti "kulungamitsa" ndi chinthu choikika mwa lamulo pa nthawi yoikika chimene chitanthauza kudzikiritsa chilungamo, kudziyeretsa, kulengeza mau kapena kulandiridwa.
2. Nthawi kapena nyengo yakulandiridwa ndi kuima kwabwino pamaso pa Mulungu m'mene wina amalowamo mwa chikhulupiriro kupyolera kukhetsedwa kwa mwazi wa Yesu.
3. Mphatso yaulere ndipo siilandiridwa mwa malipiro (Aroma 5:1-2,15-16).
4. Ndi Mulungu amene amalungamitsa (Aroma 8:33).
5. Kusintha kwa malo - nthawi ina unali pansu pa chiwerudzo choopsa - unali wotsutsidwa.
6. Kufafanizika kwa machimo ndiponso kupatsidwa kwa chilungamo cha Yesu kwa ife (mulandu wosavuta wochotsera ndi kuonjedzera).
7. Mulungu amachita ndi kusamalira munthu wolungamitsidwa monga ngati sadachimweponso koma monga wochita bwino (Mwana Wolowelera).
8. Kulungamitsidwa (chilungamo) kumabweretsa madalitso.
 - a. Kumasulidwa ku imfa (Miyambo 10:2).
 - b. Moyo wochulukika (Miyambo 11:19,30;12:28).
 - c. Mtendere ndi chitsimikizo (Yesaya 32:17).

C. Kubadwanso

1. Mchitidwe wa Mulungu womwe umapereka moyo wa Khristu kwa wokhulupirira.
2. Kulongotsola kwa Chipangano Chatsopano kwa kubadwanso.
 - a. Kubadwa (Yohane 3:3-8)
 - b. Kutsukidwa (kuyeretsedwa) (Timoteo 3:5)
 - c. Chilengedwe (2 Akorinto 5:17; Aefeso 2:10).
3. Moyo wa uzimu umafika mwadzidzidzi, umaonekera mwa chinsinsi(modadwitsa), ndipo umakula pang'onopang'ono.
4. Mkhalidwe wake woposa - Palibe chipembedzo china chili chonse chimene chimalonjeza kusintha chikhalidwe cha uchimo ndikubweretsa mwaicho moyo wa Mulungu.
5. Kubadwanso chimene sichili:
 - a. Ubatizo wa m'madzi (Yohane 3:5) - Madzi ndi njira ya chifaniziro cha mau a Mulungu (Aefeso 5:25-26).
 - b. Kusintha - kubadwanso sintchito za munthu ndipo sizikhuzana ndi kupanga maganizo (Tito 3:5).
 - c. Chiwalo cha mpingo - nyama ngakhale itavekedwa ngati munthu komabe idzakhala nyama. Chikhalidwe choipa cha munthu sichingasinthike koma chiyenera kusiya choipa.
6. Kubadwanso kutanthauza:
 - a. M'chitidwe wa uzimu m'mene Mulungu amapereka moyo watsopano mu mzimu wa munthu (1 Petro 1:23).
 - b. Pamene tikhulupirira mwa Yesu, Mzimu wa Mulungu, umene unachoka chifukwa cha tchimo limene linabala imfa (Adamu ndi Hava) umabwerera chifukwa cha mphatso ya chilungamo.
 - c. Mtima (muuzimu) umadzalidwanso (Ezekieli 36:26).
7. Kutsendereza: popeza mwabadwanso mwatsopano zitanthauza kuti muli ndi moyo wa Mulungu mwa inu. Muli ndi chikhalidwe chake ndi mphamvu (mchitidwe) zake (Yohane 15:5; Agalatiya 2:20; Akolose 1:27). Mwayi wako woti uchite bwino kapena kuti kupambana kumaikidwa malire ndi kusakhulupirira.

D. Kutengera (kulandiridwa monga mwana mnyumba yomwe sunabadwiremo).

1. Njira yomwe Mulungu amapatsira umwana kwa iye amene sikunali koyonera mwa chikhalidwe cha umunthu (Aroma 8:15; Agalatiya 4:5).
2. Mulungu satengera okhulupirira monga ngati ana, koma obadwa m'banja la Mulungu ndi Mzimu Woyera kudzera mchikhulupiriro (bukhu lotanthauzira mau lonena poyera la W.E. Vine). Matanthauzo a ma baibulo a NKJ ndi NIV amatsokoneza pamene athanthauzira mau a chi helene monga "kutengera kwa tiana." Kunayenera lithanthauzidwe kuti "kutengera kwa ana okula msinkhu."
3. Kutengera kufaniziridwa kulowa mbanja monga mwana wokula msinkhu.

4. Pali kusiyana pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano.
 - a. Mchipangano Chakale, Aisraeli anali kuledwa ngati ana aang'ono chifukwa anali pansu pa utsogoleri wa olamulira ndi aphunzitsi apadera (chi lamulo) koma Mchipangano Chatsopano okhulupirira amaleredwa ngati ana akulu misinkhu.
 - b. Ubwino weniweni wa kutengera (kulowetsedwa mnyumba monga mwana) ndi woti Mzimu Woyera umakhala mwaiwo ndi kuwatsogolera.
5. Pali phindu ndi mwayi popanga ubale ndi Atate.
 - a. Chisamaliro cha Atate (Luka 12:4-7).
 - b. Chilango choopsa (kudzudzulidwa) (Ahebri 12:5-11).
 - c. Chithonhozo (2 Akorinto 1:3-4)
 - d. Cholowa (aroma 8:16-17).
6. Landirani madalitso pokhala mbanja la Mulungu.
 - a. Pogawana nao dzina la mbanja (Afilipi 2:9)
 - b. Pogawana nao chifaniziro cha mbanja (2 Akorinto 5:17)
 - c. Pogawana nao chikondi cha mbanja (1 Yohane 1:3, 3:14)
 - d. Pogawana nao zochita ndi ntchito za mbanjamo.
7. Madalitso a mtsogolo - thupi la ulemerero ndi loomboledwa (Aroma 8:23; Afilipi 3:20-21).

IX. KUYERETSEDWA (KUPATULIDWA)

A. Njira imene Mulungu amaitanira, kutsukira ndi kupatulira wokhulupirira kuchokera ku machimo chifukwa cha ntchito yake ndi ulemerero wake.

B. Matanthauzo awiri - kupatulidwa ku choipa kudzipereka kwa Mulungu (2 Akorinto 7:1)

C. Kutanthauza kwa mau akuti " kuyeretsa."

1. Kuchitenga chinthu kukhala choyera kapena kuchidzindikiritsa kukhala choyenera kuchilemekeza ndi kuchitamanda (Luka 11:2; 1 Petro 3:15).
2. Kudzipatula ku zinthu za mwano ndi kudzipereka kwa Mulungu - kupatulidwa (Mateyu 23:17).
3. Kudziyetsa kapena kudzitsuka ku zodetsa (Aefeso 5:26; 1 Atesalonika 5:23).

D. Kupatulidwa, choncho, kumakhala ndi izi:

1. Pamalo.
 - a. Kupatulidwa kwa wokhulupirira kwa Mulungu kumene kumachitika pa nthawi ya kutembenuka mtima (1 Akorinto 6:11; Ahebri 10:14; 1 Petro 1:2).
 - b. Khristu ndiye chiyeretso cha wokhulupirira (1 Akorinto 1:30).
2. Mwa chidziwitso (zokuchitikira).
 - a. Chiyeretso cha wokhulupirira ku zoipa zonse (2 Akorinto 7:1)
 - b. Wokhulupirira amakhala wogwirizana ndi chikhalidwe cha Khristu

(Aroma 8:29; 2 Akorinto 3:1)

- c. Kuvula moyo wakale ndi kuvala wa tsopano (Akolose 3:8-13).
 - 1) Kudzipereka wekha kwa thunthu kwa Mulungu monga mwa machitidwe akufuna kwako (Aroma 12:1).
 - 2) Kukonzanso maganizo anu ndi mau (Aroma 12:1-2, Aefeso 4:23).
 - 3) Kukhala pansu pa mpatso za mautumiki asanu operekedwa kukumangirira oyera mtima (Aefeso 4:11-12)
 - 4) Tsatirani mzimu wanu (Agalatiya 5:16)
 - 5) Kudalira Yesu kuti akuthandizeni (Machitidwe a Atumwi 26:18).
3. Kutsendera (kumangirira): Chiphunzitso cha kuyeretsedwa chimaphunzitsa kuti pamene mwakhala m'khristu munasiya kukhala munthu wamba. Mwapatulilidwa ku ntchito ya padera.

X. MPINGO

A. Mpingo ndi chiyani? Mau a chi helene a mpingo "eklesia" amatanthauza "msonkhano wa anthu oitanidwa."

1. Mau ogwiritsidwa ntchito pofotokoza thupi (gulu) la akhristu lokhala m'mudzi (mzinda) umodzi (Machitidwe a Atumwi 11:22; 13:1)
2. Agwiritsidwa ntchito kunena kagulu ka anthu opemphera malo amodzi (Aroma 16:5; 1 Akorinto 14:19, 35).
3. Agwiritsidwa ntchito pofotokoza mpingo wa padziko lonse lapansi womwe uli wokhala ndi okhulupirira onse (Aefeso 5:32).

B. Mau a chizungu "mpingo" amachokera ku liu la chihelene loti "kos" kutanthauza "Ake a Ambuye."

C. Tsono, mpingo, "ndi bungwe la anthu oitanidwa kuchokera mdziko lapansi, amene avomereza kukhulupirira mosavuta kwa Ambuye Yesu Khristu." (Pearlman, Kudzindikira chiphunzitso cha Baibulo, 1937.)

D. Mpingo ukufaniziridwa monga izi:

1. THUPI LA KHRISTU (1 Akorinto 12:12-27; Aefeso 4:4)
 - a. Chinthu choyenda, chinthu cha moyo, osakhala bungwe ayi).
 - b. Lopatsidwa mphamvu ndi moyo wa Khristu.
 - c. Liri ndi ziwalo zambiri ndipo chili chonse ndi ntchito yake.
2. KACHISI WA MULUNGU (Aefeso 2:20-22; 1 Petro 2:5-6).
 - a. Mulungu amakhala mu mpingo mwa Mzimu wake (1 Akorinto 3:16-17).
 - b. Akhristu, monga a nsembe (mkachisi wa Mulungu), ayenera kupereka nsembe za uzimu za mapemphero, matamando, ndi ntchito zabwino.
3. MKWATIBWI WA KHRISTU (2 Akorinto 11:2, Aefeso 5:25-27)
 - a. Yesu amakonda. amasamala ndi kuteteza mpingo mwa nsanje.

b. Mpingo umagonjera kwa Yesu monga mkazi achitira kwa mwamuna wake.

E. Ntchito ya mpingo ndi chiyani?

1. Kulalikirira uthenga wabwino wa Yesu kuti anthu apulumutsidwe (Machitidwe a Atumwi 28:19-20; 1 Timoteo 2:4)
2. Kupereka mapemphero ndi mayamiko kwa Mulungu (Akolose 1:12; 1 Atesalonika 5:16-18; 1 Petro 2:9)
3. Kuphunzitsa ophunzira a Yesu ndi kukulitsa ukulu msinkhu wa akhristu kudzera m'mau a Mulungu (2 Timoteyo 3:16; 1 Petro 2:2).
4. Kupereka chiyanjano ndi:
 - a. Utatu Woyera (Afilipo 2:1; 1 Yohane 1:3)
 - b. Wina ndi mnzake (Machitidwe a Atumwi 2:42; 1 Yohane 1:7).
5. Kutetedzera dziko ku chikhaliidwe choipa (Mateyu 5:13-16).
6. Kuchita (kuonetsera) mphamvu ndi ulamuliro pa ufumu wa mdima (Luka 10:18-20; Aefeso 1:15-23).

F. Zina mwa zabwino (phindu) zakukhala chiwalo champingo ndi chiyanjano cha akhristu:

1. Mgwirizano (Amosi 3:3)
2. Magwero a mphamvu (Luka 22:32).
3. Njira yakutonhozana (Aroma 1:12).
4. Ena angagawane nawe zothodwetsa zako (Agalatiya 6:2).
5. Kudyetsana (kugawana) zauzimu (Akolose 3:16).
6. Kuthandiza wokhulupirira kugonjetsa chinyengo cha tchimo (Ahebri 3:13).

XI. KODI YANKHO LANU LIKHALA LOTANI?

A. Musaleke kusonkhana kwanu pamodzi (Ahebri 10:24-25)

B. Chikondi cha pa abale chikhalebe (Ahebri 13:1).

C. Gwirizanani mu Mzimu pamodzi ndi okhulupirira anzanu ndi moyo umodzi kugwirira ntchito pamodzi pa chikhulupiriro cha uthenga wabwino (Afili 1:27).

PANGANO (MGWIRIZANO) LA MWAZI

I. PANGANO LA MWAZI NDI CHIYANI?

A. Ndi mgwirizano wokhala pakati pa anthu kapena mbali ziwiri wosungidwa (kusindikizidwa) ndi kukhetsa kwa mwazi.

1. Lapafupifupi, lokhalitsa, pangano lopatulika ndilo dziwika kwa munthu
2. Lopanga mgwirizano kapena umodzi wosasungunuka (wosatha).

B. Pangano lakalekale lodziwika kwa munthu.

1. Ophunzira ambiri amakhulupirira linayamba m'munda wa Edeni.
 - a. Mulungu anapha nyama kuti afunditse umaliseche wa Adamu ndi Hava (Genesis 3:21).
 - b. Mwazi wa nyama unabisa machimo awo (Ahebri 9:22).

C. M'Baibulo kukhetsa kwa mwazi kumasonyeza kupereka kwa moyo.

1. Sizisonyeza imfa (Lev. 17:10, 14).
2. Kupereka kwa moyo chifukwa cha wina ndi mchitidwe waukulu wa chikondi (Yohane 15:13).

D. Pangano lopanda malire.

1. Zinthu zonse zobwezera (zolipira), za mangawa, za chikhaliidwe ndi za umwini (katundu yemwe uli naye) zili mkati mwa pangano.
 - a. Mangawa okhala ndi wina amagawanidwa ndi wina.
 - b. Zolipira (chuma) zokhala ndi wina zimagawanidwa ndi wina.
2. Mapangano ambiri lero ali achikhaliidwe chokhazikika pamodzi (okhala ndi malire).
 - a. Mwachitsanzo, mgwirizano wopaka nyumba Pentu sungakhuzenso ntchito ya magetsi.
 - b. Pangano la mwazi, mulimonse, ndi losakhazikika pamodzi (lopanda malire) limakhuza mbali zonse za moyo.

E. Pangano losasweka.

1. Pangano lopatulika lokhala pakati pa anthu akalekale (a nthawi yoyamba) opanda chitukuko.
2. Pangano la mwazi ndilopezeka paliponse ndi lodziwika dziko lonse lapansi kwa anthu onse.
3. Kulikonse komwe likuchitidwa, chonena ndi choti silinaswekepo chiyambire.
 - a. Chilango chakuswa pangano la mwazi ndi imfa.
 - b. Aini mabanja (abale) adzatsaka munthu amene amaswa pangano la mwazi.

II. ZIFUKWA ZOLOWERA MU PANGANO LA MWAZI:

A. Chitetezo.

1. Munthu wopanda mphamvu kapena fuko (mtundu) la anthu limalowa pangano ndi

munthu kapena fuko lamphamvu pa chifukwa cha chitetezo.

- a. Kuputa m'modzi wa pangano kunali ngati kuputa onse awiri.
- b. Ena akanabwera ku tchinjirizo la iwo.

B. Muzolinga za ntchito

1. Anthu a ntchito amalowa pangano la mwazi ndipo palibe yemwe amatenga ubwino wa wina.
2. Mbala nthawi zina zimalowa pangano la mtundu uwu kutsimikizira tchinjirizo kuchokera kwa anzao omwe ndi mbalanso (zitsanzo zaposachedwa monga: anthu opalamula - mafia, magulu a anthu ena achifwamba).

C. Chifukwa cha chikondi.

1. Chikondi ndiye chifukwa chachikulu cholowera pangano.
2. Jonatani ndi David anacheka pangano chifukwa cha chikondi (1 Samueli 18:1,4).
3. Nthawi zina kucheka pakati pa anthu okwatirana, kusonyeza gori losasweka.

III. NJIRA ZOLOWERA MU PANGANO LA MWAZI:

A. Kucheka chikhatho (padzanja) chadzanja ndi kuligwedeza (kulikhutchumula).

1. Chiyambi cha kugwirana dzanja - kugwedeza dzanja.
2. Manja anali kuchekedwa ndipo abale anali kugwedezana manja, kutsakaniza mwazi (magazi).

B. Kucheka polumikizira dzanja ndi kutsakaniza magazi.

C. Kucheka polumikizira dzanja ndi kutsakaniza magazi mkapu ya vinyo.

1. Wina aliyense anamwa theka la vinyo/theka la magazi zosakaniza.
2. Zoletsedwa m'malembo (Levitiko 17:10).
3. Chokhulupiridwa kukhala chiyambi cha kudyana anthu okhaokha - ufiti.

D. Kuika magazi anyama kulowesa m'malo mwa magazi a munthu zinali kuchitidwa m'Chipangano Chakale.

Mulungu anavomera (kalandira) magazi anyama kuti abise machimo a munthu.

IV. ZOCHITIKA (MAKWERERO) POLOWA MU PANGANO LA MWAZI

A. Zinthu zisanu ndi zitatatu zozitsata moyenera.

1. Kusinthana kwa zovala. Mwa chitsanzo, Jonatani ndi David anasinthana zovala (1 Samueli 18:3-4).
2. Kusinthana kwa zida za nkondo.
 - a. Ichi chinasonyeza kuti mphamvu zonse ndi machiri a nkondo (nyonga) zinagawanidwa.
 - b. Tili ndi mphamvu za Mulungu ndi mchitidwe ulamuliro wake mbali yathu.
 - c. Zida zonse za Mulungu ndi zopezeka kwa ife.

- d. Pangano lathu ndi Mulungu limatipatsa ife mwai (ufulu) kuchitetezo chonse chimene ku mwamba kungathe kupereka.
3. Kusinthana kwa maina.
- Munthu aliyense amatenga mbali (gawo) la dzina la mnzake.
 - Anthu mupangano ali ndi ulamuliro wa thunthu kugwiritsa ntchito dzina la mnzawo wa pangano (monga: mbanja mkazi amatenga ndiponso ndi chololedwa kugwiritsa ntchito dzina la mwamuna wake.)
 - Dzina la Yesu ndilo dzina la pangano lathu.
4. Kukhetsa mwazi mwa kudula (kucheka).
- Liu la chi hebri logwiritsidwa ntchito m'Baibulo limatanthauza "kucheka mpaka mwazi utuluke."
 - Kukhetsa kwa mwazi kofunikira; ndi chisindikizo cha pangano.
 - Phulusa kapena kanthu kena zimapakidwa pochekedwapo kupanga chidzindikiro (chilema) choonekera. Chirema ichi chimabwera kukhala chidziwitso kapena chitsimikizo cha pangano.
 - Ichi chinaonetsa mbale wa pangano ndipo onse ankatha kuona.
 - Anthu ocheka (kudula) pangano amatchedwa mitu ya pangano. Mwina muli monse, pangano silinali la mitu yokha koma la onse a banjalo ndi mibadwo yonse.
5. Kugawanika kwa nyama.
- Nyama inali kudulidwa pawiri ngati mbali ya mwambo wa pangano.
 - Magawo awiriwa anali kuikidwa pansu ndipo anthuwo anali kuyenda pakati pa magawo awiriwo mu nambala (chiwerengero) ya zisanu ndi zitatu (8) (Genesis 15:9-19).
6. Kulankhulidwa kwa mdalitso ndi themberero.
- Wina aliyense anali kulankhula mdalitso ndi themberero kwa mnzake wogawana naye - wolowa naye pangano.
 - Mdalitso pa kumvera malamulo a pangano ndipo themberero pakusamvera.
 - Deotoronomo 28 ndiye mndandanda wofunikira wa mdalitso ndi themberero.
7. Kukhazikitsa chikumbutso
- Anthu a mgwirizano amamanga chikumbutso kapena kuchita kanthu kena kowakumbutsa iwo za pangano lawo.
 - Zitsanzo zogwiritsidwa ntchito monga mbiri:
 - Mwala waukulu (Genesis 31:44-45).
 - Mulu wa miyala (Genesi 31:46-51).
 - Mwala pomwe amgwirizano analembapo pangano.
 - Kusinthana kwa nkhoa kapena nyama zina (Genesis 21:28-30)

5) Kudzala (kuoka kubzala) mitengo ya nthawi zonse (yaitali) (Genesis 21:31-32).

c. Chimodzi mwazonsezi kapena mosakaniza zonse zinali kugwiritsidwa ntchito.

8. Kudya kwa chakudya cha pangano.

a. Mkate ndi vinyo ndiye chakudya cha mwambo mwapangano.

b. Mkate umaimira thupi; ndipo vinyo amaimira mwazi (magazi).

B. Sikofunikira kumaliza zinthu zisanu ndi zitatatu zonsezi; ziwiri kapena zoposera mwa zonsezi ndi zololedwa (zovomerezeka).

V. PANGANO LATHU LA MWAZI NDI MULUNGU.

A. Chifukwa chiyani kuli kofunikira kuti tikhale ndi pangano la mwazi ndi Mulungu?

1. Mulungu anampanga Adamu kukhala wolamulira wa dziko lapansili (Genesis 1:26,28).

2. Mulungu anampatsa munthu ufulu wa kusankha.

a. Adamu anasankha kusamvera Mulungu.

b. Anapereka ulamuliro wake kwa satana.

c. Mzimu wake unafa nthawi imeneyi; analekanitsidwa ndi Mulungu mu uzimu.

d. Nthawi yomweyo; themberero la umphawi, matenda (kudwala), ndi imfa zinagwa pa munthu.

B. Mulungu anafuna chiyanjano ndi munthu.

1. Iye anaika mu ntchito kakonzedwe lakubweza munthu kumuikanso mchiyanjano.

2. Mwa Abrahamu Mulungu anapeza munthu amene akanatha kumukhulupirira ndi kumumvera iye.

3. Mulungu sakadamuononga Adamu ndi kupanganso munthu wina kuchokera ku fumbi la nthaka.

a. Dziko lapansi ndi zonse zili momwemo zinakhala zake za satana.

b. Mulungu sakadatha kugwiritsa ntchito fumbi la pa nthaka - silinalinso lokhuzana (lake) ndi iye kapena Adamu.

4. Mulungu anayenera kubweretsa Adamu wachiwiri (Yesu Khristu) m'dziko lapansi. Munthu anayambitsa kugwa - Munthu anayenera kuombola umunthu. (Aroma 5:17,18).

C. Mulungu anapeza mwa Abramumu munthu amene iyeyo akanagwira naye ntchito.

1. Mulungu anayamba kuchita ndi Abramumu (Genesis 12:1-6).

2. Abramumu anali wa zaka makumi asanu ndi awiri kuza mphambu zisanu (75) pamene Mulungu anayamba kuonekera kwa iye.

3. Mulungu anamuza Abramumu kusiya nyumba, dziko ndi abale. Iye pambuyo pake anakhulupirira Mulungu ndipo anachoka.

4. Mulungu analonjeza zinthu zambiri kwa Abramumu. Abramumu anakhulupirira

Mulungu(Genesis 12:2-3).

D. Mulungu anapanga pangano lamwazi ndi Abramum kumarizitsa chomwe anachiyamba pa Genesis 12:.

1. Pangano lamwazi pakati pa Mulungu ndi Abramum (Genesis 15:1-17).
 - a. Mulungu anati adzakhala chikopa cha Abramum ndi mphoto yake yaikulu (ndime 1).
 - b. Abramum akufunsa Mulungu, "Mudzandipatsa ine chiyani? (ndime 2).
 - c. Mulungu akumuuza (ndime 5).
 - d. Abramum anakhulupirira, ndipo kunawerengedwa kwa iye ngati chilungamo (ndime 6).
 - e. Mulungu akunena chomwe Iye adzamuchitire Abramum (ndime 7-15).
2. Abramum anafunsa momwe iye akadadziwira kuti Mulungu akadatha kuchitadi ichi.
 - a. Mulungu anamuuza Abramum kuti "amtengere (Iye) ng'ombe yaing'ono"
 - 1) Uku ndikukambirana kwa pangano la mwazi.
 - 2) Pangano la mwazi linali lodziwika bwino kwa Abramum.
 - 3) Abramum anadziwa kuti Mulungu sanali kucheza.
 - 4) Abramum anayenera kutsimikiza kuti Mulungu adzasunga mau ake.
 - b. Abramum anatenga nyamazoz nazigawa pakati,
 - 1) Kuthamangitsa kwa mbalame kukuimirira satana kuba mau.
 - 2) Anali kudikira munthu wina wa mu pangano kuti ayende pakati pa mbali ziwiri za nyama zogawikazo pamodzi naye.
 - c. Abramum anagona tulo tatikulu (ndime 12). Ndipo Mulungu analankhula kwa Abramum ndi kumulola kuti aone chomwe chinali kuchitika.
 - d. Ng'anjo yofuka utsi ndi muuni woyaka moto zinadutsa pakati pa mabanthuwo (ndime 17).
 - 1) Ng'anjo yofuka ndiye Mulungu Atate (Ezekieli 19:18)
 - 2) Muuni woyaka moto ndiye Mulungu Mwana (Chibvumbulutso 21:23)
 - 3) Yesu anatenga malo a Abramum potsindikiza pangano.

E. Mulungu tsono anatha kukhala ndi ubale ndi munthu kudzera mu pangano la Abrahamu.

1. Pangano ili linali chinthu choyamba mu kutengera Adamu wachiwiri (Yesu) m'dziko lapansi.
2. Anthu okhala panso pa pangano ili anali ndi zokoma zambiri.
 - a. Ngati anakwaniritsa magawo awa, iwo analandira madalitso a umoyo (ukhondo), ulemerero ndi moyo wautali (Deutoronomo 28:1-4).
 - b. Kulandiridwa, mu zigawo, kusanadze kupachikidwa. Timalandira chifukwa

chakupachikidwa.

c. Anthu okhala pansu pa pangano la Abrahamu sangathe kubadwa mwatsopano kapena kuzazidwa ndi mzimu.

3. Anayang'ana kuloza ku mtanda, ndipo kwa iwo chinawerengedwa ngati chilungamo.

F. Kusintha kwa maina linali kwerero pakupanga pangano la mwazi.

1. YHWH ndilo dzina la Mulungu m'chi hebri. Chilembo chofunikira ndi "H."

a. Mulungu anaonjeza "H" kuchokera ku dzina lake kwa Abram, kupanga Abrahamu. Ichi chitanthauza "tate wa mtundu waukulu - unyinjira."

b. Anaonjeza "H" kupanga Sarai kukhala "Sara" (Genesis 17:15) Sara atanthauza "Mfumu kazi."

2. Mulungu anasinthanso dzina lake.

a. Atatha kupanga pangano ndi Abram anazitcha yekha "Mulungu wa Abrahamu."

b. Pambuyo pake anaonjezera "Isake ndi Yakobo" ku dzina lake (Eksodo 3:6).

G. Pangano la Mulungu ndi Abrahamu ndi pangano losatha.

1. Tili mbeu ya Abrahamu ndi olova nyumba (Agalatiya 3:13, 14,29).

2. Sitikanatha kukhala olova nyumba a chinthu china chimene sichingakhale (sichili moyo).

3. Pangano la Abrahamu lilipobe; silinachoke (silinafe).

4. Chilamulo cha Mose ndi nsembe zake za mwazi pamodzi ndi malamulo ake a mphamvu zinathedwa pa mtanda.

5. Sitilinso pa themberero la chilamulo.

6. Tili olova nyumba ku lonjezo chifukwa cha Yesu.

H. Chinthu china mu pangano la mwazi; kukhetsa kwa mwazi kumbali zonse ziwiri.

1. Mupangano la Abraham, mwazi wa munthu unakhetsedwa (Genesis 17:8,11,23) pamene Abrahamu anadulidwa.

2. Mu pangano lachiwiri ndi labwino koposa, mwazi wa Yesu unakhetsedwa. Yesu anatsanula magazi Ake pa mtanda.

3. Mdulidwe unamukumbutsa Abrahamu za pangano lake.

a. Pamene anali kuvala kusamba kapena anakhala ndi ubale ndi Sara (kugona pamodzi) anali kukumbutsidwa za pangano.

b. Mdulidwe unampatsa chidzindikiro Abrahamu ndi mbeu zake monga okhala ndi pangano pamodzi ndi Mulungu.

I. Pangano la mwazi linapangitsa Mulungu mwa lamulo kutha kutenga (kubweretsa) Adamu wachiwiri kudza naye m'dziko.

1. Anthu awiri amu pangano ali ndi zinthu zao, matalente (mphatso) pamodzi ndi zochitika zofanana.

2. Mbali iliyonse ingathe kufuna kanthu ka mbali ina ndi kuyembekezera kulandira.

3. Mulungu anafunsa nsembe ya Isake(Genesis 22:2).
 - a. Mulungu anadziwa Abrahamu akanatha kupereka zake zonse.
 - b. Mulungu anamuyesa Abrahamu ndipo sanampeza wosowa.
 - c. Mulungu anaona kufuna (kuvomerezeka) kwa Abrahamu pa kupereka zake zonse, ndipo anachirewenga icho ngati waperekadi Isake nsembe (Ahebri 11:17).
 - d. Mulungu anapereka kankhosa koperekera nsembe (Genesis 22:13).
4. Abrahamu anali wovomereza kupereka mwana wake m'modzi yekha nsembe. Chomwechonso Mulungu monga mnzake wa mgwirizano mu pangano sakadachitira mwina. Mulungu anatuma Yesu kudzafa pamtanda chifukwa mnzake wa mgwirizano mu pangano, Abrahamu, anali wovomereza (kufuna) kupereka mwana wake.

VI. BAIBULO LIRI NDI ZIPANGANO ZIWIRI KAPENA KUTI MAPANGANO AWIRI: PANGANO LAKALE NDI LATSOPANO.

A. Pangano lakale linali pakati pa Mulungu ndi Abrahamu.

B. Chilamulo chinaonjewedwa mu nthawi ya Mose.

1. Chilamulo chikupezeka mbukhu la Eksodo ndipo ndi mndandanda wa zochita ndi zosachita.
2. Bukhu la Levitiko - mndandanda wa nsembe ndi miyambo pamene chilamulo chinatswedwa.
 - a. Potsatira nsembe ndi miyambo izi, tchimo limabisidwa.
 - b. Nsembe za mwazi zinali kungobisa chabe tchimo, koma sizinachotse tchimo.
 - c. Mwazi wokha wa Yesu ungate kuchotsa tchimo.

C. Pansi pa chilamulo, mwazi wa atonde ang'ombe ndi mbuzi unabisa machimo kwa kanthawi.

1. Nthawi iliyonse yomwe anthu anachimwa, ankayenera kupanga nsembe yolondola kuti abise tchimolo.
2. Nsembe kapena zopereka za mitundu isanu pansu pa lamulo (Levitiko 1-7).
 - a. Nsembe yopsereza, nsembe ya chakudya, nsembe ya mtendere, nsembe ya uchimo ndi nsembe yopalamula.
 - b. Izi zinafunikira kubwereza nthawi ndi nthawi tchimo likachitika.

D. Chilamulo, muyeso wosakhalitsa (Agalatiya 3:19).

E. Mulungu anakonzeratu zomutumiza Yesu kuyambira pachiyambi cha dziko.

1. Khristu anali mwana wa nkhosa wopanda banga kapena chirema, wophedwa lisanakhazikitsidwe dziko (1 Petro 1:19-21).
2. Mulungu anadziwa kuti munthu adzaperewera nagwa koma anakonzeratu njira yachipulumutso.
3. Chilamulo ndi miyambo ndi nsembe zinapatsidwa kumusonyeza munthu kuti adzakhala woperewera kawirikawiri.

- a. Anamuonetsera munthu kuti anafunikira (anali kusowa) chisomo cha Mulungu.
- b. Anamuonetsera kuti sakanatha kuchita zofuna za Mulungu ndi mphamvu za iye yekha.
- c. Anamusonyeza (kumulozera) munthu ku mtanda ndi kufunikira kwake kofuna mpulumutsi.
- d. Palibe munthu akadakwaniritsa zonse za chilamulo.

VII. CHOSOWA CHA MUNTHU POFUNA MPULUMUTSI

A. Yesu anatchulidwa (anasankhiridwatu) pachiyambi kudzafa dziko lisanakhazikitsidwe (1 Petro 1:19-21).

B. Mulungu anatuma Yesu mu nthawi yake kudzafa pa mtanda (Agalatiya 4:4)

C. Munthu anachimwa, munthu anayenera kufa kuti ayanjanitse mtundu wa anthu.

1. Simunthu wina aliyense kuti akanatha kutero.
2. Momboli anafunika kukhala munthu wina amene alibe chikhalidwe cha uchimo.
3. Yesu yekha, munthu woyera ndi Mulungu Woyera akanatha kutero.
 - a. Ngati mwazi wa munthu wamba unali wokwanira, Abrahamu akadapereka Isake nsembe.
 - b. Mwazi wa Isake sunali wokwanira.
4. Mwazi unayenera kukhetsedwa, koma mwazi wake umene unalibe tchimo.
5. Mwazi wa munthu umaperekedwa ndi mbeu ya mwamuna.
 - a. Mwazi wa Yesu unaperekedwa ndi Mulungu.
 - b. Mwazi wa Yesu unali wopanda chilengedwe cha uchimo, imeneyi ndiyo nsembe yolandirika.

VIII. TILI NDI PANGANO LOPAMBANA (LABWINO LOPOSA) CHIFUKWA CHA YESU.

A. Pangano lopambana lokhala ndi malonjezano opambana (Ahebri 8:6).

1. Pangano lakale silinali la mgwiro (Ahebri 8:7).
2. Silikanatha kumuyanjanitsa munthu kwathunthu kwa Mulungu.
3. Chilamulo chinali muyeso wosakhalitsa posonyeza tchimo la munthu ndi
4. kuperewera kwake pofuna kukwaniritsa zofuna za Mulungu (Agalatiya 3:24-25).

B. Yesu anadza kudzakwaniritsa chilamulo (Mateyu 5:17,18)

1. Yesu anakwaniritsa chilamulo ndipo chinathedwa.
 - a. Chilamulo chinaonjezedwa kufikira mbeu inabwera (Agalatiya 3:19).
 - b. Yesu, yemwe ndi mbeu, anabwera ndipo anagonjetsa lamulo.
2. Atangokhetsa mwazi wake Yesu, nsembe ya nyama inali yosafunikiranso.
3. Chifukwa chiyandinso tiyesera kubisa chomwe chinachotsedwa kale?

C. Pangano la Abrahamu lidakali la mphamvube.

1. Pangano lomwe Mulungu anapanga ndi Abrahamu ndi losatha.

2. Pangano silingamalizidwe (kuchotsedwa) mpaka litakwaniritsidwa.
3. Akolose 2:14
 - a. Yesu anachotsa, cholembedwacho mzoikikazo chotsutsana ndi ife.
 - b. Pangano la Abrahamu silinali lotsutsana; chilamulo chinali chotsutsana.
 - c. Anatenga chilamulo kuchichotsa mu njira ndi kukachipachika ku mtanda.
 - d. Tili omasulidwa ku themberero la chilamulo.

D. Pangano la Abrahamu lidzakwaniritsidwa (kutsirizidwa) pakudza kwake kwachiwiri.

1. Pamene Yesu adzabwera, dziko lonse lolonjezedwa kwa Abrahamu pa Genesis 15; lidzabwedzeretsedwa.
2. Ichi chidzakwaniritsa malonjezano onse apangano.
3. Pangano lizathedwa (lidzachotsedwa) pamenepo.
4. Tidzapita mu zaka zana (1000) zolamulira Yesu Khristu.
5. Pangano la Abrahamu lidzachotsedwa m'malo mwache chifukwa silidzakhalanso lofunikira.

IX. PANGANO LATSOPANO NDI PANGANONSO LA MWAZI

A. Pangano lakale losindikizidwa ndi mwazi wa munthu, Abrahamu (pa mdulidwe).

B. Pangano latsopano losindikizidwa ndi mwazi wa Mulungu Yesu (pa mtanda).

C. Kukhetsa kwa mwazi kofunikira nthawi zonse pa mbali ya pangano la mwazi.

1. Pangano latsopano ndilopambana chifukwa linasindikizidwa ndi mwazi wa Mulungu.
2. Mwazi wa Yesu unali wokwanira kulipira ngongole ya tchimo ya mtundu wa anthu.

D. Njira zisanu ndi zitatu zothekera (zochitika) mupangano la mwazi: Yesu anakwaniritsa zonsezi.

1. Yesu anasinthanitsa zovala ndi tchimo (Yesaya 64:6, Aroma 3:23).
 - a. Yesu anatenga zovala zathu zodetsedwa za chisalungamo ndikutipatsa ife zake zoyera za chilungamo (2 Akorinto 5:21).
 - b. Zovala zathu zodetsedwa, zodetsedwa ndi tchimo tsopano zayera ndikutsukika.
2. Timalandira zida za Mulungu (Aefeso 6:13-17).
 - a. Tili ndi zida za Mulungu ngati china mwa zabwino zathu za pangano.
 - b. Tiyenera tivale koma ndi zathu zoti tigwiritse ntchito.
3. Yesu anakhetsa mwazi wake kulemba pangano (kutsimikizira).
 - a. Kukhetsa kwa mwazi nthawi zonse kofunikira pa pangano la mwazi.
 - b. Chinsalu cha mkachisi chinang'ambika pamene Yesu anafa, kusonyeza kuti panalibenso kusiyana pakati pa Mulungu ndi munthu (Mateyu 27:51)
 - c. Mwazi wa Yesu unagulanso ubale wathu ndi Mulungu.
 - d. Themberero pa munthu linachotsedwa kwa muyaya.

- e. Yesu anali mwana wa nkhusa wotsiriza wa paska kuti aphedwe (1 Akorinto 5:7)
4. Mdalitso ndi themberero.
 - a. Yesu anapangidwa kukhala themberero chifukwa cha ife kuti mdalitso ubwere pa ife (Agalatiya 3:13).
 - b. Yesu anamva ululu wa matenda onse, zowawa ndi zopweteka za dziko ili lapansi ndipo sitifunikanso ife kutero (Yesaya 53).
 - c. Anasiyanitsidwa ndi Mulungu kuti tikhale ndi ubale ndi lye.
 - d. Anapita ku gehena kuti ife tithe kupita kumwamba.
 5. Kusinthana kwa maina.
 - a. Mupangano la mwazi, anthu amgwirizano ali ndi mphamvu kugwiritsa ntchito maina a anza mu mgwirizano.
 - b. Dzina la Yesu ndilo dzina lapangano lathu.
 - c. Tili ndi mphamvu kugwiritsa ntchito dzina la Yesu ndikukandira zosowa pamodzi ndi zokhumba zathu.
 6. Kukhazikitsa chikumbutso.
 - a. Yesu anapereka chiyanjano, (mgonero wotsiriza), ngati chikumbutso kwa lye.
 - b. Nthawi iliyonse pamene tidya mgonero, tikumbukira imfa yake ndi kuuka kwake (1 Akorinto 11:25-26).
 7. Kugawa pakati kwa nyama.
 - a. Ndi ndime (gawo) yokhayo yomwe sinakwaniritsidwe ndi Yesu.
 - b. Mwazi wake unali wokwanira. Mwazi wa nyama sunali wofunika (wosoweka).
 8. Chakudya cha pangano.
 - a. Mgonero wotsiriza kapena chiyanjano ndiye pangano la chakudya.
 - b. Lokhala ndi mkate ndi vinyo (pangano la zakudya za mwambo)
 - c. Tanthauzo lofunikira pa chimene Yesu anachita.
 - d. M'miyambo yakale ya chiyuda mipukutu (maphukusi) itatu yathumba la chikopa lodzadzidwa ndi mikate linali pa gome la mgonero.
 - 1) Yesu anatenga mkate mthumba lapakati (monga unali mwambo) ndi ku nyema.
 - 2) Ayuda anaganiza kuti mkate unaimirira Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Sanadziwe kuti nchifukwa chiyani "Isake anali m'modzi wonyemedwa.
 - 3) Mkate unasonyeza Atate, MWana ndi Mzimu Woyera.
 - 4) Yesu ananyema mkate wapakati, mwa njira iyi, kuonetsera (kusonyezera) thupi lonyemedwa la mwana.
 - e. Miyambo yakalenso ya Chiyuda inali ndi zikho zinayi pa gome la mgonero; zitanu zozaza ndipo chimodzi chopanda kanthu, chomwe chimaikidwa mozondotsa.

- 1) Zikho zodzadzazo kusonyezera Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Chikho chopanda kanthu chinali cha Mesiya.
 - 2) Yesu anatenga chikho cha Mesiya, nachidzadza, namwa mwa icho (Marko 14:36).
 - 3) Pa mchitidwe uwo anali kunena kuti "Ine ndine Mesiya."
 - 4) Thanthauzo ili linali lodziwika kwa ophunzira Ake.
9. Ndime (gawo kapena kuti kwerero) ina mupangano la mwazi inali kupaka phulusa pochekedwa, kupanga chirema (chipsera).
- a. Mdulidwe unawadzindikiritsa a Yuda ngati anthu a pangano.
 - b. Lero, chidzindikiro chathu cha pangano ndi Mzimu Woyera (1 Akorinto 1:22; Aefeso 1:13,4:30).

E. Tili ndi pangano ndi Mulungu, lotsindikizidwa (lolembedwa) ndi mwazi wa Yesu.

1. Pamene Yesu anafuula, "kwathu" mau amene lye anawagwiritsa ntchito ndi "tettelesti." Uku kunali kufuula kwa mtsogoleri wa nkhondo wa chiroma akuyang'anira nkhondo ali paphiri. Pamene anali kuona kuti mbali yake ili kupambana kwambiri, anali kufuula motere kudziwitsa gulu lake kuti nkhondo yagonjetsedwa motheratu.
2. Asilikali ambiri ankhondo achi roma anali pafupi ndi mtanda. Msilikali m'modzi amene anamva kufuula uku anati, "zoonadi uyu anali mwana wa Mulungu." Sanathe kumvetsa chifukwa chomwe munthu amene anali nkufa pa mtanda akanathera kufuula kwa chigonjetso kwa mtsogoleri wa chiroma. Pa ichi iye anati; "Zoonadi uyu anali mwana wa Mulungu." (Mateyu 27:54).
3. Yesu anapambana (anagonjetsa) nkhondo.
 - a. Chomwe chinatsala ndi kungokatha masiku atatu (usiku ndi usana) muhade.
 - b. Iye anadziwa kuti anapambana.
 - c. Iye anafuula chigonjetso chifukwa anatsiriza mwa kupambana (mwachigonjetso) ntchito yake yomwe anapatsidwa kuti aichite.
 - d. Yesu anampindula munthu ndi kumubwezera kwa Mulungu.

CHIKHALIDWE CHA MULUNGU

I. MAGWERO A VUMBULUTSO

A. "Kodi ukhoza kupeza Mulungu mwa kufunafuna" (Yobu 11:7)?

B. Mulungu waziulula bwanji yekha?

1. **Kuziulula kwa wamba** - muzolengedwa ndi mu mbiri (Masalimo 19:1-6; Aroma 1:18-20)
2. **Kuziulula kwapadera** - kuzera mwa Yesu ndi Bukhu Lopatulika (Luka 24:27, 44-45; Yohane 1:18, 5:39, 14:9).

II. ZOCHITIKA ZA MULUNGU (ZOSAKHALA ZA UMUNTHU)

A. WODZIWA ZONSE: Zochitika za Mulungu mu mphamvu yomwe imamupangitsa kudziwa zonse za tsopano, zakale ndi za mtsogolo.

1. Mulungu amadzidziwa yekha ndi zinthu zina zonse kuyambira ku nthawi zosayamba, kaya ndi zoonza kapena zosaziwika ngati zingatheke.
2. Iwo mwa okha (Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera) ali ndi chidziwitso cha wina ndi mnzake. (Mateyu 11:27; 1 Akorinto 2:11).
3. Mulungu akudziwa zinthu zomwe zili ndi moyo, kuphatikizirapo zolengedwa (Masalimo 147:4), anthu ndi ntchito zao (Masalimo 33:13-15), maganizo a anthu ndi mitima yao (Masalimo 139:1-4) a anthu mavuto ndi zofuna zao (Eksodo 3:7; Mateyu 6:8).
4. Mulungu akudziwa zinthu zonse zimene zili zotheka (1 Samueli 23:11; Mateyu 11:28).
5. Mulungu amadziwa tsogolo. Zochitika mtsogolo sizichitika chifukwa zikudziwika, koma zikuoneka/kudziwika chifukwa zichitika.
6. Mulungu amadziwiratu; Amaona zinthu kamodzi umo m'mene ziliri, chimodzichimodzi pachokhapachokha, osati modukiza ayi.

B. WOPEZEKA PENA PALIPONSE: Zochitika za Mulungu zomwe mu mphamvu zake amadzadza dziko lonse pena paliponse.

1. Mulungu yense, osati mbali ya iye, amapezeka pa malo ena ali onse.
2. Simulungu m'modzi yemwe amaphunzitsa kuti china chilichonse ndi mbali ya Mulungu (mwachitsanzo, mpando kapena pensulo)koma kuti Mulungu ali pa maloponse ndi mosiyana ndi zolengedwa zake.
3. Ngakhale Mulungu amapezeka penapaliponse, pali kusiyana pakapezekedwe kake.
4. Chiphunzitso chimenechi ndi cholimbikitsa komanso chochititsa mantha, kwa wokhulupirira, Mulungu yemwe apezeka penapaliponse ndi kuthandiza wopezeka nthawi zonse (Deutoronomo 4:7; Masalimo 46:1; Mateyu 28:20). Kwa wochimwa, kaya achita bwanji kuyetsetsa, sangathawe Mulungu (Masalimo 139:7-12).

C. WAMPHAMVU ZONSE: Chikhalidwe ichi chimafotooza mphamvu ya Mulungu yochita china chili chonse chomwe afuna.

1. Chifuniro cha Mulungu chili ndi malire chifukwa cha chilengedwe chake. Sangachite

china chili chonse chomwe chili chosiyana ndi chilengedwe chake changwirow.

- a. Mulungu sanganame (Tito 1:2)
 - b. Mulungu sangaziononge yekha (2 Timoteo 2:13).
 - c. Mulungu sangakondere ndi tchimo.
 - d. Mulungu sangachite cholakwa.
 - e. Mulungu sangachite chomwe chili chosakondweretsa (chopusa) kapena chosemphana ndi lye, monga kupanga chinthu cha makona anayi kuti chikhale chozungulira, kupanga zinthu ziwiri kuphatikiza ziwiri zipherezera zisanu ndi chimodzi, kapena kuchita chinthu choyipa.
2. Mulungu saongoleredwa ndi mphamvu zake: umoyo wa mphamvu zonse siulirira kuonetsa mphamvu. Ali ndi mphamvu kuposa mphamvu zake, kapena akanaleka kukhala waufulu. Akhoza kuchita zomwe afuna (aganiza) koma alibe maganizo kuti achite chili chonse.
 3. Wamphamvu zonse kuphatikizirapo mphamvu za malire ochita yekha. Mulungu amazipatsa yekha malire kufikira pamalo omwe amapereka ufulu ku zolengedwa chotsatha. Nchifukwa chake tchimo padziko mwa mphamvu zake ndiponso nchifukwa chake sapulumutsa aliyense monkakamiza.
 4. Mulungu ali ndi mphamvu zonse zotha kukhazikitsa zomwe wina aliyense alibe.
 - a. Mphamvu zenizeni: Mulungu akagwira ntchito moonekera, monga zochitika mwa milakuli (zodabwitsa) ndi mchilengedwe mwa chili chonse mwa "zinthu zosaonedwa."
 - b. Mphamvu zapadera: Pamene Mulungu amachita ntchito yake kuzera ku ntchito ina, monga timachitira kubzala ndi kukolola.
 5. Maumboni a m'Bukhu Lopatulika ndi maumboni ena:
 - a. "Kodi chilipo chinthu chomlaka Yehova?" (Genesis 18:14)
 - b. "Ndidziwa kuti mukhoza kuchita zonse ndi kuti palibe choletsa cholingirira chanu chili chonse." (Yobu 42:2).
 - c. "Chiri chonse chimkonda Yehova achichita, kumwamba ndi pa dziko lapansi, m'nyanja ndi mozama monse." (Masalimo 135:6).
 - d. "Iye achita mwa chifuniro chache m'khamu la kumwamba ndipo palibe woletsa dzanja lake, kapena wakunena naye, Muchitanji? (Danieli 4:35).
 6. Chiyambi cha kutonthozedwa kwambiri ndi chiyembekezo kwa wokhulupirira. Kwa wochimwa Mulungu sakulekeza kuwachenjeza ndi chiyambi cha mantha (1 Petro 4:17; Chimbvumbulutso 6:15-16).
 7. Ngakhale mizimu yoipa imaopa (Yakobo 2:19). Tsiku lina ngakhale amphamvu ndi akulukulu adzafuna ofuna kubisala kwa lye (Chimbvumbulutso 6:15); bondo liri lonse lizagwadira dzina la Yesu (Afilipi 2:10).

D. KUSASITHIKA: Chikhalidwe cha Mulungu mwa mphamvu chomwe chima mpanga kukhala wosasinthika ndi wosasinthidwa.

1. "Ine Yehova, sindisinthu..." (Malaki 3:6)
(Onaninso Masalimo 33:11 ndi Yakobo 1:17).
2. Kusinthika kwa munthu kungathe kukhala kwabwino kapena koipa, koma Mulungu sangasinthe kuti akhale wabwino kapena woipa chifukwa iye ndiwabwino (wangwiro).
3. Nanga ndime monga Genesis 6:6, Eksodo 32:14 ndi Yona 3:10 zomwe zinena kuti Mulungu "analapa" kapena anasintha maganizo ake?
 - a. Mulungu sasintha poyerekeza ndi khalidwe lake (Masalimo 102:26, 27) kapena ntchito (cholinga) yake (Masalimo 33:11).
 - b. Kutu akhale wokhulupirika ku khalidwe ndi ntchito (zolinga) zake zomwe sizingasinthe, Mulungu amasintha m'machitidwe ake ndi anthu pakusinthu zochitika mu kasinthisintha (monga mwachitsanzo Nineve).
 - c. "Yesu Khristu ali yemweyo dzulo ndi lero ndi ku nthawi zonse." (Ahebri 13:8).

III. ZOCHITIKA ZA MULUNGU (ZA UMUNTHU)

A. CHIYERO: Maganizo a Mulungu a kumwamba (chikhalidwe cha Mulungu chomwe mu mphamvu zake amafuna ndi kukhazikitsa zolengedwa zake.

1. Kutionetsa kusiyana pakati pa Mulungu ndi zolengedwa zake.
2. Khalidwe lake lamuyaya lopanda cholakwa (chomdetsa). Iye ndi wosiyana ndi zinthu zina zonse ndi tchimo. Mwa chitsanzo, kukhala wamoyo wabwino (wathanzi) kumapitirira wopanda kudwala. Chimodzimodzi, woyera kusiyana ndi kusapezeka kwa tchimo. Ndi chikhalidwe changwiro ndi maganizo ovomerezeka abwino. (Levitiko 11:44; 1 Petro 1:15).
3. Mulungu anati, "Usayandikire kuno; vula nsapato zaku kumapazi ako, pakuti pamalo pamene upondapo iwe, mpopatulika." (Eksodo 3:5).
4. Chifukwa cha chiyero chake Mulungu sangakhale ndi mgwirizano ndi tchimo.
5. Kuyankha kwake kwa munthu kuvumbulutso la chiyero cha Mulungu, ndikudziona monga wosayenera pamodzi ndi chikumbu mtima chodetsedwa (Yesaya 6:5)
6. Chiyero ndi chikhalidwe chimene Mulungu anafuna kudziwika nacho mChipangano Chakale.
 - a. Liu likugwiritsidwa ntchito kopitirira 830 mchipangano chakale.
 - b. Chiyero chiri kusimikizidwa m'malo a m'kachisi kapena chihema posiyanita malo oyerera ndi oyeretseta.
 - c. Chiyero chili kufotokozedwa m'malamulo a misonkhano: zopereka, unsembe, maphwando komanso malamulo okhuzana ndi zodetsedwa (Levitiko 1-5, 23)
 - d. Chiyero chivumbulutsidwa mu lamulo la umunthu lomwe limalankhula kudzera mwa Yesu "woyera ndi wolungamayo" ku chikumbu mtima cha anthu. (Machitidwe a Atumwi 3:14)
7. Chiyero cha Mulungu chitiphunzitsa:
 - a. Pali kulekana pakati (pompho) pa Mulungu ndi wochimwa (Yesaya 59:1,2).

- b. Munthu mwa iye yekha sangathe kupeza mwai wosakhala ndi tchimo womwe ndi wofunika pofikira Mulungu.
- c. Pali chosoweka cha chiombolo chimene chikasoweka chiweruzo chimene chiririkudza palibe kuthawa.
- d. Munthu ayenera kubwera kwa Mulungu molemekeza ndi mwa mantha "Pakuti Mulungu wathu ndiye moto wonyeketsa" (Ahebri 12:28-29)

8. Chomwe chiyero chake chimafuna chikondi chake chinapereka (Aroma 5:6-10).

B. UBWINO: Iye ali mu njira ina iri yonse imene Iye ali monga m'mene anayenera kukhalira - Iye ndi okwanira mu chili chonse chimene chipereka tanthauzo loti Mulungu.

1. Chifukwa choti Mulungu ndi wabwino, amachita zinthu zake mochuluka ndi machikondi ndi zolengedwa zake (Masalimo 145:9,15,16).
2. Chifukwa choti Mulungu ndi wabwino amakonda mosayang'anira zimene munthu ali.
 - a. Mulungu ndi chikondi (1 Yohane 4:8).
 - b. Chikondi ndi chomwe chifuna ubwino wa chinthu chokonedwacho.
 - c. Mulungu amakonda kuposa umunthu wa aliyense (1 Yohane 4:8-10).
 - d. Machitidwe a chikondi (1 Akorinto 13:4-8).
 - e. Chiyambi cha chilimbikitso (chilimbikitso) wokhulupirira.
 - 1) Adzachita ntchito zake kwa ubwino wa okhulupirira (Aroma 8:28- 39)
 - 2) "Iye ndi Atate amene amadziwa chimene ana ake akusowa (Mateyu 6:8).
 - 3) Amapereka zinthu zabwino kwa ana ake (Aroma 8:32; Yqkobo 1:17).
3. Chifukwa choti Mulungu ndiwabwino Iye ndiwachifundonso.
 - a. Chifundo ndi ubwino wa Mulungu womwe umaonetsedwa kukhuza omwe ali m'mavuto ndi mokhumudwa.
 - b. Mulungu ndi odzadza ndi chifundo (Aefeso 2:4), wodzala ndi chisoni ndi chifundo (Yakobo 5:11), ndipo ali ndi chifundo chodzadza (1 Petro 1:3).
 - c. Chifundo chimayendetsa Yesu.
 - 1) Mzimu woipa waku Gadara (Luka 8: 26-39)
 - 2) Machiritso a munthu wa khate (Marko 1:40,41).
 - 3) Chifukwa Mulungu ndi wabwino ndi wokoma mtima.
 - a) Chisomo ndi ubwino wa Mulungu womwe umaonetsedwa kwa anthu omwe sayenera kulandira.
 - b) Chisomo cha Mulungu chimapulumsa munthu wochimwa ngakhale ali wolakwa.
 - c) Chisomo ndi mayambiriro a madalitso auzimu omwe amaikidwa kwa anthu ochimwa (Aefeso 2:8-9).
 - d) Yesu anapereka chitsanzo cha chisomo pamene ankanena za mkazi

yemwe anagwidwa akuchita chigololo (Yohane 8:1-11).

4. Chifukwa choti Mulungu ndiwabwino amaleza mtima nthawi zambiri.
 - a. "Koma inu, Ambuye, ndinu Mulungu wasoni ndi chisomo, wosapsa mtima msanga ndi wochulukira chifundo ndi choonadi." (Masalimo 86:15).
 - b. Mulungu amapirira ndi anthu ochimwa ngakhale nthawi zambiri akhala osamvera.
 - c. Kupirira kwa nthawi yaitali kwa Mulungu kumakhala koti kuthandize anthu kuti alape ndipo kusatanthauziridwa ngati kulekelera kwa Mulungu (2 Petro 3:3-9).

C. CHILUNGAMO NDI CHIWERUZO

1. Chilungamo ndi chiweruzo ndi maziko a mpando wake (Masalimo 89:14; 97:2)
2. "Kodi sadzachita zoyenera woweruza wa dziko lonse lapansi? (Genesis 18:25)
3. Zanedwa kuti "boma lamakhalidwe abwino linakhazikitsidwa pa dziko lino ndi Mulungu pokhuzana ndi malamulo a chilungamo ndi mavomerezo abwino.
 - a. Malamulo a Mulungu amachitidwa kuzera mukulandira mphoto ndi zilango.
 - b. Mphoto ya chiweruzo - kugawa kwa mphoto (2 Mbiri 6:15; Masalimo 58:11)
 - c. Chilango cha chiweruzo - kupereka kwa chilango (Genesis 2:17; Eksodo 34:7)
4. Mulungu sangapange lamulo ndi kupanganso (kukhazikitsa) chilango, ndiyeno nkusatsatira ngati lamulolo sili mveredwa.
5. Chiweruzo (chilungamo) chimaitanitsa chilango pa wochimwa, komanso chimalandira imfa yoopsa ya wina, monga zalambedwera mu Yesaya 53:6 ndi Aroma 5:8.)
6. Chilungamo ndi chiweruzo cha Mulungu zavumbulutsidwa mu:
 - a. Chilango chake pa ochimwa (Chibvumbulutso 16:5-9)
 - b. Powateteza anthu ake kwa anthu ochita zoipa (Masalimo 129:1-5).
 - c. Kukhulukira okhulupirira zochimwa zao (1 Yohane 1:9).
 - d. Kusiya malonjezo kwa ana ake (Ahebri 10:25)
 - e. Kubwezera mphoto okhulupirika (Ahebri 6:10).
7. Mchitidwe wa chilango.
 - a. Chisamaliro cha chiweruzo.
 - b. Kusungidwa kwa anthu ndi dziko.
8. Chilungamo ndi chiweruzo cha Mulungu zimalimbitsa wokhulupirira chifukwa iye amadziwa kuti Mulungu amaweruzo mwa chilungamo ndipo chifukwa cha chimenechi, amakhala ndi chitsimikizo kuti zinthu zachilungamo zomwe wachita sizingapite zopanda kuonedwa (Miyambo 19:17).

IV. TANTHAUZO LAKE LAMULUNGU

"Mulungu ndi mzimu, wopanda malire, wamuyaya, wosasintha mu chikhalidwe, mu mnzeru, mu mphoto, mu chiyero, chiweruzo ndi choonadi." (Westminster

catechism).

V. CHIKHALIDWE CHA MULUNGU CHIVUMBULUTSIDWA KUPYOLERA M'MAINA AKE.

A. Kupambana kwake kwa dzina la munthu m'Bukhu Lopatulika.

1. Kudziwa dzina la munthu ndiko kudziwa chikhalidwe chake.
2. Chikhalidwe chake cha munthu chinali nthawi zonse kulumikizidwa mu dzina lake. Kusintha kwa dzina lake kunali kusinthika kwa chikhalidwe chake, ntchito yake kapenanso udindo wake (chitsanzo Simoni linasinthidwa ndi kukhala Petro mu Mateyu 16:17-18).
3. Pamene wina apereka dzina kwa munthu, iye amakhazikitsa ubale wa ulamuliro kapenanso chuma (chitsanzo Adamu popereka maina kwa nyama).
4. Munthu angathe kupereka dzina lake ku zinthu zimene iye wazigonjetsa kapena kuti zimene ziri zake monga mzinda kapena dziko (2 Samueli 12:28; Masalmo 49:11).
5. Dzina ndi munthu sizingathe kkulekanitsidwa chifukwa ali amodzi.
6. Chifukwa chachimenechi, kudziwa dzina la Mulungu ndiko kudziwa chikhalidwe cha Mulungu ndi kulandira mphamvu, ulamuliro, kulimba mtima kwake komanso kuzipereka kwa Mulungu mwini.
7. Dzina ndi ulamuliro: Dzina la Yesu ndiwo ulamuliro wake woperekedwa kwa munthu kotero kuti athe kuchita zozizwa, kulalikira ndi kupemphera kwa Atate (Marko 16:17; Machitidwe a Atumwi 4:7). Yesu anatipatsa mphamvu yovomerezidwa ndi lamulo kuti tikachite m'malo mwake.

B. Maina a Mulungu ndi zida za mavumbulutso a malamulo ake, chikhalidwe chake, pamodzi ndi ntchito zake.

1. **El japena Elohim** - kumasulira kuti "Mulungu" ndi "m'modzi woyenera kulambiridwa"
 - a. Matanthauzo ena ndi awa:
 - 1) Kukhala wa mphamvu.
 - 2) Kukhala ndi malo akulu owalamulira
 - 3) Kukhala nazo, mphamvu yomangirira.
 - b. Kugwiritsa ntchito paliponse pamene mphamvu yakulenga ndi mphamvu zonse pamene zifotokozedwa ndi kuchitika.
 - c. Kuchulukitsidwa kwa dzina la Mulungu kutsonyeza utatu wa Mulungu.
 - d. Zifotokoza Mulungu monga mphamvu yolamulira imene iima pambuyo ndi kusintha chilengedwe.
 - e. El Shaddai, "Mulungu wa mphamvu zonse", - kuonetsera ukulu ndi kukhazikika ; pothawira podalirika; mzati wosasinthika.
2. **Jehovah (Yahweh)** - kumasulira "Yehova".
 - a. Dzina la Mulungu la mapangano.
 - b. Limabwera kuchokera ku mau ochitika akuti, "kukhala" (Eksodo 3:13-14).
 - c. Kufotokozerakuti Mulungu ndi wa muyaya amene anali, ali ndi amene

adzakhale.

- d. Dzina ili linali ndi ulemu waukulu koposa kotero kuti Alembi anali kuopa kulitchula dzinali.

3. **Jehovah-Rohi-** "Yehova ndiye mbusa wanga.

- a. Yehova ali kuonetsedwa mchipangano chakale monga m'busa (Masalimo 23:1, 80:1).
- b. Chipangano chatsopano: Yesu mbusa Wabwino, amene anapereka moyo wake chifukwa cha nkhosa (Yohane 10:11).
- c. Pasoweka mbusa wathupi.
 - 1) Nkhosa sizingathe kuzisamalira zokha.
 - 2) Sizidziwa komwe ziri - zimatha kusochera mosavuta.
 - 3) Pamakhala zoopsa pa nkhosa kuzera ku nyama zolutsa za kuthengo komanso mbala.
 - 4) Izi zilinsu chimodzi modzi kwa anthu. Iwo atha kusocherera kuzoopsa nthawi ndi nthawi.
- d. Ubale (chiyanjano) wapakati pa mbusa ndi nkhosa zake.
 - 1) Kudziwana kwenikweni pakati pa mbusa ndi nkhosa.
 - a) Amadziitana nkhosa zake ndi dzina (Yohane 10:3) Yesu amaitana inu ndi dzina lanu.
 - b) Nkhosa zake zimadziwa liu lake (Yohane 10:4)
 - c) Iye amaonetsetsa ngati imodzi yasowapo (Mateyu 18:12-13).
 - d) Palibe mbusa wina aliyense padziko lino lapansi amene anatha kudziwa bwino nkhosa zake kuposa Yesu (Yohane 10:14).
 - 2) Iye amatsogolera nkhosa zake (Masalimo 23:3; Yohane 10:4)
 - a) Sizidziwa njira, ndipo njirayo ndi yaying'ono ndi yoopsa.
 - b) Iye amadzitsogolera kotero kuti sidziyenda machisawawa koma kuti ziri ndi komwe zikupita.
 - 3) amazibwezera m'malo nkhosa zomwe zinasochera.
 - a) Nkhosa yomwe yasochera imakhala yothedwa nzeru ndi yosadziwa choyenera kuchita.
 - b) Mbusa ayenera kuifuna ndikuibweza nkhosa yosochera ku khola lake.
 - c) Izi zomwe zimachitika ndi mbusa wathu Yesu (Masalimo 23; Yesaya 53:6).
 - 4) Popeza kuti Atate ali ndi ana ambiri sizitanthauza kuti ana ang'ono ang'ono samawasamalira ayi.
 - 5) Mbusa wabwino samafuna choipa chifikire pa nkhosa zake zing'ono zing'ono ayi (Mateyo 18:12-14).
- e. Mbusa wosamalira nkhosa mwapadera mu nthawi yake yakusowa (Yesaya 43:2)

- 1) Kwoloka misinje ndi yaing'ono yomwe komanso moto.
 - 2) Kusamalira nkhosa zodwala ndi zopweteka.
 - a) Mankhwala odziwika omwe anali kuwagwiritsa ntchito ndi mafuta azitona.
 - b) "Mwadzodza mutu wanga mafuta (Masalmo 23;5). Pamene tiri kudwala kapena tavulazidwa, Ambuye amatidzodza ife mafuta ake a mzimu ndi kutichiritsa. Msamariya wa chifundo (Luka 10:30-37) ndi kuchiritsa odwala (Yakobo 5:14) ndizo zitsanzo ziwiri za mchipangano chatsopano.
 - f. Zikhalidwe zake za mbusa; Amakhala maso nthawi zonse, kulimba mtima kopanda chikondi.
4. **Jehovah-Rapha**- "Yehova wa kuchiritsa iwe" (Eksodo 15:22-26; Masalimo 107:20)
- a. Palibe munthu amene ali ndi umamuliro wosintha maina achiombolo a Mulungu iwo sananene kuti Mulungu sachiritsa lero.
 - b. Machiritso ndicho chifuniro chake cha Mulungu kwa onse.
 - 1) Zakhala zakulankhulidwa kunena kuti chikhulupiriro chimayambika pamene chifuniro cha Mulungu chadziwika.
 - 2) Ndicho chifuniro chake cha Mulungu (mwachitsanzo, kuchiritsidwa kwa wa khate mu bukhu la Marko 1:40,41)
 - 3) Machiritso ndi lonjezo la pangano pamodzi ndi phindu lake (Deotoronomo 7:15; Masalimo 103:1-5).
 - 4) Chifuniro changwiro cha Mulungu chovumbulutsidwa mu utumuiki wa Yesu.
 - a) Mateyu 4:24; 9:35;10:1;12:15; 14:14; 34-36; Marko 1:40-41; Luka 6:17-19; Machitidwe a Atumwi 10:38).
 - b) Yesu sanabwezepo wodwala ndi m'modzi yemwe kapena kuuza kuti "sindingachite."
 - 5) "Wokonedwa, ndi pemphera kuti pa zonse ulemere, nukhale bwino, monga mzimu wako ulemera" (3 Yohane 2).
 - c. Machiritso mu chiombolo (imfa ya pa mtanda).
 - 1) Soteria, mau a chihelene omasulira "chipulumutso" amanthauza, chiombolo, machiritso, chitetezo, ukhondo ndi umoyo wabwino.
 - 2) Sozo, mau a chihelene omasulira "kupulumutsidwa kupulumutsidwa" ndi "kuchiritsidwa" amanthauza kupulumuka ndi kupangidwa kukhala a moyo (Machitidwe a Atumwi 14:9; Aroma 10:9).
 - 3) Kuombedwa kuthemberero la chilamulo (Deotoronomo 28:15-62; Agalatiya 3:13).
 - 4) Ndi mikwingwirima yache ife tapulumutsidwa (Yesaya 53:4; Mateyu 8:17; 1 Petro 2:24).
 - 5) Njoka ya mkuwa (Nume 21:9)
 - a) Chiphunzitso cholakwika cha munga m'thupi la Paulo ndi cholepheretsa

ku machiritso (2 Akorinto 12:7-10).

(1) "Munga m'thupi" ndi mau okuluwika.

(2) Sanayambepo agwiritsidwa ntchito m'Bukhu Lopatulika ponena za matenda (Nemeri 33:55; Yoswa 23:13).

(3) Mau a chihelene "anglos" agwiritsidwa ntchito m'Bukhu Lopatulika malo okwana 188, m'malo onsewa amafotokoza za munthu osati zao chinthu ayi.

(4) Paulo akuulula za munga m'thupi; kuti anali wamithenga wa satana.

VI. MAINA ASANU NDI AWIRI (7) A MULUNGU OFOTOKOZA ZA CHIOMBOLO

Maina amenewa amavumbulutsa madalitso amene aperekedwa kudzera mu chiombolo (imfa ya pa mtanda).

A. Jehovah-Yehova wopezekeratu (Ezekieli 48:35).

B. Jehovah-Shalom - Yehova ndiye mtendere (Oweruza 6:24).

C. Jehovah-Rohi - Yehova ndi mbusa wanga (Masalimo 23:1).

D. Jehovah-Jireh - Yehova aona kapena kuti akwaniritsa (Genesis 22:14).

E. Jehovah-Niss - Yehova chitetezo kapena kuti chigonjetso changa (Eksodo 17:8-15).

F. Jehovah-Tsidkenu - Yehova chilungamo chathu (Yeremiya 23:6)

G. Jehovah-Raph- Yehova wa kuchiritsa ine (Eksodo 15:26)

VII. MAINA ENA

A. El-Elyon-Mulungu wa m'mwamba mwamba (Genesis 14:18-20).

B. El-Olam-Mulungu wosatha (Genesis 21:33).

C. Abba-Atate kapena kuti Abambo (Aroma 8:15).

UDINDO (KAPITAWO) WA CHIKHRISTU

I. KUONA KOYENERA (Kumvetsetsa)

A. Mulungu ndiye mwini wake wa dziko lonse lapansi pamodzi ndi zonse zimene ziri m'dziko (Masalimo 24:1)

B. Ndife adindo amene akhulupiridwa ndi udindo wosamalira ndi kuyang'anira zinthu zomwe mwini wake ndi Mulungu.

C. Yesu ananena zambiri za Udindo:-

1. Fanizo la matalente (Mateyu 25:14-30).

a. Mulungu amapereka mphatso zosiyanasiyana ndi maudindo ake.

b. Mulungu amayembekezera kuti inu mugwiritse ntchito zomwe muli nazo pamodzi ndi zomwe mungathe kuchita kufikira pa mapeto pake mosasiya kanthu.

c. Udindo wabwino umalandira mphoto pamodzi ndi udindo wake waukulu, koma Mulungu adzachotsa kwa mdindo wosakhulupirika zomwe ali nazo.

d. Gwiritsani ntchito ntchito muli nazo kapena zitayeni.

2. Mdindo Wabwino ndi mdindo Woipa (Luka 12:35-40)

a. Mdindo sali mfulu kuchita zofuna zake, iye adzadziwerengera zochita zake.

b. Nthawi ndi yochepa; Ambuye angathe kubwera nthawi ina ili yonse.

3. Mdindo (Kapitawo) wonyenga (Luka 16:1-15)

a. Tiyenera kukhala wokhoza ndi wodzipereka pakufunitsitsa zinthu za Mulungu monga momwe amachitira munthu wochimwa pofunitsitsa ndi kulondetsa pa zinthu za dziko.

b. Gwiritsani ntchito chuma kapena kuti katundu amene muli nawo pobweretsa anthu kumwamba (:9).

c. Iye amene akhala wokhulupirika mu zinthu zazing'ono, adzakhulupiridwa mu zinthu zambiri (zochitika).

d. Munthu sungathe kukhala kapolo wa ambuye awiri (kutumikira ambuye awiri).

II. MULUNGU AMAFUNITSITSA KULEMELETSA ATUMIKI AKE - Deutoronomo 28

A. Maumboni a m'Chipangano Chakale

1. Abrahamu (Genesis 13:2, 24:35)

2. Isake ndi Yakobo (Genesis 26:12, 30:43)

3. Solomoni (1 Mafumu 3:13)

4. Yobu (Yobu 42:12)

B. Maumboni a m'Chipangano Chatsopano

1. (Marko 10:29; Luka 6:38; Afilipi 4:19; 3 Yohane 2)

2. (Paulo sanasilire golide kapena siliva wa wina aliyense chifukwa chakuti iye anadzipangira chuma chambiri chomwe anachipereka kudzera mu ntchito yake yopanga zihema (Machitidwe a Atumwi 20:32-35; Afilipi 4:18:19).

3. Yesu
 - a. Iye anali ndi msungi chuma
 - b. Iye anatha kusamalira gulu lake lopindula miyoyo ya anthu khumi ndi awiri (12)
 - c. Iye anali kuvala mkanjo wopanda msoko komanso chovala cha mtengo wake wapatali.

III. ZOOPSA ZOGWIRIZANA NDI ULEMERERO

- A. Chikhumbo chofuna chuma pa zifukwa za chuma zimatsogolera ku zoipa za mtundu uli wonse (1 Timoteo 6:9-10).
- B. Ngozi yokundika (Mlaliki 5:13; Luka 12:15-21; Yakobo 5:1-3).
- C. Kulinga kufunikira kwako kolinga ndi akatundu amene uli nawo ndiko kugwiritsa ntchito muyeso wolakwika ku moyo (Yobu 36:19; Miyambo 11:4;13:7; 1 Timoteo 6:17).
- D. Ulemerero ungatsogolere kukudzikuzza ndiponso kuiwala Ambuye - Chimaliziro chake ndi chionongeko (Deutoronomo 8:11-19)
- E. Mnyamata mwini chuma yemwe anakonda chuma chake koposa Mulungu - Ndalama zake zinali kumulamulira m'malo moti iye azizilamulira ndalamazo (Marko 10:17-27).
- F. Vuto siliri ndi ndalama koma chikhalidwe chathu pa ndalamazo. Chidziwitso choonetsa kuti uli pambali yabwino kapena yoipa pokhuzana ndi ndalama ndi pamene iwe uli "wokonzeka kugawira ena chumacho kapena ndiwe wovomereza kugawa" (1 Timoteo 6:6-19).
- G. Pomangilira: Ulemerero m'moyo mwa wina aliyense amene mtima wake suli pa chiyanjano ndi Mulungu ndi ngozi (choopsa) yaikulu.
- H. Malangizo ogonjetsera mavuto (ngozi) a ulemerero.
 1. Funani zakumwamba osati zapansi pano (Akolose 3:1,2).
 2. Musafune kukhala a chuma koma kuti mukhale mdalitso. Lolani kupereka chikhale cholinga chanu pofuna ulemerero.
 3. Monga adindo sititenga zinthu zimene watipatsa Mulungu kukhala ngati zathu zathu. Khalani ngalande yodzeramo madalitso, osati nkhokwe ayi.

IV. MAFUNGULO (Makiyi) OLOWERA MU ULEMERERO WA M'BUKHU LOPATULIKA (Baibulo)

- A. Chachikhumi - Limodzi la magawo Khumi pa zomwe wapindula ziyenera kuperekedwa pothandizira ntchito ya mpingo (Malaki 3:10).
 1. Lamulo: "Limodzi mwa magawo khumi la zonse m'dziko, la mbewu zake za dziko, la zipatso za mtengo, ndilo la Yehova; likhale lopatulikira Yehova (Levitiko 27:30).
 2. Zinachitika lamulo lisanadze:-
 - a. Abrahamu anapereka limodzi la magawo khumi la zonse anali nazo kwa Melikizedeki (Genesis 14:18-24).
 - b. Yakobo analonjeza kupereka limodzi la magawo khumi la zonse anali nazo (Genesis 28:10-22).

3. Cholinga cha gawo limodzi mwa magawo khumi:-
 - a. Zitiphunzitsa kumuika Mulungu m'malo oyamba m'miyoyo yathu (Deutoronomo 14:22).
 - b. Zimatithandiza kukhala afulu osalamuliridwa ndi zinthu ndiponso zimatithandiza kusakhala akapolo a chuma (ndalama).
 - c. Zimathandiza utumiki ndi zonse zochitika mu mpingo (Numeri 18:21).
 - d. Zimapereka mbewu zimene Mulungu amazichulukitsa pokumana (kukwaniritsa) zosowa zathu (Luka 6:38; 2 Akorinto 9:10).
 - e. Zimatikuza ife monga adindo ndikutiphunzitsa kukhala okhulupirika posamalira katundu wake wa Mulungu.
4. Chachikhumi ndi Chipangano Chatsopano.
 - a. Chifukwa chiyani sitikumva zambiri za chachikhumi mu Chipangano Chatsopano? Chiphunzitsochi chinali cholandiridwa ndi onse ndipo panalibe kusamvetsetsana pakati pawo.
 - b. Yesu anaphunzitsa kuti chachikhumi chisaiwalike (chisakanidwe)(Mateyu 23:23).
 - c. Yesu, monga wa nsembe mwa maitanidwe a Melikizidweki, amalandira limodzi la magawo khumi ngakhale zikuoneka ngati timapereka kwa anthu (Ahebri 7:8).
5. Chachikhumi ndi Zopereka.
 - a. Zopereka ndi mphatso zomwe timapereka poyimirira zopitirira pa limodzi la magawo khumi la zonse zimene tapindula.
 - b. Kuchuluka kwa zopereka zathu kudzakopedwa ndi zomwe tapindula, chikondi chathu, chikhulupiriro chathu pamodzi ndi kutsogolera kwa Mzimu wa Mulungu.
 - c. Lamulo lakupereka ndi kulandira (2 Akorinto 9:6).
 - d. Zopindula zathu zonse ndi zake za Mulungu. Iye akutitsogolera pa chomwe tingachite ndi limodzi la magawo khumi. Bweretsani ku nyumba yosungira. Kenaka akutipatsa ufulu wogwiritsa ntchito asanu ndi anayi magawo khumi a zopindula zathu (zomwe watipatsa) pofuna kukwaniritsa zosowa zathu komanso kuti tithe kuthandiza kupititsa patsogolo Uthenga kupyolera mu zopereka zathu.
 - e. Madalitso ndi matemberero mogwirizana ndi limodzi la magawo khumi (chachikhumi).

B. Kuzipereka kopanda malire ku Ufumu wa Mulungu.

1. Zinthu zonse zimene tizisowa (zovala, chakudya, zakumwa ndi zina zotero) zalonjezedwa kwa mwana wa Mulungu (Mateyu 6:24- 34).
 - a. Pali zoyenera kuchitika pofuna kuti lonjezo ili likwaniritsidwe.
 - 1) Yambani mwathanga mwafuna Ufumu wa Mulungu. Pangani Ufumu wa Mulungu ndi kukondweretsa Mulungu kukhala chinthu choyambirira m'moyo wanu (Mateyu 6:33).
 - 2) Khulupirira Mulungu ndipo usadere nkhwana; khala ndi chikhulupiriro (:31)

- b. Atichenjeza pa zakudera nkhwawa pa zinthu za moyo uno.
 - 1) Umaonetsa kuti sukukhulupirira Mulungu.
 - 2) Zinthu zimene timazifuna zitha kukhala fano.
 - 3) Kupembedza mafano kapena kuti kusilira kumafikira kwa osauka ngakhalenso olemera.
2. 2 MAFUMU 4. Chitsanzo cha zochita za Mulungu pamene tamuyika Iye pa malo oyamba ndi kumukhulupirira Iye (mafuta a mkazi wamasiye ndi mwana wa mwamuna wa mkazi wa ku Sunemu).
- a. Mkazi wamasiye anaonetsa chikhulupiriro chake pakumvera Mawu a Ambuye.
 - b. Taonani: Pamene Iye anali kubweretsabe zotengera zake, mafuta anali kubwerabe.

Timaletsa madalitso athu pamene tisiya kubweretsa zotengera zathu zopanda kanthu (kuyembekezera zodadwitsa).
3. Abrahamu anapindula ulemmerero wa uzimu ndi wathupi womwe. Chinsinsi chake chinali chiyani?
- a. Iye anafunafuna Ufumu wa Mulungu poyambirira, osati zinthu za dziko ayi.
 - 1) Iye anasiya zofewa (zokoma) za pamudzi wake ku Harani namvera Mulungu (Genesis 12:1).
 - 2) Ngati maso ake akanakhala pa zinthu za moyo uno, Iye sakanachoka kwao chifukwa mzinda wawo unali pakati pake pa zamalonda pamene akanatha kulemera kwambiri.
 - 3) Iye anali kufunafuna Ufumu wa Mulungu, Mzinda wosamangidwa ndi manja (Ahebri 11:8-10).
 - b. Abrahamu anali kuyenda mwa chikhulupiriro, osati mwa zoonekazo; Iye anakhala mogwirizana ndi Mawu a Mulungu.
 - 1) Pamene Mulungu anamuuza kupita ku dziko lomwe sanalidziwe, Iye anamvera.
 - 2) Pamene anauzidwa kupereka Isake nsembe, Iye anamvera.
 - c. Abrahamu anadzichotsa yekha ku moyo wa makangano nayenda mu mtendere ndi abale ake. (Genesis 13:8-12).
 - d. Abrahamu anali wopanda umbombo koma wopatsa (Genesis 13:9).
 - e. Abrahamu anali munthu wa choonadi ndi wangwiro (Genesis 14:13-24)
 - 1) Iye anakana kutenga njira ya chifupi (chidule) pofuna kulemera mwa msanga mu njira zomwe sizikanalemekeza Mulungu.
 - 2) Iye anazemba yeso, lokhala pa chiyanjano ndi dziko ndi kukhala bwenzi m'machitidwe a dziko pofuna kuzipindulira yekha.
 - f. Abrahamu anakumbukira lamulo la ulemmerero ndipo anapereka limodzi la magawo khumi la zonse anali nazo (Genesis 14:20).

g. Abrahamu anapereka zonse kwa Mulungu, ngakhale Isake mwana wake wokondedwa (Genesis 22).

V. MALAMULO OCHITIKA AKUPEREKA NDI KULANDIRA

A. Gwiritsani ntchito chikhulupiriro chanu pamene mukupereka.

1. Mbewu ya chikhulupiriro
2. Vomereza kuti Mulungu wakudalitsa ndipo ali kukudalitsa.
3. Khala ndi chikhalidwe chokhulupirira m'maganizo ako ndi chikhalidwe cha ngwiro poganizira Mulungu.

B. Lemba zonse zimene ukhulupirira Mulungu kuti akuchitira (Habakuku 2:2).

1. Zomwe walembazo zipangitsa chikhulupiriro chako kukhala maso ndi kuona Mulungu akugwira ntchito yokwaniritsa chosowa.
2. Mtambo wa chikaiko udzakuphimba iwe ngati uli ndi zosowa zomwe sizinafotokozedwa bwino m'maganizo ako.

C. Pempherera zinthu zonse ndipo uyenera kuzidziwa pachokha pachokha.

1. Pemphera pa chosowa chako chenicheni (Luka 11:5-8).
2. Kumbukira chomwe wapemphacho.
3. Mapemphero a zinthu zosadziwika, ndi zopanda maina ndi ovuta kuyankhidwa.

D. Khala m'chifuniro cha Mulungu (Aefeso 5:17).

1. Mulungu amafuna kudzipereka kwako kokonzekera kuchita chili chonse lye asanakuvumbulutsire zimene akufuna kuti iwe uchite. Chifukwa cha chimenechi dzipereke wekha kukuchita chifuniro chake cha Mulungu pa mtengo wina uli wonse - chidze-chidze.
2. Tsimikiza kuti uli kumvera Mawu.

E. Panga ndondomeko zazikulu mosamalitsa zomwe zingafune kuti Mulungu aloweleremo.

1. Ngati zomwe ukupangazo ziri zoti zingathe kuchitika popanda thandizo lake la Mulungu, ndiye kuti ndi zazing'ono kwambiri.
2. Musaziikire malire chifukwa cha zomwe muli nazo, ndipo musayese kulingalira za umo m'mene Mulungu angachitire.

F. Chitani kolingana ndi chikonzekero chanu. - Yambani kuchitapo kanthu ndipo kumbukirani kuti chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.

G. Perekani kwa iwo amene akutumikirani (kukuphunzitsani) (Agalatiya 6:6; 1 Akorinto 9:7-14).

H. Khalani ndi moyo lero ngati kapena Ambuye abwera lero lomwe (Aefeso 5:16).

I. Konzekerani kupereka tsiku loperekalo lisanafike (1 Akorinto 16:1.2)

J. Ikani (perekani) mwa anthu chifukwa chinthu chomwe chimakhudza Yesu poyambirira mu mtima mwake ndi anthu.

K. Funsani Mzimu Woyera akutsogolerani mukupereka kwanu.

L. Onetsetsani (tsimikizani) kuti ku mpingo kapena mtumiki amene mukumuthandiza

ndi chuma chanu ali kulalikira Mawu oona a Mulungu, akugwiritsa ntchito ndalamazo moyenerera monga kuti adzadzaiwerengera mlandu, ndipo kuti iyeyo ali kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu.

M. Pereka mokondwera (2 Akorinto 9:6-7)

N. Pereka ndi mtima wonse (2 Akorinto 9:7)

O. Pereka ku ulemerero wa Mulungu (2 Akorinto 9:12-13)

P. Maphunziro ochokera m'Mawu a Mulungu (Luka 10:30-37).

CHIPHUNZITSO CHA ZIWANDA

Kuona za kuphunzira chiyambi ndi kagwiridwe ka ntchito ka Satana ndi mizimu ya ziwanda

"Siikudza mbala koma kuti ikabe ndi kupha ndi kuononga." (Yohane 10:10)

- I. **SATANA ANALI KUMWAMBA MONGA LUSIFALA (Ezekieli 28:1-19).**
 - A. Anatusidwa kunja (Chibvumbulutso 12:9)
 - B. Anjelo ochepa anatuluka naye (Chibvumbulutso 12:4)
 - C. Amalamulira pa zochitika za dziko ngati mulungu wa dziko (2 Akorinto 4:4)
 - D. Ali ndi ulamuliro wa uzimu ndi ufumu (Aefeso 6:12)
- II. **SATANA NDI ZIWANDA ZAKE AKUGWIRABE NTCHITO MPAKA LERO**
 - A. Akupitapita naononga (1 Petro 5:8)
 - B. Ali otanganidwa kunena za abale (Chibvumbulutso 12:10)
 - C. Sangathe kuzichulukitsa pogwiritsa ntchito mphamvu za umunthu.
 - D. Sangathe kuwerenga maganizo.
- III. **YESU ANAGONJETSA SATANA (Akolose 2:15)**
 - A. Yesu anatipatsa ife ulamuliro pa satana pamodzi ndi mizimu yake yoipa (Mateyu 28:18-20; Marko 16:15-20; Luka 10:19)
 - B. Tiyenera kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera kuti tithe kupambana ziwanda zoipa.
 - C. Musakhale osazindikira njira zake, kuti angakhale ndi mwayi wokugwirani (2 Akorinto 2:11)
- IV. **NJIRA ZISANU NDI ZIWIRI (7) ZOMWE SATANA AMAZIGWIRITSA NTCHITO POLIMBANA NAFE**
 1. **KUONA NGATI SUNACHITE BWINO** - kubwerera m'mbuyo;
 2. **KUZINYOSES**A - zosaneneka; osazionetsa; kukhala chete; kumyata; samanena zokhuzana ndi mavuto.
 3. **KULEPHERA KUPANGA CHISANKHO CHOMUTHANDIZA** - kuzichepetsa mozinyozesa; kubisa zochitika mthupi lako ndi zomwe umva
 4. **KUSOWA MTENDERE/KUTAYA MTIMA** - kukhala wa nkhwawa; kusweka mtima, kusokonezeka; kukwiya; kusowa mtendere; kusowa chisangalalo; kuzipha; kusaona tsogolo; kusowa mphamvu; kusowa machawe.
 5. **KUPHINJIKA/KUSENDEREZEKA** - kukusanjikiza chinthu chimene sichili cha msinkhu wako, kudwala; nthenda; chisoni; mantha.
 6. **KUTEMBENUZA KWA ZINTHU** -kulephera komvetsa zinthu; kuopa zinthu zosaoneka; chonama chimakhala choona; choona chimakhala chabodza; sangathe kuganiza za china chili chonse. Amafuna chithandizo chochokera kwa ena kuti akhale waufulu.
 7. **KULAMULIRIDWA MWA NKHANZA**(njira yosiliza) - mdierekezi amamulamulira kotheratu; amamva mau, misala kapena kuzungulira bongo; maso ali ndi kuyang'ana kwa ziwanda; chithandizo cha ena akunja chingawatuluse m'mavuto.

V. MAINA A SATANA

- A. **Abaddon (Apollyon)** - "Ndipo linali nayo Mfumu yakutilamulira, m'ngelo wa kupompho dzina lake m'chihelene ndilo Apoliyoni. (Chibvumbulutso 9:11).
- B. **Woneneza wa abale** - " Pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku." (Chibvumbulutso 12:10) Onaninso Yobu 1 ndi 2
- C. **Mdani** - :Khalani odzisungira, dikirani, mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufuna wina kuti amuononge." (1 Petro 5:8)
- D. **M'ngelo wa kuwala** - "Ndipo kulibe kudadwa pakuti satana yemwe adzionetsa ngati m'ngelo wa kuunika." (2 Akorinto 11:14).
- E. **Keubi wadzodzedwa** - "Unali kerubi wodzodzedwa wakuphimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu, anayendayenda pakati pa miyala yamoto." (Ezekieli 28:14)
- F. **Beelzebule** - "Koma Afarisi pakumva, anati, uyu samaturutsa ziwanda koma ndi mphamvu yake ya Beelzebule, mkulu wa ziwanda." (Mateyu 10:25,21:24)
- G. **Beliyani** - "Ndipo Khristu avomerezana bwanji ndi Beliyani? Kapena wokhulupirira ali nalo gawo lanji pamodzi ndi wosakhulupirira?" (2 Akorinto 6:15)
- H. **Wosokoneza maganizo** - "Koma ndiopa, kuti monga njoka inanyenga Heva ndi kuchenjera kwake, maganizo anu angaipidwe kusiyana nako kuona mtima ndi kuyera mtima ziri kwa Khristu." (2 Akorinto 11:3)
- I. **Mdierekezi (wonyenga)** - "Ndipo chinaponyedwa pansu chinjoka chachikulu, njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi ndi satana, wonyenga pa dziko lonse; chinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi." (Chibvumbulutso 12:9)
- J. **Njoka** - "Ndipo chinaoneka chizindikiro china m'mwamba, taonani, chinjoka chofiira, chachikulu, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri (7), ndi nyanga khumi ndi pamutu pake nduwira zachifumu zisanu ndi ziwiri." (Chibvumbulutso 12:3) onaninso (Chibvumbulutso 20:2-7)
- K. **Mdani** - "Ndipo mdani amene anamfesa uwu, ndiye mdierekezi ndi kututa ndicho chimariziro cha nthawi ya pansu pano ndi otutawo ndiwo angelo." (Mateyu 13:39)
- L. **Mulungu wa dziko lino** - "Mwa amene Mulungu wa nthawi yino ya pansu pano unachititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti chiwalitsiro cha Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Khristu, amene ali chithunzithunzi cha Mulungu chisawawalire." (2 Alorinto 4:4)
- M. **Mfumu** - "Ndipo linali nayo Mfumu yakutilamulira, mngelo wa phompho." (Chibvumbulutso 9:11 onaninso Aefeso 6:12).
- N. **Wonama** - "Inu muli ochokera kwa atate anu mdierekezi, ndipo zolakalaka zake atate wanu mufuna kuchita. Iyeyu anali wambanda kuyambira pachiyambi, ndipo sanaima m'choonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wake, pakuti ali wa bodza, ndi atate wake wabodza." (Yohane 8:44)
- O. **Lusifala** - "Wagwadi kuchokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kucha! wagwetsedwa pansu, iwe wolefula amitundu!" (Yesaya 14:12)
- P. **Wokupha** - "Iyeyu anali wambandadi kuyambira pachiyambi, ndipo sanaima m'choonadi pakuti mwa iye mulibe choonadi." (Yohane 8:44)
- Q. **Wosausa** - "Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdodza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu, amene anapitapita nachita zabwino, nachiritsa onse osautsidwa ndi

mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye." (Machitidwe a Atumwi 10:38)

- R. Mkulu wa mu mlengalenga** -"Mfumu ya mphamvu za mu mlengalenga." (Aefeso 2:2)
- S. Mkulu wa mu mdima** -"Kulimbana ndi olamulira a mdima pa dziko lino." (Aefeso 6:12)
- T. Mkulu wa dziko lino** - "Tsopano pali kuweruza kwa dziko ili lapansi, mkulu wa dziko ili lapansi adzatayidwa kunja tsopano." (Yohane 12:31) onaninso Yohane 16:11.
- U. Mkango wobuma** -"Khalani odzisungira, dikirani, mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire." (1 Petro 5:8)
- V. Satana** - "Ndipo panali tsiku lakuti ana a Mulungu anadza kudzionetsa kwa Yehova, nadzanso satana pakati pao." (Yobu 1:6) onaninso Chibvumbulutso 12:9
- W. Njoka** - "Koma ndiopa, kuti pena, monga njoka inanyenga Hava ndi kuchenjerera kwache."(2 Akorinto 11:3)
- X. Woyesa** - "Ndipo woyesayo anafika ..." (Mateyu 4:3)
- Y. Mbala** -"Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha ndi kuononga. Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo ndi kukhala nao wochuruka." (Yohane 10:10)
- Z. Woipayo** -"Munthu ali yense wakumva mau a ufumu, osawadziwitsai, woipayo angodza, nakwatula chofesedwacho mu mtima mwache." (Mateyu 13:19)

VI. MAINA A MIZIMU YOIPA

- A. Mzimu wakumdwalitsa (Luka 13:11)**
- B. Mzimu wosalankhula ndi wogontha (Marko 9:25)**
- C. Mzimu wonyatsa mau amenewa agwiritsidwa ntchito malo okwana 22 (Mateyu 12:43; Marko 1:23; Luka 9:42)**
- D. Mzimu wozolowereka(wobwebweta) (Levitiko 20:27; 2 Mafumu 23:24;Yesaya 8:19)**

Mizimu yoipa (yomwe sianthu) ndi yodziwika kwa maonekedwe a anthu opita (omwalira), zokonda zao ndi moyo wao.

Mizimu yoipayo imachita zinthu zofana ndi zomwe munthu yemwe anamwalirayo ankachita pofuna kuwasocheretsa anthu olira kuti ayambe kutsatira mizimu yoipa. Zochitikazi zimakhala zooneka ndi zauzimu. Komanso ndi zabodza. Anthu ambiri anyengedwa mpaka kuyamba kukhulupirira kuti wobwebwetayo anali mchiyanjano ndi wokonededwayo anamwalirayo ndipo iwo anayamba kukhala ndi chidwi ku mizimu yoipa.

Obwebweta mu nthawi yawo yakupembeza, amakhala atazazidwa ndi kulamuliridwa ndi mizimu yoipa.

- E. Mngelo (2 Akorinto 11:14)**
 - 1. Mzimu wonyenga
- F. Mzimu wonama (1 Mafumu 22:22-23; 2 Mbiri 18:21-22)**
- G. Mizimu yosocheretsa (1 Timoteo 4:1)**
 - 1. Zilakolako zoipa
 - 2. Chigololo
 - 3. Chiwerewere
 - 4. Kukwatirana kwa amuna okhaokha
- H. Mzimu woipa (Marko 9:25; Chibvumbulutso 18:2)**

I. Mzimu wa nsanje (Numeri 5:14,30)

1. Mkwiyoy
2. Udani
3. Kutaya mtima

J. Mzimu wa mantha (2 Timoteo 1:7)

K. Mzimu wolosera (wobwebweta) (Machitidwe a Atumwi 16:16)

VII.UMO M'MENE UNGATETEZEKERE MKATI KATI MWA NKHONDO YA UZIMU

A. VALA ZIDA ZAUZIMU ZA MULUNGU (Aefeso 6:10-18)

1. Chapachifuwa chachilungamo.
2. Mu mchiuno momangiriridwa ndi choonadi mutaziveka.
3. Mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere.
4. Chisoti cha chipulumutso.
5. Chikopa chachikhulupiriro.
6. Lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu.

**B. "Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembezera oyera mtima onse."
(Aefeso 6:18)**

MAU OTSOGOLERA KUKUKHALA WOPHUNZIRA

I. MAU OTSOGOLERA KUKUKHALA WOPHUNZIRA

A. Kuitanidwa kuti ukhale wophunzira (Luka 14:25-27). Mau kudana ali ndi tanthauzo losiyana lero.

1. Kodi wophunzira ndi ndani?
 - a. Ndi munthu wochitetsa ndi wotsatira wa Yesu Khristu.
 - b. Ndi munthu yemwe waleka zonse ndi kutsata Khristu.
 - c. Ndi munthu amene amatha kupanga malamulo a moyo, osati a imfa (onani VII, B-4).
 - d. Kusi yana pakati pa kufalitsa uthenga ndi kupanga ena kukhala ophunzira.

B. Kuitana kuti ukapange ena kukhala ophunzira (Mateyu 28:19-20; 2 Timoteo 2:2)

II. ZOLINGA PA KUPANGA ENA KUKHALA OPHUNZIRA:- KUPITITSA MTSOGOLO UFUMU WA MULUNGU

A. Cholinga chakukhalira ophunzira ndi kukupangani inu kuti mukhale okwanira kukutumikira mu ufumu wa Mulungu.

1. Yesu anakhala zaka zitatu ndi theka kuphunzitsa anthu kuti akhale ophunzira. (Luka 9:62).

B. Chikhalidwe cha mpingo wake ndi zomukhuza kwambiri Yesu Khristu.

1. Makalata Chibvumbulutso (Chibvumbulutso 2-3) analembedwa ku mipingo isanu ndi iwiri (7) pokhuza zachikhalidwe chao cha uzimu.
2. Makalata a Chipangano Chatsopano ankapereka malangizo a moyo ndi chikhalidwe chachikhristu. Makalata amenewa, mwa njira zambiri, akutiunikira za chikhalidwe ndi mavuto a mpingo woyambawo.
3. Popanda kulenga chikhalidwe cha moyo mu mpingo ndiye kuti ufumu wa Mulungu sungapitirire pa tsogolo.
4. Zochitika zomwe zinaimitsa kupitirira (kusefukira) kwa moyo, kumapanga chikhalidwe cha imfa:
 - a. Kunyada (kuzikuza) - kuziona wekha kuti ndine wofunikira kwambiri, mzimu woima payekha kapena wokanika.
 - b. Kukonda koyamikidwa - kukonda kuonedwa pazomwe wachita; kukonda ukulu; kukhala ndi chidwi cha iwe wekha ngati ukulankhula ndi wina - kufuna kudziwika.
 - c. Kutsutsana - mzimu wolongolola kwambiri; kuvuta, mzimu wosaphunzitsika; woganiza zako zokha, wosapindula, wokhala penapaliponse; mzimu woumiriza mzimu wolamulira mzimu wonyoza; wosamvera anzake, nkhwani, chikondi chonyengereredwa kapena phwete.
 - d. Kupezera ena zifukwa - kulankhula kwa zovuta ndi zolephera za ena m'malo monena za amene ali ndi luso ndi kuwathokoza kuposa iwe mwini.
 - e. Chilakolako - zilakolako zokhalitsa; machitidwe oipa; kusatsiriza kwa zofuna zake

ndi zozolowera kwa munthu wa chiwalo chosiyana ndi ena; chisiriro.(mwamuna ndi mkazi)

- f. Kusakhulupirika - mtima wonyenga; kubisa choonadi.
- g. Umbombo - chikondi cha pa ndalama ndi zofewa, ulesi , kuziganizira iwe wekha pakati pa anzako.
- h. Kukonza (Kuzolowera) - moyo wauzimu wakufa; osakhuzidwa ndi miyoyo; kuuma mtima ndinso kulekana maganizo.

III. ZIMENE YESU ANAPHUNZITSA PA KUKHALA OPHUNZIRA

A. Wophunzira ayenera kukhala monga m'phunzitsi wake (Mateyu 10:24-25, Luka 6:40).

- 1. Kuchita ntchito zomwe Yesu anachita iwe kukhala m'moyo umene anakhalamo kudzakhalala kuziika wekha pa mwamba pomposa lye (Yohane 14:12).
- 2. Tiyenera kutsatira chitsanzo chake (1 Petro 2:21-23; 1 Yohane 2:6).

B. Uzikane (Uziwale) wekha, tenga mtanda wako ndi kutsatira Yesu (Mateyu 16:24-25; Marko 8:34-35; Luka 9:23-24).

C. Ngati mukhala inu m'mau anga, muli akuphunzira anga ndithu (Yohane 8:31).

- 1. Njira zomwe zimatsamwitsa Mau m'miyoyo yathu ndikutipangitsa ife kusabala zipatso (Marko 4:13-19)
 - a. chinyengo cha ulemerero
 - b. zokhumbira za dziko lino
 - c. zilakolako pa zinthu zina (1 Yohane 2:15-17)
- 2. Kulola mau a Mulungu kuti akhale mwa inu kuti mubeleke zipatso kukuthandizani kuti mukhale wophunzira wake (Yohane 15:7-8).

D. Ngati simufa kuzifuniro zanu zimungabeleke zipatso zochuluka (Yohane 12:24).

IV. UMO M'MENE YESU ANAKONDERA NDI UMO M'MENE ANAYENDERA - ZIMENE IYE ANANENA

A. Kugwirizana kwake ndi Atate.

- 1. M'mapemphero (Marko 1:35; Luka 6:12)
- 2. Kusala kudya (Luka 4:1-4)

B. Chikhalidwe cha moyo wake.

- 1. Anakaniza ndikugonjetsa mayesero adziko lapansi, thupi ndi satana (Luka 4:1-13).
- 2. Anazuzidwa, pokhala yekhayekha, ndinso pokanidwa (Mateyu 10:25; Luka 9:22,58).
- 3. Anapirira mtanda (Ahebri 12:2) ndipo anakhala moyo wotumikira ndi woziipereka nsembe (Luka 22:27; Aefeso 5:2)

C. Maganizo ake pamodzi ndi chikhalidwe chake (Afilipi 2:5-8; 1 Petro 4:1,2).

KUKHALA WOPHUNZIRA

I. UBWINO WA CHIPANGANO CHATSOPANO POYEREKEZA NDI CHAKALE.

A. Kuona za chipangano Chatsopano

1. Uthenga wabwino - zimakhuza za kuonetsedwa kwa chipulumutso chathu.
2. Machitidwe a Atumwi - bukhu lambiri yolongosola za chipulumutso chathu ndi ufumu wa Mulungu.
3. Makalata - mabuku a chiphunzitso olongosola za chipulumutso chathu ndi ufumu wa Mulungu.
4. Chibvumbulutso - bukhu la uneneri lomwe limakhuzana ndi kumaliza kwa chipulumutso chathu.

B. Kuona za mabukhu a Uthenga Wabwino

1. "Uthenga" utanthauza mbiri yabwino.
2. Mauthenga abwino (olembedwa ndi alembi anayi osiyanasiyana) uli wonse wolembedwera gulu losiyana ndi zolinga zosiyana.
3. Zofanana kapena zosiyana m'mauthenga a Mateyu, Marko ndi Luka poyerekeza ndi uthenga wa Yohane, (Mateyu 58%; Marko 93%; Luka 42%; Yohane 8%)
 - a. Zofana za uthenga wabwino zomwe Yesu anafotokoza adakali munthu ndinso anzichita. Ali ndi zodabwitsa zambiri.
 - b. Yohane akunenetsa za umulungu wa Yesu ndinso kuti Iye ndi ndani.
 - c. Mabukhu a Uthenga Wabwino amene ali ndi zofanana zambiri amaonetsa Yesu ali kuphunzitsa zaufumu wa Mulungu mu Galilea.
 - d. Yohane akuimira Yesu ku Yerusalem komwe Yesu akuziulula yekha kuti Iye ndi Mulungu wobadwa, Mulungu m'thupi.
 - e. Mu Yohane, tiona Yohane ali ngati mtolankhani akufotokoza malankhulidwe ndi kukuma kwa Yesu ndi anthu.
4. Zamoyo(Zirombo) zinayi zimaimirira mauthenga anayinso (Chibvumbulutso 4:7)
 - a. **Mkango(Mateyu)** - Yesu ankafotokozedwa ngati "Mkango wa fuko la "AYuda"
Unalembedwa kwenikweni kwa Ayuda (nkhani 29 za Mchipangano Chakale kufotokozedwa mbukhu limeneli) Iye, Yesu, ali kuonetsedwa monga Mfumu.
 - b. **Munthu (Marko)** - bukhu losakuluwika ndi losavuta ndi umunthu wake linalembedwa kwa Aroma. Bukhu limasonyeza mphamvu zake; Ankafotokozedwa ngati wogonjetsa ena.
 - c. **Ng'ombe za ngolo (Luka)** - inanena za ntchito ndi zopereka nsembe. Yesu ankafotokozedwa ngati mtumiki wamkulu. Uthengawu unalembedwa kwa ahelene omwe anali ndi maganizo kwa munthu. Yesu, mwana wa munthu, akupherezera kukwaniritsa ganizoli.
 - d. **Chiombankhanga(Yohane)** - Uthenga kwa onse, Chiombankhanga ndi

chizindikiro cha ulemerero(ulemu) ndi mphamvu zonse. Chionetsera umulungu wa Yesu, Mwana wa Mulungu.

- 1) Mkango, ng'ombe za ngolo ndi munthu ali panja pa khomo.
- 2) Chiombankhanga chili pa khomo m'malere. Ichi ndi chizindikiro choti Yesu ndi wochokera kumwamba.

II. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI MATEYU

A. Mutu wake

1. Mutu wake wa pakati: Yesu ndi Mesiya kapena Mfumu. (Mateyu 2:2, 21:5, 22:11; 25:34, 27:11,27:42).
2. Unalembedwa kwa Ayuda. Podziwa za zoyembekezera zao za Mesiya wolonjezedwa, Mateyu akulongosola zoti Yesu ndi yemwe wapherezera m'malemba a chipangano chakale ngati Mesiya (Genesis 3:15;22:18,49:10, Deutoronomo 18:15; Yesaya 2:4, 7:14,9:6, 11:1,28:16,42:1,53 nkhani yonse) 59:16,61:1,63:1, Yeremiya 23:5. Danieli 9:25; Mika 5:2; Hagai 2:7; Zakariya 3:8, 6:12, 9:9, 11:12, 12:10, 13:7; Malaki 3:1).
3. Kugwiritsa ntchito ndime za m'Chipangano Chakale zikusonyeza monga umo m'mene Mesiya Mesiya ayenera kukhalira. Zochitika za Yesu zikusimikiza kuti lye ndi Mesiya.
4. Kugwiritsagwiritsa ntchito kwa mau "ufumu" ndi "ufumu wa kumwamba" mu Mateyu (kunaoneka makumi asanu mwina makumi atatu mogwirizana).
 - a. Ufumu womwe ukufotokozedwa ndi Mateyu ndi ufumu womwewo udalonjezedwa m'Chipangano Chakale.
 - b. Yohane Mbatizi analalikira kale za ufumuwu (Mateyu 3:2)
 - c. Yesu analalikira za ufumuwu (Mateyu 4:17)
 - d. Mpingo tsopano ndiye chikwaniritso cha ufumu umenewu.
 - 1) Tiri kuonanso m'chigonjetso pakubwera kwachiwiri kwa Yesu.

B. WOLEMBA

1. Mateyu akuyamikiridwa kwambiri ndi odalilika pazofufuza chifukwa cholembe uthengawu.
2. Mchipanano chatsopano zochepa zanenedwa za Mateyu. Iyeyu anali wokhomesa nsonkho mboma la Aroma ndipo anaitanidwa ndi Ambuye kuti akhale wophunzira ndi mtumwi (Mateyu 10:3; Marko 2:14).

C. ZA MKATI

1. Kubwera kwa Mesiya (Mateyu 1:1 mpaka Mateyu 4:11)
2. Utumiki wa Mesiya (Mateyu 4:12 mpaka Mateyu 16:12)
3. Nsembe ya Mesiya (Mateyu 24: mpaka Mateyu 27)
4. Kupambana kwa Mesiya (Mateyu 28)

III. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI MARKO, WOLEMBEDWA MCHAKA CHA 67-70 YESU

ATABADWA

A. Mutu wake

1. Yesu ngati Mwana wa Mulungu.
2. Unalembedwa kwa Aroma, anthu ankhondo. Yesu akuonetsedwa ngati "mkulu wa chipulumutso chatu ndinso "wogonjetsa ena onse."

B. WOLEMBA

1. Marko anali mwana wa Maria, mkazi waku Yerusalem, yemwe nyumba yake inatsegulidwa kwa akhristu oyamba aja (Machitidwe a Atumwi 12:12)
2. Marko anatsagana ndi Paulo ndi Barnaba pa ulendo wao woyamba wofalitsa chikhristu, koma anabwerera ku Yerusalemu. Kenako Barnaba anapereka ganizo loti paulendo wao wachiwiri amtenge Marko koma sanagwirizane pakati pa Paulo ndi iye. Barnaba poona kuti Marko ayenera kukhala ndi mwayi wozipulumutsa yekha, analekana ndi Paulo ndipo anamtenga Marko kulowera ku Kupro (Machitidwe a Atumwi 15:36-41). Kenako kafukufuku wao akusonyeza kuti Yohane Marko zinamuyendera bwino pa ntchito yake. (2 Timoteo 4:11; 1 Petro 5:13).
3. Dzina la chiroma loti "Marko" likusonyeza kuti iyeyu anakulira ku chiroma, chomwe chinamchititsa kukhala woyenera kulemba uthenga wopita kwa Aroma.

C. ZA MKATI

1. Kubwera kwa mgonjetsi wa mkulu.
 - a. Dzina lake pamodzi ndi kufalitsa kwake (Marko 1:1-8)
 - b. Chigonjetso chake pa satana. (Marko 1:9-13)
 - c. Kulalikidwa koyamba kwa Ufumu Wake (Marko 1:14-20)
 - d. Ntchito zake zoyamba za mphamvu (Marko 1:21-2: 12)
2. Kukangana (kulimbana) kwa Mfumu ya mphamvu.
 - a. Kusanja (kulowetsa) kwa mitu ya ufumu wake - atumwi, anthu wamba ndi ochimwa odwala ndi osowa (amphawi). (Marko 2:13-3:35).
 - b. Kulongosola kakulidwe ka ufumu wake (Marko 4:1-34) kugonjetsa zachilengedwe, ziwanda, nthenda, ndi imfa (Marko 4:34-5:43).
 - c. KUSUSIDWA NDI ANTHU (Marko 6:1-6), Herod (Marko 6:14-29), alembi ndi Afarisi (Marko 7:1-23, 8:10-12).
3. Mgonjetsi aitanitsa (afotokoza) ufulu wake ku ufumu wa mphamvu.
 - a. Kuphunzitsa otsatira ake m'mene chigonjetso chingalandiriridwe mu ufumu wake, mwa njira ya kuzunzika mpaka imfa (Marko 8:31-38; 10:28-45)
 - b. Kuvomereza ufulu wake ku ufumu polowa mu Yerusalemu mwachigonjetso (Marko 11:1-11), poyeretsa mnyumba(kachisi) yopemphereramo (Marko 11:15-19), pogonjetsa akuluakulu omwe ankamfutsa za ulamuliro wake (Marko 11:27- 12:44), ndinso polotsera kunenera za kubwera kwake kachiwiri mu ulemu (Marko 13:1-37).
4. Kukonzekera zakukhazikitsa ufumu wake

- a. kukonzekera imfa (Marko 14:1-72)
 - b. kuzipereka ku imfa (Marko 15:1-47)
5. Kutenga kwa ufumu (mu uzimu)
- a. kugonjetsa imfa (Marko 16:1-14)
 - b. kutumiza omutsatira ake kuti akalalikire zakupambana kwake (Marko 16:15-20)

IV. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI LUKA MCHAKA CHA 62 YESU ATABADWA

A. Mutu wake

1. Yesu monga mwana wa munthu, mpulumutsi
2. Unalembedwa kwa anthu achihelene omwe ankafuna kuti anthu azikhala moyenera kuzochita zao, zanzeru ndi zolimbisa matupi ao, ndiponso zochita zao zinali za munthu (wangwiro) wabwino. Poona kufooka kwao polephera kupulumutsa munthu kuzera kuzophunzitsa zao, Ahelene odziwa za kuganiza kwambiri anaona kuti chiyembekezo cha chipulumutso chikanabwera ndi munthu woyera. Kukwaniritsa zosoweka za Ahelene, Luka akunena za Yesu monga munthu woyera woimirira ndi mpulumutsi wa anthu onse.

B. WOLEMBA

1. Luka anali mnzake wa Paulo mtumiki (Akolose 4:14; 2 Timoteo 4:11; Filemoni 24).
2. Zikuganizidwa kuti Luka anali mhelene pokhala iye dotolo ndiye kuti anali wophunzira kwambiri.
3. Zomwe Luka walembe zikusonyeza kuti anali munthu woganiza bwino, wolembe kwa Ahelene obindikira ndi oganiza mwakuya mndandanda wake ngati munthu wolembe ndakatulo. Mu uthenga wonsewu kulankhula kwa Yesu kukusindikizidwa ndi kutsutsidwa kwa zochita zake ndi zomwe akuzitsimikiza mu Uthenga wa Marko. Marko anadumpha zolembe zimene ziri zenizeni za Ayuda, kulankhula zochepa kapena osanenapo zokhuza kanthu zoneneredwa za Chipangano Chakale.

C. Zamkati

1. Mau otsogolera (Luka 1:1-4)
2. Kubwera kwa munthu wopatulika (Luka 1:5-4:13)
3. Kuyamba poyera kwa ntchito (utumiki) zake makamaka ku Galileya (Luka 4:14-9:50).
4. Ulendo wopita ku Yerusalemu (Luka 9:51-19:28)
5. Masiku otsiriza, kuphatikizirapo kupachikidwa kwake pa mtanda. (Luka 19:29 mpaka 23:55).
6. Kuuka kwake m'manda ndi kukwera kwake kumwamba (Luka 24:1-53).

V. UTHENGA WOLEMBEDWA NDI YOHANE MCHAKA CHA 80-90 YESU ATABADWA

A. Mutu wake

1. Yesu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wa moyo.
2. Zanenedwa kale kuti uthenga wa Yohane unalembedwa pofuna kuyankha pempho la mpingo womwe unali kale ndi mauthenga ena.

3. Unalembedwa patapita zaka zambiri mauthenga ena atalembedwa, Uthenga uwu unalembedwa kwenikweni ku mpingo. Ena anali mauthenga oyendayenda ndi cholinga chofalitsa uthenga mokhulupirika wolembedwera kwa munthu wosakhala wauzimu (wosapulumuka).

B. WOLEMBA

1. Unalembedwa ndi Yohane mtumwi yemwe mwa atumwi onse ankasangalala kukhala pafupi paubwenzi ndi mbuye wake. Iyeyu ankaziimira pa yekha, Petro ndi Yakobo.
2. Anali Yohane yemwe anasamira pa chifuwa cha Ambuye pa nthawi ya chakudya chomaliza cha mgonero; iyeyu ndi uja pamene ophunzira anathawa, anawatsatira Ambuye mpakana ku chiweruzo (Yohane 19:15); mwa atumwi onse, iyeyu ndi yemwe anaima pafupi ndi mtanda wa Ambuye kuti alandire mthenga wa imfa yake (Yohane 19:25-27)
3. Ubale wake ndi kugwirzana kwake ndi Ambuye pamodzi kwa zaka ngati mbusa ndiponso mlaliki, ndi woyenera kulemba Uthenga momwe mukupezeka zauzimu ndi zophunzitsa zokhuza umunthu wa Khristu.

C. Zamkati

1. Mau otsogolera ndi otsegulira ziganizo / (Yohane 1:1-18)
2. Utumiki wa pabwalo wa Yesu (Yohane 1:19-12:50). Yohane analemba milakuli yonse yomwe anaona kuti ndi yothandiza kwa owerenga kuti Yesu Khristu ndi mwana wa Mulungu.
3. Utumiki wa Yesu kwa ophunzira ake (Yohane 13:1-17:26)
4. Kuzunzidwa ndi kuuka m'manda kwa Yesu (Yohane 18:1-20:31).
5. Mau otsekera kumangirira (Yohane 21:24,25)

D. Maumboni a Umulungu wa Yesu

1. Kutsintha(kusanduliza) madzi kukhala vinyo kusonyeza kuti Yesu ndi mbuye wa kapangidwe kabwino.
2. Kuchiritsa mwana wa mfumu kuulula kuti Yesu ndi Ambuye wa kutali ndi 'malere.
3. Kuchiritsa mwamuna wopanda mphamvu posambira ku Betesda kuulula kuti Yesu ndi Ambuye wanthawi (munthu anadwaka kwa zaka makumi atatu ndi zisanu ndi zitatu = 38).
4. Kudyetsa anthu zikwi zisanu (5 000) kuulula kuti Yesu ndi Ambuye wa kuchulukitsa.
5. Kuyenda pa nyanja kusonyeza kuti Yesu ndi Mbuye wa lamulo la zolengedwa.
6. Kumchiritsa munthu wakhungu kusonyeza kuti Yesu ndi Mbuye pa matsoka.
7. Kudzutsidwa kwa Lazaro kusonyeza kuti ndi Ambuye pa imfa.
8. Maumboni ambiri a umulungu wa Yesu:
 - a. Yohane 1:1-5,14-18
 - b. Yohane 15:18-24

- c. Yohane 8:12
- d. Yohane 10:33-38,11:4
- e. Yohane 11:25-27
- f. Yohane 14:1-11
- g. Yohane 20:26-31
- h. Yohane 12:48-50

MACHIRITSO OCHOKERA KUMWAMBA

KODI NDICHOLINGA CHA MULUNGU KUCHIRITSA ONSE? KUPHATIKIZIRAPO INE?

I. ADAMU NDI HAVA M'MUNDA WA EDENI.

- A. Panalibe uchimo kapena matenda pa dziko lapansi munthu asanagwe..
- B. Ichi chisonyeza chifuniro chake cha Mulungu pamene analenga munthu.
- C. Kugwa kwa munthu mu uchimo kunapereka mpata ku tchimo ndi matenda mu dziko lapansi.
- D. Mulungu anapereka machiritso ngakhale munthu anagwa..

II. MACHITIDWE A MULUNGU MU CHIPANGANO CHA KALE.

A. Masalimo 145:1-21

- 1. "UBWINO WONSE" kutanthauza kuonetsa chifundo ndi chisomo. (v. 8)
- 2. "Yehova achitira zokoma onse (v. 9)
- 3. "Ndi nsoni zokoma zache zigwera ntchito zache zonse." (v. 9b)
 - a. Ife tili mbali imodzi ya ntchito zake (Aefeso 2:10)
 - b. Dziko lapansi ndi mbali imodzi ya ntchito zake.

B. Iye ndi Yehova yemwe amandichiritisa ine. (Eksodo 15:26)

- 1. Palibe malo mbukhu lopatulika pomwe anena, "Ine ndi Yehova wakuononga iwe!"
- 2. Mchipangano Chakale chinali chifukwa cha kusamvera kwa anthu a Mulungu kuti zinthu zoopsazi zichitike.
 - a. Kunali kufuna(kusankha) kwao kuti asamvere Mulungu (Deotoronomo 28:58)
 - b. Mulungu analolera kuti zinthuzi zichitike; Iye sanazilamulire izo kuti zichitike.
- 3. Kodi Mulungu amatumiza nthenda kwa anthu?
 - a. Yesu anati, "Siidza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga." (Yohane 10:10)
 - b. Amawalola anthu kuti aphe, abe, amwe ndi zina zotere koma samawatumiza kuti achite zimenezi.

C. Masiku ako ndizawakwaniritisa (Eksodo 23:25-26)

D. Amafuna kuzionetsa Iye Yekha wamphamvu pakati pa amene mitima yao ili yoyera mwa Iye (2 Akolose 6:9).

E. "Palibe choipa chidzakugwera, ndipo cholanga sichidzayandikiza hema wako (Masalimo 91:10,16).

F. "Yemwe achiritisa nthenda zako zonse." (Masalimo 103:2-3) onani liwu "zonse."

G. Atumiza mau ache nawachiritisa, Nawapulumsa kuchionongeko chao (Masalimo 107:20). Awa ndi mau aulosi. okhuza Yesu Khristu, yemwe ndi Mau.

III. ANAYAMBITSA MATENDA NDANI?

A. Satana anazunza Yobu ndi zirona zowawa (Yobu 2:7).

B. Satana anam'manga mkazi zaka khumi, zisanu ndi zitatatu(18) ndi mzimu

wachisautso (Luka 13:16).

1. Mwana wa mkazi walonjezo la Abrahamu.
2. Satana anam'manga mkaziyu; Yesu anam'masula!

C. Anatembenuziridwa kwa satana yemwe anaononga thupi lake (1 Akorinto 5:5).

D. Yesu: anachiritsa onse omwe anavutitsidwa ndi mdierekezi (Machitidwe a Atumwi 10:38).

1. Matenda ndi chisautso ndi ukapolo wa satana.
2. Mphatso ina iliyonse yabwino ichokera kwa Mulungu (Yakobo 1:17). Kuchiritsidwa ndi mphatso yabwino
3. "Pakuti iye amene Ambuye amkonda a mlanga" (Ahebri 12:6).
 - a. Kodi kudwala ndi chilango cha Mulungu?
 - b. Palibe zogwirizana ndi kudwala mu m'malembawa.
 - c. "Kulanga" atanthauza kuti "kuphunzitsa mwana." "kulangiza ndi kumukonza"
 - d. Akhristu (angobadwa kumene) ayenera kulangidwa (kuphunzitsidwa) ndi Ambuye chifukwa akuphunzira ndi kukhwima (kukula) mu uzimu.

E. Satana wonyenga (Chibvumbulutso 20:3,10)

1. Kunyenga kutanthauza ku mchititsa wina kukhulupirira chinthu chomwe sichili choona.
 - a. Satana adzayetsesa kukunyengeza iwe, kukukhulupiritsa kuti Mulungu osati iye, amaika/matenda pa iwe.
2. Satana amanyengeza kuti usachite zomwe zomwe udziwa.

IV. YESU KHRISTU MCHIRITSI

A. Yesu: Wodziwika mbuku lonse la Chipangano Chakale.

1. Khristu (pasika) wathu (1 Akorinto 5:7)
 - a. Pasika m'Chipangano Chakale ndi mtundu wa nsembe ya Khristu..
 - b. Yesu nsembe yathu (Yohane 10:11).
2. Chithunzithunzi cha uneneri (Eksodo 11:1 mpaka 12:51)
 - a. Imfa ndi chiweruzo choyera cha tchimo (Eksodo 11:5)
 - b. Nsembe ya nkhusa:mLOWAMALO (Eksodo 12:3)
 - 1) Yesu anali mwana wa nkhusa wa Mulungu (Yohane 1:29)
 - 2) Anali mLOWAMALO wa machimo athu (Agalatiya 1:4)
 - 3) Mulungu anazipereka yekha chifukwa cha ife (Tito 2:14)
 - 4) "Pa nyengo yache Khristu anawafera osapembedza." (Aroma 5:6)
 - c. Kudutsa (kuwoloka) kwa nyanja yofiira ndi mtundu wakubadwa mwa tsopano.
 - 1) Kanani ndi mtundu wa dziko lathu lamalonjezano.

- a) Tiri ndi mphamvu yakusankha.
- b) Tiyenera kumenya nkondo posunga zimene ziri zathu.
- 2) Mulungu anaziwonetsa yekha powaturutsa a Israeli mu ukapolo
 - a) Yesu anaonetsedwa kutitulusa mu uchimo (1 Yohane 3:5)
 - b) Yesu anaonetsedwa kuononga ntchito zake za mdierekezi (1 Yohane 3:8)
- d. Kuyamba kwa tsopano (Eksodo 12:2)
 - 1) Anasankha nkosa (Eksodo 12:5)
 - a) Yopanda chilema cholakwa (yopanda kenakalikonse koidetsa)
 - (1) Yesu analibe tchimo mwa Iye (2 Akorinto 5:21)
 - (2) Analibe chirema ndi kenakalikonse chidetso (1 Petro 1:19)
 - (3) Analibe chovuta chili chonse mwa Iye (Yohane 19:6)
 - (4) Anayetsedwa mwa njira iriyonse koma analibe tchimo (Ahebri 4:15)
 - b) Onetsetsani "mwana wa nkosa" alibe mchulukitsi wake wa mau(Pulula). Mulungu anali ndi mwana wa nkosa imodzi m'maganizo: Yesu.
 - 2) Kutenga kwa mwana wa nkosa (Eksodo 12:8-11)
 - a) Kumphamvu za matupi ao
 - b) Mulungu amawakonzekeretsa iwo za ulendo wautali.
 - c) Panalibe wopanda mphamvu pakati pao (Masalimo 105:37)
 - d) Yesu amapereka zomwezinso (1 Akorinto 11:23-34).
 - (1) Paulo anali ndi vumbulutso mwa Yesu (1 Akorinto 11:23)
 - (2) Kulizindikira kwa thupi la Ambuye (1 Akorinto 11:30)
 - (a) **"Wofooka"** - wopanda mphamvu, wopindika, wodwala, (kufooka kwa thupi)
 - (b) **"Wodwaladwala"** - amene mphamvu zake zatha chifukwa cha nthenda.(matenda).
 - (c) **"Kugona"** - kumwalira; kupita kunyumba kokakhala ndi Atate.
 - (d) Ichi ndi chifukwa chachikulu chomwe akhristu ndi odwala lero. Sazindikira thupi la Ambuye.
 - (3) Kuona(uziyese) wekha (1 Akorinto 11:28)
 - (4) Landira machiritso kudzera mu mgonero wa Ambuye.
 - (a) Mwazi wake umapereka ufulu kuchoka ku machimo.
 - (b) Mikwingwirima yake imapereka ukhondo ku matupi athu (1 Petro 2:24)

B. Anawachiritsa onse.

1. Atate amachita ntchito (Yohane 14:8-10)

- a. Ngati mufuna kuona Atate, onani Yesu.
 - b. Yesu anaulula kwa anthu maganizo a Mulungu nzochitika.
 - c. Yesu anachita zofuna za Mulungu (Yohane 6:38)
 - 1) Zochitika zonse za Yesu pamodzi ndi mau ake zinali zoti awononge ntchito za satana (1 Yohane 3:8)
 - 2) Chinali chifuniro cha Mulungu ntchito iliyonse ya mphamvu ndi chichiritso. Ntchito ina ili yonse ya mphamvu, machiritso onse, chinali chifuniro cha Mulungu.
2. Yesu anachiritsa anthu ambiri (Mateyu 14:14)
 - a. Anabwera kuyembekezera kuti alandire.
 - b. Anabwera kuti achiritsidwe.
 - c. Palibe ndi munthu m'modzi yemwe Yesu sakanatha kumuchiritsa pakati pa unyinji. Panali anthu abwino pamenepo: panali anthu oipa pamenepo.
 3. Yesu anachiritsa nthenda iliyonse ndi zofooka zonse (Mateyu 9:35)
 4. Anawachiritsa onse (Mateyu 12:15)
 5. Anawachiritsa (Mateyu 15:30-31)
 6. Anasanjira manja kwa onse ndipo anawachiritsa (Luka 4:40)
 7. Anawachiritsa onse (Luka 6:17-19)
 8. Kodi anachiritsa ena? **AI!** Anachiritsa **ONSE** omwe anagwidwa ndi matenda (Machitidwe a Atumwi 10:38).
 9. Pali malo amodzi okha omwe Yesu anaphimbidwa kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu m'miyoyo yao (Marko 6:5-6).
 - a. Yesu anazizwa ndi kusakhulupirira kwao.
 - b. Kukaika kunawalanda iwo dalitso la Mulungu.
 - c. Yesu sanangonyamuka ndi kuwasiya popanda kanthu; ankayenda "m'midzi yodzungulira akuphunzitsa" (v. 6). Mau ankawasintha osakhulupirira kukhala ndi chikhulupiro. (Aroma 10:17).
 10. Mphamvu zochiritsa zinkazera mwa Yesu, kuchiritsa aliyense yemwe ankabwera kwa iye ndi chikhulupiro.
 - a. Pamene Yesu anapita kukakhala pa dzanja lamanja la Mulungu anapereka mphamvu ku mpingo (thupi lake) ndipo mphamvu inkatsikira kuzera ku mpingo woyambirira (Machitidwe a Atumwi 5:16).
 - b. Imatsikirabe kuzera mthupi lake lero pamene tisanjika manja kwa odwala (Marko 16:18)

C. Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi lero ndi ku nthawi zonse.(Ahebri 13:8)

D. Machiritso anaperekedwa kudzera mu chiombolo

1. Yesaya 53:3-5

- a. "Zowawa" ndi "zisoni" sanathandauziridwe bwino mu bukhu lopatulika la Mfumu Yakobo.
 - 1) "Zowawa" (mchihebri "cholly") litanthauza kuti "kudwala" kapena "nthenda."
 - 2) "Chisoni" (mchihebri "makobah") litanthauza "kupweteka."
 - b. "Nyamulidwa" litanthauza "kuchikweza m'mwamba, kuchisuntha kupita ku malo ena."
 - 1) Tchimo ndi kudwala zachotsedwa kwa ine ndi kupititsidwa ku mtanda.
 - 2) Chipulumutso ndi umoyo zachotsedwa ku mtanda ndi kudza kwa ine.
 - c. "... ndi mikwingwirima yake tachiritsidwa" (v. 5).
2. **"Munachiritsidwa"** (1 Petro 2:24).
 - a. Ntchito yomalizidwa - ali m'mau osonyeza kuti ntchito inachitidwa kale.
 - b. Ngati "ndi mikwingwirima yake mumachiritsidwa" chomwecho machiritso ndi anu lero..
 3. Iye anamyamula matenda athu (Mateyu 8:17)
 4. Jehovah Rapha - Yehova mchiritsi wathu (Eksodo 15:26).

E. Mtima wa Yesu wofuna kuchiritsa ena (Luka 5:12-13).

1. "Khate thupi lonse" limasonyeza gawo lotsiriza la nthenda.
2. Anali wodetsedwa kumbali ya chilamulo cha Ayuda.
 - a. Ananyoza lamulo. b. Anapempha chifundo. c. Chiyembekezo chake chotsiriza anali Yesu.
3. Yesu mwatchutchutchu anayankha funso lokhuzana ndi kufuna kwake kuti achiritse, kunena kuti "Ndikufuna, konzeka"
 - a. Munthu wakhalte ankadziwa kuti Yesu akhoza kumuchiritsa iye, sankadziwa kuti angamuchiritse.
 - b. Chomukhuza chinali "Yesu mungandichiritse ine kodi?"
 - c. Yankho la Yesu kwa onse linali :Nditha." (ndi kuchiritsa).

V. NJIRA ZAPAFUPI ZISANU NDI ZIWIRI ZOMWE MULUNGU AMACHIRITSIRA

Mungathe kumasula chikhulupiriro chanu m'njira izi:-

1. Kupemphera mdzina la Yesu (Yohane 16:23)
2. Kusanjika manja (Marko 16:18; Ahebri 6:2)
3. Kudzodza ndi mafuta (Marko 6:13; Yakobo 5:14).
4. Kutulusa mzimu woipa (Mateyu 8:16; Luka 13:11-13).
5. Pemphero logwirizana (Mateyu 18:19)
6. Pemphero lomanga ndi lomasula (Mateyu 18:18)
7. Kutenga mau a Mulungu ngati mankhwala (Miyambo 4:20-22).

VI. KUCHITA PA MAU A MULUNGU

A. Ungathe kulemba tikiti yako ndi Mulungu (Marko 5:25-34)

1. Chinene! Iye anati (v 28)
2. Chichite! Iye anadza (v. 27)
3. Chilandire! Iye anachimva (v. 29)
4. Lankhula! Iye analankhula (v. 33)

B. Chitani chisankho chosabwerera m'mbuyo!

C. Landirani machiritso akumwamba kwa inu nokha.

D. Khazikitsani chikhulupiro chosagwedezeke.

E. Mkanizeni mdierekezi ndipo iye adzakuthawani (Yakobo 4:7).

UTUMIKI WOFALITSA UTHENGA WABWINO

I. UTUMIKI WOFALITSA UTHENGA WABWINO UFOTOKOZEDWA (LUKA 19:10)

A. Penyani (Yohane 4:35).

1. Uyenera kukhala nao maso-mphenya (bvumbulutso) kuti ukathe kukafikira anthu ena ndi Uthenga Wabwino (MIYAMBO 29:18)
 - a. Antchito (MATEYU 9:37-38; YOHANE 5:17)
 - b. Anyengo (YOHANE 4:23; LUKA 17:26-30).
 - c. Agahena ndi umo m'mene wochimwa aliri (MASALIMO 9:17; MIYAMBO 27:20; LUKA 16:19-31).
2. Uyenera kukhala ndi chifundo pofuna kuti ukathe kukafikira anthu ena ndi Uthenga Wabwino (MATEYU 9:36; 14:14).
 - a. Chifundo si chisoni ayi. Chisoni chimangovutika; chifundo chimachita.
 - b. Ndi chikhalidwe cha nkhanza kumaona anthu akupita ku gahena, ndipo iwe osasunthika ndi kuchitapo kanthu.

B. Pitani (Marko 16:15)

1. Akhristu ambiri sapita chifukwa ali ndi mizimu yofooka.
 - a. Iwo ndi amantha (2 TIMOTEO 1:7).
 - b. Iwo ndi aulesi (MIYAMBO 6:6-9, 10:26, 26:14).
2. Mzimu wako uyenera kukhala m'malo abwino pofuna (oyenera) "kupita" chifukwa cha Yesu. Uyenera kukhala wodzala ndi nyonga, chimwemwe ndi mphamvu.
3. Mzimu wamphamvu umalandiridwa kupyolera mkuwerenga Mau a Mulungu - Baibulo, kupemphera m'malilime ena pamodzi ndi kumulambira Yesu.

C. Uzani (Marko 5:19; 16:15)

1. Aliyense ali nawo umboni (Yohane 4:28-29) Upangeni ukhala waufupi!
2. Lalikani Uthenga Wabwino osati mbiri yoipa. Chitsanzo choipa: "Iwe wochimwa wakuda, leka kuledzera ndi kusuta kwako ngati sutero basi iwe upita ku gahena!" Umenewu siuthenga Wabwino ayi.
3. Mzimu Woyera angathe kukupatsa mawu amene sunawaganizire ndi kale lomwe (Marko 13:11).

II. ZIDA ZOGWIRITSIRA NTCHITO POFIKIRA ENA NDI UTHENGA WABWINO

A. Chikondi ndicho chida chanu chachikulu popindula miyoyo kwa Yesu.

1. Kumbukani mtundu wa Mzimu umene inu muli.
 - a. Nthawi zonse tsogoleredwani ndi kulumuliridwa ndi chikondi.
 - b. Musapikisane (kulimbana); mayankhidwe ofatsa aletsa mkwiyo (MIYAMBO 15:1).
 - c. Mwaitanidwa kulalikira Uthenga Wabwino, osati kuuteteza ayi.

2. Ngati simukutsogoleredwa ndi chikondi, simungathe kumupatsa Yesu ulemerero (1 AKORINTO 13:1)

B. Mphamvu ndi Ulamuliro (Machitidwe a Atumwi 1:8)

1. Mawu anu angathe kukhala odzala ndi mphamvu komanso ulamuliro (MARKO 1:22; LUKA 4:30-32).
 - a. Yesu anadzudzula ziwanda (LUKA 4:35).
 - b. Yesu anadzudzula malungo (LUKA 4:39).
2. Musadzaiwale chimene Yesu ali ndi chimene lye angachite (MARKO 16:20).
 - a. Yesu ali pamwamba pa mdierekezi, nthenda ndi chisautso china chiri chonse (YOHANE 3:31).
 - b. Dzina la Yesu ndi lanu! Ligwiritseni ntchito!
 - c. Munthu wochimwa musamupatse "Chipembedzo," Mpatseni mphamvu ya Mulungu!

C. Nzeru (Miyambo 11:30; Yakobo 1:5)

1. Phunzirani nthawi yoyenera kulankhula ndi nthawi yoyenera kukhala chete (MATEYU 10:19).
2. Khalani ndi ulamuliro pa kukambira kwanu.
3. Ochenjera monga njoka ndi oona mtima ngati nkhunda (MATEYU 10:16).
4. Muyenera kudziwa Mau a Mulungu (2 TIMOTEO 2:15).

III. NJIRA ZOTHANDIZA POCHITIRA UMBONI

A. Mfundo zothandiza

1. Konzani "munthu wanu wa mkati."
 - a. Musakhale nalo tchimo lomwe simunalivomereza (simunalapa) mu mtima mwanu (1 YOHANE 1:9).
 - b. Pempherani musanapite.
2. Konzani "munthu wanu wakunja." Khalani zinthu zonse kwa onse (1 AKORINTO 9:22). Muyenera kuvala mosiyana pamene muchitira umboni kwa munthu wa Zamalonda ndi munthu amene ali mulimi.
3. Tengani Baibulo laling'ono kapena Chipangano Chatsopano pamene mukupita.
4. Pitani m'magulu, anthu awiri kapena atatu.
5. Onetsani chimwemwe ndipo khalani maso.
6. Musangolankhula nokha nthawi zonse. Adziweni amene mukulankhula nawo pokhala nanu omvetsela pamene iwo ali kulankhula.
 - a. Musamufunse munthu, "Kodi ndiwe Mkhristu wopulumutsidwa ... kapena wobadwa mwatsopano?" Ochimwa amalankhula mosiyana ndi anthu otembenuka.
 - b. Funsani, "Kodi munayamba mwaganizirapo, za kumalo komwe mudzakhale

nthawi zamuyaya?"

7. Musadzalole kukhala ndi chikhalidwe chonena kuti "ndine Woyera kuposa inu."
8. Dulani mzere ndime za m' Baibulo zomwe zilankhula za Chipulumutso ndipo muzidziwa malo onse amene ziri kupezerapo!
 - a. Khalani ndi chikonzero: kulunjika osati mokhotakhota ayi (Chitsanzo AROMA 3:10, 3:23, 5:8, 10:9-10).
 - b. Musafunse funso lomwe lingabweretse yankho loti "inde" kapena "ayi" (musalore kupatsidwa yankho loti "ayi"!).
 - c. Khazikitsani maziko olimba ochokera m'Mau a Mulungu pofotokoza za chipulumutso chawo.

B. Chisankho chopulumutsidwa nacho, ndi kuwatsatira opulumutsidwa!

1. Pemphero la wochimwa. : Lipangeni kukhala lalifupi ndi losavuta kotero kuti munthu wochimwa athe kulimvetsetsa. Mutatero pempherani pemphero lakuthokozza Ambuye chifukwa chopulumutsa m'bale kapena mlongoyo!
2. Kutsatira munthu yemwe wangopulumukayo.
 - a. Muwaonetsere kufunika kwake kwa kuvomereza chipulumutso chatu pabwalo (MATEYU 10:32-33).
 - b. Muwauze kufunika kwake kwakuwerenga Bukhu Lopatulika tsiku ndi tsiku.
 - c. Muwauze kufunika kwake kwa kupemphera ndi kulambira Ambuye tsiku ndi tsiku.
 - d. Muwauze kufunika kwake kopita ku tchalitchi kukapembedza pamodzi ndi anzawo nthawi zonse.
3. Muwathandize kukhala iwo "Ophunzira" a Yesu.
 - a. Muwauze chifukwa chake.
 - b. Muwauze m'mene angakhalire.
 - c. Muwathandize kuyambapo.
 - d. Muwathandize kupita patsogolo.
 - e. Muwathandize kupindula anzawo.

C. Kuchitapo kanthu kwa iwo amene ali ndi zovuta (2 Timoteo 2:23-26)

1. Kudzikhulukira kumene anthu amakugwiritsa ntchito, ndi mayankho a m'malemba amene mungathe kuwapatsa iwo.
 - a. **Anthu omwe sakhudzidwa:** Gwiritsani ntchito malemba omwe angabweretse kutsutsika kwa uchimo (MIYAMBO 27:1; LUKA 13:3; YOHANE 3:18; AROMA 6:23; AHEBRI 2:3).
 - b. **Anthu odzilungamitsa okha:** Muwaonetsere malemba omwe amanena za tchimo lodzilungamitsa (YESAYA 53:6, 64:6-7; AROMA 3:10; AEFESO 2:8-9; TITO 3:5).

- c. **Chinyengo mu Mpingo:** Muwaonetsere kuti tiyenera kuyang'ana kwa Khristu kuti tipulumutsidwe osati kuyang'ana kwa munthu (YESAYA 45:22; YOHANE 3:14-15; MACHITIDWE A ATUMWI 17:30-31; AROMA 14:12).
 - d. Kwa iwo amene akuganiza kuti machimo awo ndi aakulu kotero kuti sangathe kupulumutsidwa awonetseni kuti Mulungu ndi woleza mtima ndipo chikondi chake ndi chonka muyaya (MASALIMO 86:5; YESAYA 1:18; YOHANE 6:37; AHEBRI 7:25; 2 PETRO 3:9; CHIBVUMBULUTSO 22:17).
 - e. **Kwa iwo amene akuganiza kuti ali ofooka kotero kuti sangathe kuleka kuchimwa:** Muwaonetsere kuti pamene tilandira Khristu timakhala "atsopano" ndipo timalandira zikhumbo zatsopano (YOHANE 10:27-28; 1 AKORINTO 10:13; 2 AKORINTO 5:17; 12:9-10; 1 YOHANE 4:4; 5:12; YUDA 24).
 - f. **Kwa iwo amene akuti moyo wa Chikhristu ndi wovuta:** Muwaonetsere malemba amene amaonetsera kuti chikhristu sichipembedzo kapena mpukutu wa malamulo ayi, koma ndi chiyanjano ndi Mulungu (MATEYU 11:28-30; YOHANE 1:12; AFILIPU 4:13; 2 TIMOTEO 1:12).
 - g. **Kwa iwo amene akuti sali "oipa":** Muwaonetsere kuti Chipulumutso sichinagone pakuipa kapena ubwino ayi (MIYAMBO 14:12; MLALIKI 7:20; YOHANE 14:6; 1 YOHANE 1:8).
 - h. **Kwa iwo amene akufuna kuyembekezera:** Muwaonetsere kuopsa kwake kwa kuchedwa (MIYAMBO 29:1; LUKA 12:16-20; YOHANE 3:18; 2 AKORINTO 6:2; YAKOBO 4:13-14).
2. **Malembo ena ofotokoza za Chipulumutso:** (EZEKIELI 36:26; MATEYU 10:32, 16:26; LUKA 19:10; MACHITIDWE A ATUMWI 4:12; AROMA 14:11; 2 AKORINTO 5:21; AHEBRI 9:27).

MAUTUMIKI OCHITIKA

I. MAU OYAMBA: KUFOTOKOZA MAUTUMIKI OCHITIKA

II. KUITANA KWA MULUNGU

A. M'mene tingakudziwire?

1. Chinthu chongofika kuchokera kwa Mulungu. Suchita kusankha monga ntchito wamba.
2. Kukhudzika kwakukulu kapena chisoni chifukwa cha miyoyo ya anthu kudzatsagana nawe limodzi.
3. Pamene uli kukula, sudzakwanitsidwa ndi kanthu kena kali konse.
4. Zinthu ziwiri zingathe kukhalapo ngati Mulungu wakuitana, koma sungathebe kudzitsimikizira.
 - a. Nyengo (nthawi) zolakwika
 - b. Kulimbana kwa zokhumbira kolingana ndi zofuna zosiyanasiyana za iwe mwini, maganizo amagawikana.

B. Kudzipereka ku maitanidwe.

1. Uyenera kukhala ndi mphamvu za kuima ndi kugonjetsa zovuta.
2. Uyenera kukhala wokonzekera ndi kuphunzira mosalekeza.
3. Uyenera kukhala ndi moyo wopemphera ndi kusala kudy.

C. Zokuyenera ku utumiki (1 Timoteo 3:1-16).

1. Ukhale wa chikondi ndi wodziwa kumvetsa anthu.
2. Ukhale munthu wodalirika m'makhalidwe, wambiri yabwino kwa anthu akunja komanso mu mpingo.

D. Zotsogola (zofunika) m'moyo.

1. Mulungu ndi Mau Ake
2. Banja ndi pakhomo (m'nyumba)
 - a. Zokuyenera pa ukwati wabwino
 - b. Zokuyenera kwa ana abwino
3. Utumiki kapena mpingo
4. Ntchito

III. MBALI (MADERA) ZOCHITACHITA ZA UTUMIKI

A. Kuyang'anira - Machitidwe (makonzedwe) a zinthu ndi anthu.

1. Malongosoledwe (makonzedwe): Ngati pa khomo pako pali posakonzeka (poipa), motero uli iwenso (1 Timoteo 3:4)
2. Makonzedwe ndi kukhazikitsa cholinga.
3. Chuma.

- a. Makhalidwe ako pa za chuma cha iwe mwini, amakhudza makhalidwe ako pa za chuma cha Utumiki wako.
- b. Phunzira kulongosola za chuma.

B. Machitidwe (Makhalidwe)

1. Makhalidwe oipa
 - a. Kupsa mtima
 - b. Kudzikonda (chipongwe)
 - c. Kuweruza monyoza ena
 - d. Nsanje
 - e. Kunyada - Kudzikunza
 - f. Kupikisana
2. Makhalidwe abwino
 - a. Kudzichepetsa
 - b. Kuphunzitsika (Wokonda kuphunzira)
 - c. Wa chifundo
 - d. Wopilira
 - e. Wodziwa kupatsa/kuthandiza
 - f. Wolimba (Wokhala ndi changu.)
 - g. Wokonda ntchito.
3. Makhalidwe mu kulalikira

C. Maubale

1. Nthawi zambiri kupambana mu utumiki wako kudzatengera machitidwe ako pokhazikitsa maubale okwanira bwino.
2. Zinthu ziwiri za mphamvu zosoweka m'moyo ndi mu utumiki wako:
 - a. Chofunika, polandira chikondi, chitsimikizo (kuvomerezeka), kumvetsetsa, ndi kudekha (kufatsa).
 - b. Chofunika popereka chikondi, chitsimikizo, kumvetsetsa, ndi kufatsa.
3. Maubale a mtumiki - kwa - mtumiki (utumikilo wa malamulo oyamba a chikhalidwe chabwino).
 - a. Kuteteza maubale abwino ndi iwo omwe umawalemekeza ndi kuwapatsa ulemu.
 - b. Kuwakonda ndi kuwachitira zabwino omwe amakuipitsa (amakunyoza).
4. Maubale a ntchito
 - a. Kukhala ndi ulemu kwa iwo okhala nawo pamodzi - mbiri yabwino (Machitidwe a Atumwi 6:3).
5. Ubale woposa - Iwe ndi Mulungu

D. Maonekedwe a iwe mwini

1. Anthu amaona chomwe tili asanamve kuti ndi ife.
 - a. Umangokhala ndi mwawi (mwayi) umodzi wokha wakupanga chithunzi chabwino choyamba.
 - b. Timaonetsa makhalidwe athu kupyolera m'mavalidwe. Timaonetsa chikhalidwe chathu cha chiphunzitso cha moyo wathu kupyolera m'maonekedwe athu.
2. Umoyo (unkhondo) wa iwe mwini
 - a. Khala wa ukhondo ndi wodzisamalira
 - b. Khala ndi mpweya wabwino

IV. MAYESERO

A. Maganizo - Mayesero amayamba m'maganizo.

1. Chomwe umalingalira kwambiri chidzaganizira njira ya moyo wako.
2. Uyenera kuthetsa (kulimbana) mayesero pa mayambiro pake.
3. Kumbukira kuti cholinga cha satana ndi kuononga alaliki ndi ma utumiki.

B. Chokhumudwitsa - Mayesero okuletsa kuti usapite patsogolo.

1. Kodi ndi chiyani chimene chimamupangitsa mtumiki kufuna kusiya utumiki wake?
 - a. Kuweruzidwa kaya molungama kapena mosalungama
 - b. Kusoweka kwa kupambana kwenikweni mu utumiki wake
 - c. Kufanizira utumiki wake ndi munthu wina amene akuonetsa kukhala ndi kupambana koonekera.
2. Choyenera kuchita pa nthawi ya kukhumudwa
 - a. Zindikira kuti malingaliro ako ndi oyenera, a umunthu, ndi oneneka.
 - b. Bwerera ndi kukhazikika pa zofunikira (zotsogola) za moyo wako
 - c. Leka kukolezera moto kupyolera mu zokamba zopezera zifukwa ndi anthu ena.
 - d. Thandiza munthu wina yemwe ali pafupi ndiwe yemwe akusowa thandizo.
 - e. Moona, kumana ndi chifukwa chenicheni choyambitsa kukhumudwa. Anthu sapsa mtima kawirikawiri kapena kumva chisoni pa zifukwa zomwe iwo amaganiza.
 - f. Funa uphungu kuchokera kwa mtumiki mnzako yemwe ndi wozindikira ndi wodalirika. Chotsa kunyada kwako.
 - g. Yambitsa kusintha mu zochita (kapena m'malo opezeka) iwe, monga kuwerenga buku latsopano, kupita ku malo atsopano ndi zina zotere.
 - h. Kumbukira, iwe umapambana kapena kulephera kudzera ku zomwe umamva

C. Kulwana ndi yemwe sali wako - chiwerewere kapena chigololo)

1. Chidetso ndi chopundula, chononga, ndipo chidzaweruzidwa ndi Mulungu mopanda kukondera.

2. Pali magulu asanu a atumiki mwa kusamalira mayesero a thupi - kukhala pamodzi mwana ndi mkazi omwe sali amodzi mu ukwati.
 - a. Atumiki amene mosazolowera, amakumana ndi kukakamizika kwa mphamvu kulowa mu ubale woipa wogona mwamuna ndi mkazi molakwira malamulo a Mulungu.
 - b. Atumiki amene amakumana ndi mayesero koma kukwanitsa kulimbana nao movutika ndi kuwagonjetsa.
 - c. Iwo omwe amayesetsa kulimbana koma amagonjetsedwa nthawi zonse.
 - d. Iwo omwe samayesetsa kulimba koma movomereza ndi mopusa naononga zifundo za Mulungu,
 - e. Iwo omwe amalemekeza chikhalidwe cha chiyero koma mobisika amaopa kuvomereza mayesero mu nthawi ya kufooka.
3. Zolingirira za munthu pa kugonjetsa mayesero.
 - a. Sankha kukhala moyo wa umulungu, wopanda chidetso, ndi moyo woyera pamaso pa Mulungu ndi anthu.
 - b. Chotsa m'nyumba ndi m'moyo wako, ubale wina uli wonse wa chidetso kapena polowera pa satana kudzala mbeu za chisalungamo (chiwerewere).
 - c. Pewa kuchita uphungu ndi munthu amene sali wofanana nawe mchilengedwe (mwamuna kapena mkazi) popanda mkazi wako kapena mwamuna wako kapena wina aliyense wokhala ndi iwe.
 - d. Dzada pakamwa pako ndi mapembedzo ndi matamando mosalekeza.
 - e. Dyetsa maganizo ako tsiku ndi tsiku ndi Mau a Mulungu.

D. Chinyengo, kunena bodza, ndi kusinjirira (kuonjezera). Ungwiro ndiye mphamvu yosaoneka ya Mulungu ndi munthu. Ichi ndiye chofunikira chenicheni pomanga Utumiki wosatha ndi wopambana.

V. ZOLIMBANA (NKHONDO)

A. Mtumiki kulimbana ndi chikhalidwe cha dziko: Kumbukira kuti sulimbana ndi wochimwa koma adana ndi tchimo.

B. Mtumiki kulimbana ndi mtumiki mnzake:

1. Kumbukira, ndi chinthu chopusa kumalimbana ndi iwo omwe ali apanyumba pako m'malo molimbana ndi mdani.
2. Osaneneza wina aliyense popanda umboni.
3. Yang'anira Mau ako.

C. Mtumiki kulimbana ndi gulu la Mpingo:

D. Mtumiki kulimbana ndi aku mipando amnzake:

VI. KUPAMBANA MU UTUMIKI

A. Chifukwa chiyani atumiki (mautumiki) ena amalephera?

1. Kusasamala m'makhalidwe
2. Kulalikira moipa - Kutengedwa ndi phokoso (mtsutsano) chiphunzitso.

3. Ukwati wosakhala m'chifuniro cha Mulungu.
4. Kulephera kukhala wolimbika mu ntchito
5. Kugwiritsa ntchito chuma moipa (kusakaza chuma)
6. Kusoweka kwa kuphunzira ndi kukonzekera
7. Kusoweka kwa alangizi auzimu kapena alangizi achabe
8. Kukhumudwitsidwa (kubwezeredwa pambuyo) mu uzimu.
9. Kulowa mu utumiki asanakonzeke
10. Kunyada - kuopsa kwa kupambana mwachangu
11. Kumanga (kukhazikitsa) dzina/utumiki/mtundu wa chikhulupiriro m'malo mwa Ufumu wa Mulungu.

B. Zinsinsi zisanu ndi ziwiri zopambana (zabwino) pa Utumiki wopambana:

1. Dziwa mtundu wa maitanidwe ako.
2. Pezana (kuyenderana) ndi anthu odziwa kale.
3. Khazikitsa tsiku ndi tsiku makhalidwe opambana omwe adzakutengera ku malo komwe ukupita.
4. Kuphunzira zinthu zatsopano - Panga kuwerenga kwako kukhala kwa moyo nthawi zonse.
5. Khala ndi nthawi yabwino ya pemphero tsiku ndi tsiku
6. Khala mthupi la bwino ndi kupeza mpumulo wokwanira.
7. Khala wophunzitsika; vomereza uphungu ndi kukonzedwanso. Uyenera kukhala wokonzekera nthawi zonse kusintha ngati nkoyenera kutero.

MAZIKO A CHIKHULUPIRO

I. CHIKHULUPIRO NCHIYANI? TIMACHIPEZA BWANJI CHIKHULUPIRO?

A. Kufotokozero/Matanthauzo

1. Chikhulupiro ndi chionetsero chokhulupirika mwa Mulungu, chisankho chotsatiridwa ndi zochitika (ntchito) zake.
2. Chikhulupiro chenicheni mwa Mulungu, chikhulupiro cha mumtima, ndi kukhulupirira ndi kuchita momwe mau a Mulungu anenera, posayang'anira umboni wooneka.
3. Chikhulupiro sichinthu chomwe tikhala nacho kapena kuti chikhala chinthu chomwe tichita.
 - a. Chikhulupiro ndi dzanja lomwe limatenga zinthu zomwe tikuzifuna kwa Mulungu
 - 1) kutsogolera ndi fanizo: kulandira mphatso.
 - b. Kukhulupirira ndi mau omwe amachitila, mneni. "Kukhulupirira" mchitanthauzo cha Bukhu Lopatulika ndi "kutenga" kapena "kugwira." Ungathe kukhulupirira mwa Yesu ndi chipulumutso koma osapulumsidwa ngati sunamtenge iye ngati Mpulumutsi - ungate kukhulupirira za machiritso popanda kuchiritsidwa ngati iwe machiritso ako. Kukhulupirira ndi zochitika za chisankho (chifuniro chako)
 - c. Chikhulupiro nthawi zonse chimakhudzana ndi chinthu chakale (chomwe chinapita). Yesu anatipatsa kale zonse zomwe tizifuna kudzera mu kutiombola kwake. Zinthu sizimangokugwera iwe; koma ziyenera kutengedwa (kugwiridwa) mu mzimu.
 4. Chikhulupiro chobwerezabwerezera (cha nthawi zonse) ndi chosiyana ndi "mphatso ya chikhulupiro" kapena kunena kuti "chikhulupiro chapadera." (1 Akorinto 12:9).

B. Okhulupirira onse ali ndi chikhulupiro.

1. Ndife okhulupirira. Tili ndi chikhulupiro kapena sitipulumutsidwa (2 Akorinto 4:13; Aefeso 2:8,9).
 - a. Tabadwa mwa Mulungu ndiponso talandira zochitika zake. Chimodzi mwa izo ndi chikhulupiro.
 - 1) kutsogolera ndi chitsanzo chooneka: sityenera kupempha manja kwa adotolo pamene tili ndi zaka zinayi (5) zakubadwa; timabadwa nawo pamodzi.
2. Popanda chikhulupiro sikungatheke ku mkondweretsa Mulungu, ndiyeno nchofunika kwambiri (Ahebri 11:6).
 - a. Poti Mulungu amatilamula kuti tikhale ndi chikhulupiro, ayenera kuika m'manja mwathu njira zomwe chikhulupiro chiyenera kupezekera.
 - b. Chikhulupiro chimabwera ndi kumva mau a Mulungu (aroma 10:17)
 - c. Bukhu Lopatulika limatchedwa "Mau a chikhulupiro" (Aroma 10:8).
3. Chikhulupiro ndi cha mu mtima kapena mzimu wa munthu.
 - a. Chikhulupiro chimachokera kwa Mulungu ndipo chimabzalidwa mu mzimu

- mwako pamene ubadwa kachiwiri (Aefeso 2:8).
- b. Tonse tizi ndi muyeso wa chikhulupiriro (Aroma 12:3)
 - c. Chikhulupiriro cha mu mtima sizigwirizana ndi maganizo (Miyambo 3:5)
 - 1) Chikhulupiriro chingathe kugwira ntchito mu mtima mwako ndi chikaiko m'mutu mwako. Ungathe kukhulupirira chinthu pamene usanachimvetse.
 - 2) Umanena bwanji pamene ukhulupirira kapena ngati kuli kugwirizana kwa maganizo: umaonetsa kuchita pamenepo?
4. Chikhulupiriro ndi momwe moyo uyenera kukhalira. "Olungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro" (Aroma 1:17; Agalatiya 3:11; Ahebri 10:38).
 5. Zooneka zosiyanasiyana.
 - a. Nthawi zonse ukhulupirira chinachake - kaya choona kapena chonama. Kukaika ndi kukhulupirira m'mbali yotsutsana nayo.
 - b. Ambiri amakhulupirira kuti zinthu zonse nzotheka ndi Mulungu (Mateyu 19:26; Marko 10:27), koma sakufuna kukhulupirira kuti zinthu zonse nzotheka ndi iye amene akhulupirira (Marko 9:23).
 - c. Anthu akhoza kuganiza kuti pang'ono wasiyana ndi mnzako koma zonse zili bwino. Munthu wobadwa sangathe kumvetsa zinthu za uzimu (1 Akorinto 2:14).

C. Chikhulupiriro chikhazikika pa Mau a Mulungu.

1. Mau a Mulungu ngosalakwa (Yohane 17:17; 2 Timoteo 3:16; 1 Atesalonika 2:13).
 - a. Mau ake ndi choonadi; Mulungu sanganame (Numeri 23:19).
 - b. Ungathe kupereka ulemu ku mau wofanana ngati Yesu ali panopa ndi thupi lake.
 - c. Umanena kuti Mulungu ndi wabodza ngati siukhulupirira mau ake.
2. Chikhulupiriro chimayambika pamene maganizo(chifuniro) a Mulungu adziwika ndiponso Mau ake ndiye chifuniro chake.
 - a. Sungalandire chithandizo popanda mau. Mulungu amayenda pamodzi (mogwirizana) ndi mau ake.
 - b. Tisoweka kudziwa chifuniro cha Mulungu ndi chikondi chake ndinso chisamaliro chake. Yesu anali Mulungu ndi thupi la umunthu; ku dziwa za Yesu ndiko kudziwa za chikhalidwe cha Mulungu
 - c. Pafunika kukonza maganizo ako nthawi zonse kuti kodi ndiwe yani mwa Khristu. Mwa lye, mwandani, ndi zina zotere.
 - d. Ndi kofunikira kwambiri kuwerenga, kuchita changu (kuphunzira) ndi kulingalira m'mau a Mulungu.
 - e. Mukhale m'Mau ake, ndikulandira mayankho ku mapemphero anu (Yohane 15:7).
 - f. Kumvera ndikofunika. Muyenera kudziwa malamulo kuti muthe kuwasunga (1 Yohane 3:22).
3. Malonjezo a mau amalandiridwa ndi chikhulupiriro.

- a. Ndi chikhulupiriro timaika mphamvu ya Mulungu mu ntchito
- b. Kutsogolera ndi chitsanzo: magesi.

D. Mitundu iwiri ya chikhulupiriro.

1. Chikhulupiriro cha m'mutu - Tomasi (Yohane 20:29). Zokhuzana ndi choona chachilengedwe (nzeru, kumwa ndi kuganiza kapena chidziwitso cha thupi).
2. Chikhulupiriro cha mu mtima - Abrahamu (Aroma 4:17-21).
 - a. Chokhazikika pa mau a Mulungu.
 - b. Ukudziwa kuti wabadwa mwatsopano ngakhale suuoneka kutero kapena kumva motero. Sungalongozole momwe chipulumutso chimaonekera kapena kuchimva koma umangokhulupirira kuti uli nacho. Chifukwa chiyani? Bukhu Lopatulika likutiiza choncho (Aroma 10:9-10).
 - c. Kutsogolera ndi chitsanzo: Kodi ukafa udzapita kumwamba? Kodi kumaoneka bwanji? Munayamba mwafikako chikhalire? Kodi ndi kuti? Muli ndi chitsimikizo kuti mukupita kumeneko? Simungapereke zenizeni zokhuzana ndi kumwamba, koma umakhulupirira kuti ndi zoon. Ichi ndichikhulupiriro cha mu mtima.

E. Chikhulupiriro kulimbana ndi chiyembekezo (Ahebri 11:1)

1. Chikondi, chiyembekezo ndi chikhulupiriro zonse ndizofunika ndipo zili ndi malo ake, koma sungachotse china nkuikapo chinzake. Pali chikhulupiriro chachilengedwe cha umumunthu ndi chikhulupiriro cha uzimu chosatheka ndi munthu. Chitsanzo cha chikhulupiriro chachilengedwe: chikhulupiriro choti mpando ukugwira (kukunyamula) iweyo.

II. UMO M'MENE TINGAKULILE MCHIKHULUPIRIRO (2 Atesalonika 1:3)

A. Zonse zili ndi ife.

1. Chikhulupiriro chathu chimakula Mau a Mulungu akamakhala enieni kwa ife (Aroma 10:17)
2. Chikhulupiriro chimakula kuzera ku mwai wapadera womwe umapezeka kuti tichigwiritse ntchito!
 - a. Pazapezeka malo ena olimba. Sikuti nthawi zonse nzophweka.
 - b. Khalani odeka mtima(ndi chipiriro) (Ahebri 10:35-36; Yakobo 1:3,4)
 - 1) Chikhulupiriro pamodzi ndi chipiriro zikagwirira ntchito limodzi zimabereka nthawi zonse (Ahebri 6:12)
 - 2) Chikhulupiriro chikakhala chogwedezekagwedezeka ndi mtima wodekha (chipiriro chimene) womwe chimathandiza chikhulupiriro kuti chikhale choima. Chimapereka chipirirochoteteza mpakana yankho litaululika.
 - 3) Popanda chipiriro, nthawi zambiri chikhulupiriro chingalephere kuima molimba m'mau ndipo sichingakhalitse - chidzalephera.
3. Chikhulupiriro chimakulitsidwa.
 - a. Chikhulupiriro ndi mphamvu ndipo chiyenera kugwiritsidwa ntchito kuti chikule.
 - 1) Kutsogolera ndi chitsanzo: kukulitsa mnofu ndi masewera olimbitsa thupi.

- 2) Kuyamba ndi zinthu zophweka koyamba ndipo mukatero chitani zinthu zolimba.
- b. kutsogolera ndi chitsanzo: ana amaphunzira kuyenda.
- c. kuyamba kuyenda pomwe uli ndi chikhulupiriro chako, osati pamene pali wina wake.
4. Ngati chikhulupiriro chathu chikusonyeza kuti sichikugwira ntchito tiyenera kuyamba kusintha.
 - a. Mulungu sasintha, Yesu samalephera. Ngati sizikuyenda tiyenera kuziyang'anitsitsa tokha.
 - b. Yankho ku pemphero lako limakhuza kwambiri iwe mwini kuposa Mulungu.
 - c. Uyenera kuonetsetsa kuti sunalemphere, ndipo sipazakhala pemphero kapena kulephereka kwa chikhulupiriro m'moyo wako.
 - d. Chikhulupiriro chimagwira ntchito ndi chikondi (Agalatiya 5:6). changwirowo chimataya.
 - 1) Mau otsutsana ndi chikhulupiriro ndi mantha. Chikondi chabwino sichikhala ndi mantha (1 Yohane 4:18).
 - 2) Simuli mwana wa chikhulupiriro wa Mulungu wachikhulupiriro komanso mwana wa chikondi wa Mulungu wachikondi.
 - 3) Chikondi monga chikhulupiriro chingathe kukula. Ndi chipatso cha mzimu.
 - 4) Chikhulupiriro chathu sichingagwire ntchito ngati tiskuyenda mchikondi, m'maganizo, m'mau ndi mzochitika (1 Akorinto 13; Afilipi 2:3-4).
 - 5) Tiyenera kuyenda mukukhululukirana (Marko 11:25). Yesu anazichita. Chikhululukiro ndi kuchita chinthu ngati sichinachitike. Munthu yemwe anakulakwira ayenera kuyankha kwa Ambuye. Muleke Mulungu agwire nao ntchito. Kusakhululuka kuzatchinga m'moyo wanu Mzimu wa Mulungu . Pafunika kuziyeretsa.

III. ADANI A CHIKHULUPIRIRO

Menyani nkondo yabwino ya chikhulupiriro (1 Timoteo 6:12). Pakanakhala kuti palibe adani bwenzi palibe nkondo. Mdierekezi amatigwira ife m'njira(m'malo) zathu zofooka. Izi zimatidziwitsa ife momwe tiyenera kugwira molimbika mollimbika kukulitsa chikhulupiriro chathu.

A. Kukaika (kapena kusakhulupirira) ndi mantha.

1. Mitundu iwiri ya kusakhulupirira.
 - a. Chimodzi chimakhuzana ndi kupanda chidziwitso. Machiritso ake ndi chidziwitso.
 - b. Chimodzi ndi kufuna kusakhulupirira, kukhala wosafuna kulola mau kuti atsogolere moyo wako kapena wosanyengereredwa (kukopedwa). Chitsanzo: Ana a Israeli (Ahebrai 4:11). Machiritso(mankhwala) ake ndi kumvera.
2. M'malo atatu mBukhu Lopatulika tikuona kuti Yesu anadzudzula ophunzira ake chifukwa cha kusakhulupirira. Ngati simunganyengereredwe (kukopedwa) ndiye kuti

ndinu osakhulupirira.

- a. Petro anayamba kumira pamene anasiya kuyang'ana Yesu ndikumayang'ana ku zomwe zimachitika (Mateyu 14:22-32).
 - b. Onaninso Mateyu 17:18 ndi Marko 4:39, 40.
3. Uisalole mzimu wamantha kuti ukulamulire. Uyenera kuthana nawo. Sungapempherere nthawi zonse kuti zochitika zisinthe chifukwa choti sukufuna kuthana ndi mantha (2 Timoteo 1:7). Kutsogolera ndi chitsanzo: mkazi kuopa kuti akanakhala yekha.
4. Umo m'mene tingagonjetsere kukayika ndi kusakhulupirira.
- a. Tilizindikire ndi kuliganizira bwino
 - b. Musalivomereze, musaligonjere.
 - c. Menyani ndi mau ndi pemphero
 - d. Ngati nkofunika, mpezeni mbale kapenamlongo mwa Khristu mwa Yesu (Ambuye).
5. "Wina aliyense" m'Marko 11:23 ndi wofanana ndi "Wina aliyense" mu Yohane 3:16. Kanani kukayika. Osakhulupirira ku zochitika kuposa ku malonjezo a Mulungu.

B. Kupanda (kusowa) chidziwitso. Chikhulupiriro chimabwera pomvetsera mau a Mulungu osati pochipempherera.

C. Mnzeru zokhala wosayenera (2 Akorinto 5:17; Aefeso 2:10).

1. Mulungu sanalenge china chilichonse chatsopano chosayenera.
2. Khulupirirani zomwe Bukhu Lopatulika linena ndipo osayang'ana zolephera zako.
3. Konza maganizo ako. Ndiwe chilungamo cha Mulungu mwa Khristu. Mulungu amationa ife, ana Ake, mwa Iye (2 Akorinto 5:21).
4. Mulungu alibe ana owakonda kwambiri kuposa ena (Machitidwe a Atumwi 10:34).

MZIMU WOYERA

I. MZIMU WOYERA NDI NDANI?

A. Mzimu Woyera ndi Mulungu (Machitidwe a Atumwi 5:3-4; 1 Akorinto 3:16-17).

1. Mzimu Woyera ndi amene Mulungu Mulengi Wathu anamugwiritsa ntchito kulenga dziko lapansi (Genesis 1:1,2; Yobu33:4)
 - a. Nyama zinalengedwa ndi Iye (Masalimo 104:30).
2. Mzimu Woyera ndi amene Mulungu Atate anamugwiritsa ntchito kuti Mariya akhale wa pakati (mimba) pa Ambuye Wathu Yesu Khristu (Mateyu 1:18).
3. Mzimu Woyera anali Woyamba pa Umulungu kuonekera pa dziko (Genesis 1:2).

B. Iye ndi munthu osati mphamvu yokha yongochita zabwino.

1. Moyo uli ndi maganizo anu, mafuno, malingaliro, (nzeru) ndi mamvedwe (kumva).
 - a. Mzimu Woyera ali ndi maganizo (amaganiza) (Aroma 8:27)
 - b. Mzimu Woyera ali ndi mafuno ndi malingaliro (1 Akorinto 12:9-11)
 - c. Mzimu Woyera ali ndi mamvedwe (kumvetsera). Iye angathe kumvetsedwa chisoni (Aefeso 4:30), ndipo Iye amakonda (Aroma 15:30)
 - d. Iye amayenda (Genesis 1:2)/ Iye amalankhula chirichonse achimwa (Yohane 16:13). Iye amasanthula zinthu zakuya za Mulungu (1 Akorinto 2:10).

II. UMULUNGU (ATATE, MWANA NDI MZIMU WOYERA)

Iwo ali ofanana(amodzi) mu ntchito koma ali osiyana mu umunthu. Mulungu m'modzi, anthu atatu, osakhala munthu m'modzi, m'maonekedwe atatu ayi.

A. Umodzi Wao (Deutoronomo 6:4). Mau oti "M'modzi" ndi "achad" (chi hebri) amene akutanthauza okhala Pamodzi kapena Chinthu Chogwirizana, kutsutsana ndi chinthu chapaokha. Mwa chitsanzo: Chipatso chimodzi cha mphesa chofanirizidwa ku mphesa zambiri zokhala (zozungulira) pamodzi.

1. Atate ndi Mzimu Woyera ndi amodzi (Aefeso 4:4-6)
2. Atate ndi Yesu Khristu ndi amodzi (Yohane 10:30)

B. Kusiyana kwao (Mateyu 3:16-17; 28:19; Yohane 14:16; 1 Akorinto 12:4-7)

1. Mulungu Atate ndiye wogwira ntchito. Ambuye Yesu ndiye wotsogolera/woyang'anira. Mzimu Woyera ndiye Woonetsera (wosonyeza).
2. Muluntu Atate ndiye magwero a zonse. Ambuye Yesu ndiye Wopatsa (wopereka) zinthuzo kuchokera kwa Atate. Mzimu Woyera ndiye mphamvu ya magwerowo (ya kupatsako).
3. Mafunso awiri amene amatsimikiza kuti Iwo ali osiyana mu umunthu ndithu:
 - a. Chifukwa chiyani kuti mu Yesaya 63:8-10, Atate ali wotetezera pa Mzimu Woyera mwakuti Iye akufika pokhala mdani wa anthu?
 - b. Chifukwa chiyani kuti Yesu anati, Mwazi Wake udzatha kutsuka Chikumbukiro chonse cha uchimo, koma kuti Mwano wa pa Mzimu Woyera udzakhala

wosakhululukidwa (Mateyu 12:31).?

C. "Tiyeni Tipange Munthu Mchifaniziro Chathu" (Genesis 1:26-27).

1. Mauwa akusonyeza kuchuluka kwao.
2. Akusonyeza Umodzi (mgwirizano) Wao.

III. ZIZINDIKIRO, MAKHALIDWE AKE, NDI ZINTHU ZINA ZOKHUDZANA NDI MZIMU WOYERA.

A. Zizindikiro

1. Mafuta (Masalimo 92:10)
2. Moto (Mateyu 3:11)
3. Mphepo (Machitidwe a Atumwi 2:2-4)
4. Madzi (Yohane 7:37,38)
5. Mvula ndi Mame (Hoseya 6:3)
6. Nkhunda (Mateyu 3:16)

B. Makhalidwe a Mzimu Woyera

1. Iye angathe kukhumudwitsidwa (Aefeso 4:30)
2. Iye angathe kulemekezedwa (1 Petro 4:14)
3. Iye ndi wa chisomo (Ahebri 10:29)
4. Iye ndi wa chilungamo (Yesaya 4:4)
5. Iye ndi wosadzikonda mwa Iye Yekha ndipo ndi Wofatsa (Yohane 16:13-15)
6. Iye amatsutsa ochimwa za tchimo (Yohane 16:8)
7. Iye ndi amene amadzodza inu kuti muuze dziko lapansi za tchimo lake (Mika 3:8)
8. Iye ndi wamphamvu (Yesaya 11:2)
9. Iye ndi Mzimu Wa Ufulu ndi wofuna (wakulola) (Masalimo 51:12). Umamfunsa Iye kuti akuthandize, ndipo Amati, "Ndidzachita!" Kumufunsa kuti akuchiritse, Iye amati, "Ndidzachita."

C. Zoona zake za Mzimu Woyera

1. Sungathe kudza kwa Atate popanda Mzimu Woyera (aefeso 2:18)
2. Sungakhale wa chikondi choona popanda Mzimu Woyera (Aroma 5:5)
3. Sungapembedze Mulungu popanda Mzimu Woyera (Yohane 4:23)
4. Sungapemphere mu Mzimu popanda Mzimu Woyera (Yuda 20)
5. Sungamvere Mulungu popanda Mzimu Woyera (1 Petro 1:2)
6. Iye amafuna kukudziwani inu ndi kuyanjana nanu (Afilipi 2:1)
7. Iye ndiye chokole chathu chi chiomboledwe chathu cha Moyo Wosatha (Aefeso 1:13,14)
8. Iye amakuphunzitsani ndi kukutsogolerani (Yohane 16:13)

IV. MZIMU WOYERA M'KUBADWA MWATSOPANO NDI UBATIZO WA MZIMU WOYERA

A. Zidziwitso (zochitika) ziwiri zosiyana: China chikutchulidwa ngati chitsime cha Madzi (Yohane 4:13-14), chinacho ngati Mtsinje (Yohane 7:38).

B. Mpingo Woyamba ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

1. Iwo anali obadwa mwatsopano asadalandire (kudzadzidwa) ndi Mzimu Woyera (Yohane 20:22; Machitidwe a Atumwi 1:4-8, 2:4)
2. Kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera kumafika munthu atatha kubadwa mwatsopano (Machitidwe a Atumwi 8: 15-17)
 - a. Zomwe zinamchitikira Paulo
(Machitidwe a Atumwi 9:1-6, 9:10-12,17: 1 Akorinto 14:18)
 - b. Mpingo wa ku Efeso (Machitidwe a Atumwi 19:1-2)
3. Umboni wa Bukhu Lopatulika wa kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndiwo kulankhula M'malilime, anamva chiyani? - Malilime (Machitidwe 2:4,33).
 - a. Asamariya (Machitidwe a Atumwi 8:18-19)
 - b. Paulo analankhula ndi malilime atatha kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera (1 Akorinto 14:18).
 - c. Amitundu (Machitidwe 10:44-48)
 - d. Mpingo wa ku Efeso (Machitidwe a Atumwi 19:6)

C. Ziphunzitso ZOLAKWIKWA pa Ubatizo wa Mzimu Woyera (Onani: Malembo otsatirawa agwiritsidwa ntchito molakwika kutsimikizira ziphunzitso izi).

1. Muyenera kukhala kapena kudikira Mzimu Woyera (Luka 24:49; Machitidwe 1:4).
2. Muyenera kupempha Mulungu, kufuula, kugwedezeka, ndi kukuwa(kulira) (mwambo wa anthu).
3. Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi umboni wa kulankhula m'malilime ena zinapita ndi Atumwi.
4. Mulungu Yekha amadziwa (amalingalira) ndi ndani adzalandira Mzimu Woyera (1 Akorinto 12:30)
5. Malilime anatha (analeka) (1 Akorinto 13:8-12)

D. Chiphunzitso cholondola pa ubatizo wa Mzimu Woyera:

1. Mzimu Woyera wafika kale (waperekedwa kale)
2. Muyenera kumulandira lye
3. Atumwi anawapempherera iwo kuti alandire Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 8:14-15).

V. CHIYANJANO CHA MZIMU WOYERA (Zakariya 4:6; 2 Akorinto 13:14)

A. Kulandira Mzimu Woyera ndi kulandira Munthu Woyera. Iye amabwera kudzakhala ndi kupanga nyumba Yake m'matupi athu (1 Akorinto 3:16-17; 2 Akorinto 6:16).

1. Iye amatchedwa "Mzimu Wa Choonadi" kutanthauza kuti adzakutsogolerani, kukuphunzitsani, ndi kukulondolani (Yohane 14:16-18, 26; 15:26-27; 16:7-15;

1 Yohane 4:6).

2. Wokhulupirira aliyense wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera ali nao mkati mwake, kukonzera kugwiritsa ntchito, mphamvu zonse zopoza zomwe angazisowe kuwaika m'moyo wapamwamba m'moyo uno (Aroma 8:31; 1 Yohane 4:4)
3. Mautumiki asanu ndi awiri a Mzimu Woyera kwa inu (Yohane 14:16, AMPLIFIED BIBLE)
 - a. Nkhoswe
 - b. Mlangizi
 - c. Wopatsa mphamvu
 - d. Wopembedzera
 - e. Wothandizira
 - f. Woimirira pambali pathu (wosungiridwa)
 - g. Mthandizi
4. Chinthu chofunikira pa kuyenda mu Mzimu ndicho kukhala wozindikira nthawi iri yonse za kukhala (kupezeka) kwa Mzimu Woyera mwa iwe.

B. Kufunikira ndi madalitso akulankhula m'malilime (1 Akorinto 14:2,4,18, 39; Yuda v.20).

1. Ndi njira yolowera mu zakuya (zozama) za Mzimu.
2. Mau a Mulungu amabwera a moyo (Yohane 16:13)
3. Moyo wanu wa pemphero umalemera (umakula) (Yuda v. 20-21)
4. Kudzakutengerani vumbulutso la mphamvu la Yesu (Yohane 16:14)
5. Kudzakupatsani umboni (chitsimikizo) wamphamvu (Aroma 8:16)
6. Munthu umalowa mu chidzalo cha chikondi cha Mulungu (Aroma 5:5)
7. Munthu umapeza (kukurukira) chimwemwe chachikulu cha Mzimu Woyera (Aroma 14:17)
8. Munthu umakhala wopindula mu ntchito yako mthupi la Khristu.

MAU OYAMBIRIRA AKU UTUMIKI

MAU OYAMBA: Mulungu wapereka mphatso ku mpingo, Thupi la Khristu, kukachita mopindula ntchito yakumanga Ufumu wa Mulungu pano pa dziko lapansi. Tidzaphunzira mitundu yosiyanasiyana ya mphatso ndi m'mene tingayenerere mthupi ndi chomwe tingathe kuchita ndi mphatso zathu. Anthu ambiri a mu mpingo, ngakhale atumiki omwe, samadziwa kuti ndi mphatso zANJI ndipo ndi mphamvu zANJI zomwe Mulungu wapereka kwa iwo kapena ndi malo ati omwe iwo ali oyenera Mthupi la Khristu. Ichi chimapangitsa ambiri kusakhala opindula kapena obereka zipatso pa ufumu wa Mulungu.

I. MITUNDU ITATU YA MPHATSO

A. Mphatso za utumiki (Aefeso 4:11-12).

1. Mtumwi
2. Mneneri
3. Mlaliki
4. Mbusa
5. Mphunzitsi

B. Mphatso za zokopa (Aroma 12:6-8).

1. Kunenera
2. Kutumikira
3. Kuphunzitsa
4. Kudandaulira
5. Kugawira/kupatsa
6. Kuweruza (kukhazikitsa)
7. Chifundo

C. Mphatso a uzimu (1 Akorinto 12)

1. Mphatso zitatu zakulankhula; malilime, kunenera, ndi mamasulidwe a malilime.
2. Mphatso zitatu za makhalidwe amphamvu: kuchita zozizwa, chikhulupiriro chapadera ndi machiritso.
3. Mphatso zitatu za mavumbulutso: mau a chidziwitso, mau a mnzeru ndi kuzindikira cha mizimu.

D. Nthawi zambiri, mphatso zokopa(zothandizira) ndiye makwerero aku mphatso zamautumiki asanu aja (Machitidwe 6:1-6)

1. Mphatso ndi chiyani?
2. Kodi mphatso ingatheke kulandiridwa monga malipiriro?
3. Mphatso zokopa ndi za utumiki. Zimagwirira ntchito pamodzi motani? (Aefeso 4:11-12).

II. MPHATSO ZA UTUMIKI

Mphatso za utumiki ndi zosiyana koposa ndi mphatso zisanu ndi zinai za Mzimu. Pali mphatso za utumiki zisanu zopatsidwa ku mpingo, ndi cholinga cha zakuumangirira ndi kuufikitsa ku ukulu. timapeza madziko aizi m'bukhu la 1 Akorinto 4:15. Mu bukhu lomweli yonse Paulo akufotokoza ku mpingo wa ku Korinto kuti ife, monga atumiki a Khristu, ndife ochita a utumiki wa Khristu. Pali mpingo wa padziko lonse (wopezeka paliponse) wokhala ndi wina aliyense yemwe wavomereza Ambuye Yesu Khristu ngati mpulumutsi. Ambuye Yesu ndiwo omwe amapereka ku mpingo (Aefeso 4:8-12). Yesu ndiye mutu wa Mpingo. Chimodzi cha zinthu zokondweretsa koposa mu utumiki wa Yesu Khristu ndi choti muli zosiyanasiyana (kusiyanasiyana).

- A. MTUMWI amaoneka ngati akufungatira (kukhala nawo) mautumiki onse.**
- B. MNENERI ndi wouzira kapena kuti wouziridwa. Iye amalankhula mwa mphamvu ya Mzimu Woyera ndi vumbulutso.**
- C. MLALIKI ali ndi chitsogozo cha Ambuye ku kalalila Uthenga Wabwino.**
- D. MBUSA ndi utumiki umodzi woperekedwa ku mpingo kuti utsogolere nkhusa za Mulungu; mautumiki ena anaiwa amaperekedwa kukalangiza mpingo.**
- E. MPHUNZITSI ndi m'modzi amene saphunzitsa ndi mphamvu za chilengedwe koma ndi mphamvu za Mzimu kapena kuti mphamvu ya Umulungu.**

Pali njira ya kukumbukira mphatso zisanu za utumiki pogwiritsa ntchito zala za dzanja lako. Chala chachiwiri (cholodzera) ndi mneneri; chala chapakati ndi Mlaliki; chala chachinai ndi Mbusa; chala chaching'ono ndi Mphunzitsi; ndipo chala chachikulu ndi mtumwi.

III. MTUMWI

Mtumwi ndiye mutu wa mphatso za utumiki, monga tionera pa 1 Akorinto 12:28. Utumiki woyambirira wa Mtumwi womwe unakhalapo unali wa Ambuye Yesu Khristu (Ahebri 3:1). Mau a chi Helene a Mtumwi amanthauza "kutumidwa" kapena "wotumizidwa," ndipo Yesu ndiye chitsanzo chachikulu cha munthu wotumizidwa (Yohane 20:21). Utumiki wa mtumwi uyenera kutsatana ndi zizindikiro zopezeka pa 2 Akorinto 12:12. Munthu yemwe amakhala mu utumiki umeneu amakhala woyamba, osati wotsatira (wachiwiri). Mtumwi ndiye wotumizidwa, wosakhala munthu wongopita kwina kwake ayi. Iye amakhala ndi mphamvu. Pa Machitidwe a Atumwi 13, Paulo ndi Banaba anapatsidwa mphamvu yoti apite.

A. Zizindikiro za Mtumwi (2 Akorinto 12:12).

1. Zizindikiro ndi zoziwa ndi machitidwe a mphamvu.
2. Chidziwitso chozama (chakuya) ndi choonadi cha munthu ndi Ambuye (2 Akorinto 9:1).
 - a. Paulo adaona Ambuye.
 - b. Vumbulutso la Iye (Ambuye) linapatsidwa (1 Akorinto 11:23; Agalatiya 1:11-12).
3. Ntchito ya Mtumwi - Woika madziko (1 Akorinto 3:10; Aefeso 2:20)
 - a. Utumiki wa Mtumwi umaoneka wofukata mphatso zonse za utumiki. Zotsatira zoonekeratu ndizo kukkhazikitsa mipingo.
 - 1) Iye amakhala ndi mphatso ya uzimu (umulungu) yotchedwa "maweruziro" (Mphamvu za kukonza) zolembedwa pa 1 Akorinto 12:28.

- 2) Iye amakhala ndi ulamuliro m'mipingo yokhayo yomwe iye wakhazikitsa.
- b. Wotumidwa amene waitanidwadi ndi Mulungu ndi kutumizidwa ndi Mzimu Woyera ndiye Mtumwi (Machitidwe a atumwi 13:2-4).
4. Mtumwi adzakhala ndi mphamvu za mphatso za mautumiki onse.
 - a. Iye adzachita ntchito ya mlaliki.
 - b. Iye adzaphunzitsa ndi kuwakhazikitsa anthu.
 - c. Iye adzachita ntchito ya mbusa
 - d. Chitsanzo chatu ndiye Mtumwi Paulo.

B. Kodi alipo atumwi lero lino?

1. Osakhala monga momwe analiri atumwi khumi ndi awiri oyamba.
2. Chipangano Chatsopano chikulankhula za ena ambiri: Barnaba ndi Saulo (Machitidwe a Atumwi 14:14), mbale wake wa Yesu, Yakobo (Agalatiya 1:19), Androniko ndi Yuniya (Aroma 16:7) Silvano ndi Timoteyo (1 Atesalonika 2:6), Apolo (1 Akorinto 4:4-9), ndi Epafrodito (Afilipo 2:25). Mau oti "Msilikali" mu ndime izi akutanthauza "Mtumwi!"

C. Zizindikiro (zitsonyezo) za Mtumwi lero lino:

1. Amakhala ndi mphatso za uzimu
2. Amakhala ndi chidziwitso chakuya mu umunthu wake ndi Ambuye.
3. Mphamvu ndi ulamuliro waku khazikitsa mipingo.
4. Wokhonza kugawira utsogoleri wabwino wa uzimu.

IV. MNENERI

1. 1 Akorinto 12:28 akunena kuti "achiwiri aneneri", mu Aefeso akutchula aneneri. Utumiki wa Mneneri suyenera kulemekezedwa koposa utumiki wina uliwonse. Tili nao aneneri mpaka lero lino.

A. Ndi chiyani chimapatsa/kupangitsa/ mphamvu mneneri?

1. Chisonyezo chofanana (chogwirizana) chokhala nawo pafupifupi mphatso za mavumbulutso ziwiri (mau a chidziwitso, mau a nzeru, chizindikiro cha mizimu), kuonjezapo uneneri.
2. Amakhala ndi masomphenya ndinso mavumbulutso.

B. Kusiyana pakati pa mneneri wa Chipangano Chakale ndi mneneri wa chipangano chatsopano.

1. Anthu a m'Chipangano Chakale ankapita kwa mneneri kukafuna chitsogolero (utsogoleri).
2. Okhulupirira a Chipangano Chatsopano amatsogoleredwa ndi Mzimu Woyera.
3. Mneneri weniweni amaika mau a Mulungu patsogolo.

C. Kudzindikira kusiyana kwa pakati pa Mzimu wa Mulungu ndi mizimu wamba(mizimu yobwebweta)

1. Chifukwa kuti ndi chinthu cha uzimu sichisonyeza kuti uli Mzimu wa Mulungu (2 Akorinto 11:14).
2. Kodi umakweza munthu kapena Yesu?

D. Kusokonekeka maganizo kwa anthu komwe alinako po khuzana ndi utumiki wa Mneneri.

1. Anthu ambiri amaganiza kuti chilichonse chimene mneneri achita ndi kunenera.
 - a. Mneneri amachita zambiri koposa mavumbulutso.
 - b. Utumiki wa machiritso ndi kuika kwa manja zimayenda limodzi ndi utumiki wa mneneri.
2. Mneneri samadziwa chilichonse cha munthu aliyense, ngakhale chilichonse chimene chikuchitika pomwe iye ali.

V. MLALIKI

Mlaliki ndi munthu amene angathe kutengera miyoyo yambiri kwa Yesu Khristu. Mlaliki amapita ku malo ambiri kulalikira. Chitsanzo chabwino cha mBaibulo cha mlaliki ndi Filipo.

A. Kuitana (Maitanidwe).

1. Mulungu ndiye wokhazikitsa, osakhala munthu ayi.
2. Mulungu ndiye woitana, osakhala munthu ayi.
3. Mulungu ndiye wochita (womuzaza), simunthu ayi.
4. Kukopa ndi cholinga cha kuitana.

B. Mpatso ya utumiki ya Mlaliki.

1. Mau oti "Mlaliki" amaoneka katatu kokha mChipangano chatsopano. amatanthauza munthu amene amatenga Uthenga Wabwino, mtumiki wa Uthenga wa Chisangalero (Machitidwe a Atumwi 21:8; Aefeso 4:11; 2 Timoteo 4:5).
2. Mfundo (uthenga) yopambana ya mlaliki ndiyo Chipulumutso.
3. Chitsanzo chokhacho cha mChipangano Chatsopano cha mlaliki chomwe tili nacho ndiye Filipo
 - a. Amalalikira Khristu (Machitidwe a Atumwi 8:5, 35).
 - b. Zozizwa ndi machiritso zimatsatira (Machitidwe a Atumwi 5:5-8).
4. Kusiyana pakati pa Mlaliki ndi wodandaulira

C. Zizindikiro za kulalikira koona.

1. Kulalikira (kulengeza) mwa Mzimu (muuzimu).
2. Ayenera kulalikira Mau. Mphamvu ya Mulungu idzakoka gulu la wanthu. Zozizwa ndi Machiritso zimagwera (kukopa) anthu. Mwina mulimonse, ndi kukhulupirira kwa mau kumene kumapangitsa anthu kupulumuka (Machitidwe a Atumwi 8:6-8).

VI. MBUSA

Utumiki wa mbusa ndiwo kudyetsa nkhusa, kuzisamalira, ndikuzipatsa msipu. Pali

www.livingwordmissions.org

uindo waukulu pa mbusa mukudyetsa nkhusa za Ambuye ndi kukonza upo(gulu) la akulu (madikoni) kuti amuthandize mbusa ndikuthandizanso kutumikira ena. Pa Yakobo 5, sanaitana mbusa kuzadzoza wodwala, koma akulu ampingo: Akulu a mpingo amathandizira kuyang'anira anthu mu uzimu. Oyang'anira (madikoni) amasamalira zosowa za thupi za mpingo ndi za mbusa. Kumbukurani, ntchito ya mbusa ndiyo kudyetsa nkhusa. Njira yokhayo imene mbusa angathe kuchitira ntchitoyi ndikuphunzitsa akulu pamodzi ndi oyang'anira (madikoni) kuti amuthandize iye.

Kuthandizira kwa akulu ndi oyang'anira kumathandiza mbusa kukonzekera kwabwino pokhala ndi nthawi ndi Ambuye kukonzekera kukadyetsa gulu lake la nkhusa ndi chakudya chabwino cha Mau a Mulungu. Lingirirani pa Ezekieli 34:1-10 ndi Yeremiya 23:1-2) ngati mwaitanidwa monga mbusa. Ambuye akuyang'ana pa azibusa onse lero lino, ndipo mbusa wina aliyense adzaimirira pamaso pa Ambuye tsiku likna.

VII.MPHUNZITSI

Utumiki wa Mphunzitsi walembedwa m'malo atatu: Aefeso 4:11, 1 Akorinto 12:28-28, ndi Aroma 12:4-11. Utumiki wa mphunzitsi walongotsoledwa bwino mChipangano Chatsopano. Mphatso ya kuphunzitsa ingathenso kupezeka m'mautumiki a mbusa, mneneri ndi mlaliki. Munthu angathe kukhala mu utumiki wa mphunzitsi ndikukhalanso mbusa. Munthu angathe kukhala mneneri kapena mlaliki ndikukhalanso mphunzitsi . Komano munthu angathe kukhala mphunzitsi osakhala mbusa. Munthu uyu amayendayenda kukaphunzitsa, komanso amakhala ndi mbusa ndi mpingo kumene iye amachokera, Mkhristu aliyense angathe kuphunzitsa Baibulo kapena kugawana ndi wina chomwe adziwa; uwu umatchedwa utumiki wa Chiyanjitso (2 Arokinto 5:18). Ichi sichipangitsa munthu wotere kukhala mphunzitsi. Amene akuchita mu utumiki wa mphunzitsi amaphunzitsa mau a Mulungu ndi mphatso ya uzimu ya Mulungu.

Sangokhala munthu wokhala ndi mphamvu yachibadwidwe kapena zofuna za iye yekha za chibadwidwe kukuphunzitsa. Mphamvu ndi zofunazo zitha kukhala zothandiza, koma mphatso sizili chinthu chachibadwidwe koma cha uzimu.

VIII.UTUMIKI WA MATHANDIZO

Pakati penipeni pamene palembedwa mphatso za mautumiki mu 1 Akorinto, tipezapo utumiki wa mathandizo. Maitanidwe anu atha kukhala ku utumiki wa mathandizo (ndime 28).

A. Mau oti "Mathandizo" mu chi Helene amatanthauza "Mthandizi kapena wochepetsa mavuto."

1. Mwa umboni, mau amenewa ali ndi ganizo losiyana ndi mautumiki ena onse omwe atchulidwa. Mauwa akanafotokozedwa bwino koposa monga mofanana ndi mtundu wa utumiki wodziwikiratu wotchedwa oyang'anira (madikoni).
 - a. Mauwa agwiritsidwa ntchito pa Afilipi 1:1 ndi 1 Timoteo 3.
 - b. Agwiritsidwa ntchito pa Febe mbukhu la Aroma16:1 ndipo atanthauziridwa "kapolo/wotumikira"
 - c. Utumiki wa oyang'anira m'masiku oyamba a mpingo unalumikizika mwapadera ndi ulamuliro wa mpingo pa za chuma ndi kukhalanso oyang'anira a anthu osauka ndi odwala.

- d. Iyi ndi mphatso ya Mulungu kuchokera ku Mutu wa Mpingo. Chinthu china choposa kungokhala mphamvu ya ntchito ya chibadwidwe ndi chofunika.
2. Oyang'anira (madikoni) asanu ndi awiri oyamba (Machitidwe 6:1-6).
3. Oyang'anira ena mu mpingo oyamba (Aroma 16:3-6).
4. Utumiki woyimba - Pali kusiyana pakati pa "kutumikira" mu nyimbo ndi kungoimba wamba.
5. Mzimu Woyera ali mu utumiki wa mathandizo . Onani Yohane 14:16 (Mkhoswe - Wothandizira)
6. Akazi ali mu utumiki wa mathandizo. Onani Genesis 2:18 pamene akulongotsoledwa ngati wothandizana naye kwa mwamuna wake.

B. Zoyenera oyang'anira (1 Timoteo 3).

IX. KUTSILIZA/KUMANGIRIRA

Musatengedwe nao maina ndi maudindo. Ngati simudziwa chomwe Mulungu wakuitanirani kuti muchite, musayerekeze(musavutike) mpang'ono pomwe za ichi. Ngati mukumva za maitanidwe mkati mwanu, ingolalikirani ndi kuphunzitsa, kenako dikirani Mulungu potsatira pake akukhazikitseni mu utumiki kapena m'malo omwe lye ali nao pa inu. Mulungu amathokoza kukhulupirika, osati maudindo ayi. Mwa chitsanzo, munthu sukhala mlaliki chifukwa choti umazitcha iwe wekha kukhala mlaliki.

KUMVERA

I. MAU OTSOGOLERA A KUMVERA

A. Kodi ndi chiyani, kapena sichili?

1. Kumvera ndi zomwe zimachitika m'moyo wa munthu wokhulupirira mwaufulu kukhala tcheru ndi cholinga chotsunga ndikuchita zomwe Mulungu alamula.
 - a. kupuma ndi kuchoka kuzofuna zathu; kukhala ophunzitsika ndi ofewa (Agalatiya 6:3).
 - b. kumvera ndikuchita zinthu ndi chikhalidwe. Izi zimachokera mu mtima.
 - c. kumvera kopanda kuzipereka ndi ukapolo.
2. Kumvera sichinthu chophweka chimene chinangofunsidwa kwa wokhulupirira kumeneku ndikulamulidwa.
 - a. Zimenezi sizichita miyambo zazosema, zopeka ndizopereka. (Agalatiya 4:9-10).
 - b. Sichinthu chomwe timachita kuti tilandire mphoto.
 - c. Sichinthu chomwe timachita kulewa za pansu pa mtima wathu (chikumbu mtima choipa).
3. Kumvera ndi yankho ku chikumbu mtima cha bwino ndi choyera (1 Timoteo 3:9; 2 timoteo 1:3; Ahebri 13:18; 1 Petro 3:16)
4. Chitsanzo cha Sauli (1 Samueli 10:8, 13:1-10, 15:3-23).
 - a. Vuto la Saulo linali pa zizolowezi lopereka zopsereza ndi kupereka nsembe.
 - b. Mulungu amafuna kumvera kuposa nsembe.
 - c. Mulungu amakondwera mwa anthu omwe atsatira malangizo monga momwe iye alamulira.
 - d. Mulungu amafuna kumvera kwenikweni, osati kumvera pang'ono. Kunena zoonapalibe chinthu monga kumvera pang'ono.

B. Chikondi cha kumvera, ndi mapeto ake. (Masalimo 119:97-105, 129-139, 165-174).

1. Chikondi cha kumvera chimachititsa munthu kusinkhasinkha (kulingalira) za Mau a Mulungu. Muwasunga. (Yosha 1:8)
2. (Masalimo 119:97-100).
3. Adzakuteteza iwe ku tchimo (Masalimo 119:9, 101-104)
4. Adzakupatsa ine njira ndi chitsogozo (Masalimo 11:105; 119:105)
5. Adzakupatsa iwe mtendere waukulu (Masalimo 119:165).

II. KUMVERA: MPHAMVU IMODZI YOKHA YA KU MPALADIZO (Genesis 2:16-17; 3:11)

A. Paladizo, kalivare ndi kumwamba zimanena zonse pamodzi ndi liu limodzi

"kumvera ndi chinthu choyamba ndi chotsirizira chomwe Mulungu afuna kwa iwe" . (Aroma 5:19; Afilipi 2:8-9; Ahebri 5:8-9; Chibvumbulutso 22:14).

B. Amuna a mChipangano Chakale omvera.

1. Noah (Genesis 6:22, 7:5)
2. Abrahamu (Genesis 22:16-18; Ahebri 11:7).
3. Mose (Eksodo 19:5)

C. Amuna a mChipangano Chatsopano omvera

1. Kumvera kwa Khristu (Yohane 10:18; Aroma 5:19; Ahebri 10:9)
 - a. Mwa Khristu kumveraku linali lamulo la moyo (Yohane 6:38).
 - b. Mwa Khristu kumveraku chinali chimwemwe.
 - c. Mwa Khristu kumvera kumeneku kumatsogolera lye kuyembekezera ku chifuniro chake cha Mulungu (Masalimo 40:6-8)
 - d. Mwa Khristu kumvera kumeneku kunali kofikira imfa (Yohane 6:38).
 - e. Mwa Khristu kumvera kumeneku kumatumphuka kudzera mkuzichepetsa kwakukulu (Afilipi 2:5-8).
 - f. Mwa Khristu kumvera kumeneku kunali kwa chikhulupiriro, mukudalira kwenikweni mu mphamvu zake za Mulungu (Yohane 5:30).
2. Petro (Machitidwe a Atumwi 5:32; 1 Petro 1:2, 14-15, 22).
3. Paulo (Aroma 1:5, 16:26).
4. Zomwe Yakobo ananena zokhuzana ndi kumvera (1 Yohane 2:3,4, 3:18-22, 5:3).

D. Kusamvera kudzaletsa madalitso a Mulungu kwa inu.

1. Chikondi ndi kukhululukira (Mateyu 5:44; Marko 11:25; Yohane 13:34).
2. Mau ndi pemphero (Yoswa 1:8; Yohane 15:7).
3. Umboni - uzani anzanu za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu (Marko 16:15).
4. Kupita kutchalitchi (Ahebri 10:25).
5. Kuthokoza ndi kulemekeza (Afilipi 4:6).
 - a. kudandaula sikuthokoza ndi kulemekeza (Afilipi 4:6)
 - b. kung'ung'uza ndi kudandaula sikuthokoza ndi kulemekeza
 - c. ku kwiya sikuthokoza ndi kulemekeza
 - d. kukhumudwa sikuthokoza ndi kulemekeza ayi.
6. Chikhulupiriro chimagwira ntchito ndi chikondi (Agalatiya 5:6). Chikondi sichingagwire ntchito popanda kumvera. Pamene ukonda Mulungu ndi kumvera mau a Mulungu mosachotsera, palibe chinthu china chimene chingathe kuima munjira yako ndikuletsa chikhulupiriro chako.
7. Chitsanzo cha Kaini ndi Abele (Genesis 4:1-7)

III. KUPHUNZIRA CHINSINSI CHA KUMVERA KWENIKWENI (Ahebri 5:8,9)

A. kumvera kumaphunziridwa.

B. Maphunziro (sukulu) akumvera.

1. Mphunzitsi ndi Khristu ndi chitsanzo chake (Yohane 12:49-50)
2. Bukhu lophunzirira ndi Bukhu Lopatulika (Mateyu 4:4,7,10, Luka 24:27). Yesu anali munthu wotsatira mau, koma mau popanda Mzimu siangakhale ndi mphamvu pa ntchito za kumvera.

C. Mwana wa sukulu - Iwe!

1. Ayenera kuzipereka mtima wonse kwa mphunzitsi.
2. Ayenera kumkhulupirira mphunzitsi. Ayenera kupereka kumvetsera kwake konse kwa mphunzitsi ku zomwe afunsa.

PEMPHERO

I. KUFUNIKA KWA PEMPHERO

II. ZIMENE PEMPHERO SILIRI (Mateyu 6:5-8)

A. Pemphero si mchitidwe wopanda phindu, kutaya mtima kapena kusakhulupirira.

1. Kutaya mtima kwa ubongo kumati, "Mwina mwake pali mpata woti pemphero langa limvekera kumwamba kudzera mu kamng'ambira mpaka ku mpando wa Mulungu, kapena pemphero langa limumenya mbali yabwino imodzi ya Mulungu tsiku lina."
2. Ngati upemphera motaya mtima, uyenera kuleka ndi kulapa, tsono ungoyamba kutamanda Mulungu. Izi zithandiza moyo wako wa pemphero pamodzi ndi chikhalidwe chako.

B. Kupemphera sichinthu chomwe uchita kuti usangalatse anthu kapena Mulungu (Mateyu 6:5; Luka 18:10-14).

C. Pemphero sikupenda ganizo lina lirilonse polapa "mumbo - jumbo" (Mateyu 6:7)

III. Chimene pemphero liri

A. Pemphero ndi kupempha (Mateyu 7:7-8).

B. Pemphero ndi kulankhula mau a Mulungu kubwereranso kwa lye, kumukumbutsa za mauwo icho (Yesaya 43:26).

C. Pemphero nkusatopa, "osanena kuti ndife" popempha/Aefeso 6:12-18).

D. Pemphero ndi kucheza ndi Ambuye, monga kuthokoza/kutamanda ndi ku pembedza.

IV. ZOMWE YESU ANANENA ZA PEMPHERO

A. M'Mateyu (5:44,6:5-16,7:7-11, 9:38,18:19,21:18-22, 26:40-41).

B. M'Marko (11:19-26)

C. Mu Luka (10:2,11:1-13, 18:1-8)

D. Mu Yohane (14:10-14,15:7-8, 16:23).

V. ZIMENE PAULO ANANENA ZA PEMPHERO

A. Mu Aroma (8:26,10:1)

B. Mu 1 Akorinto (14:2,13-14)

C. Mu Aefeso (6:18-20)

D. Mu Afilipi (4:6-8)

E. Mu 1 Atesalonika (5:16-18, 23,25)

F. Mu 1 Timoteo 2:1-8, 4:5

VI. ENA ANENA ZOTANI PEMPHERO

A. Yohane 5:14-15

B. Yakobo 5:13-18

C. 1 Petro 3:7 ndi 12,4:7,5:7

D. Yuda 20

VII. MAPEMPHERO MCHIPANGANO CHATSOPANO

A. Aroma 1:8-10.

B. 1 Akorinto 1:4-5.

C. 2 Akorinto 13:7.

- D. Aefeso 1:16-23, 3:14-21.**
- E. Afilipi 1:3, 9-11.**
- F. Akolose 1:9-12, 4:3-4.**
- G. Atesalonika 1:11-12, 3:1-2..**
- H. Filimoni 4**
- I. Yohane 2**

CHILUNGAMO

I. CHIFUKWA CHOMWE MPINGO WALEPHERERA

Mpingo walephera chifukwa chosowa kumvetsetsa za chilungamo.

A. Kutsutsika m'malo mwa chilungamo ndi zomwe zakhala zikulalikiridwa.

1. Anthu akachititsidwa kuti azimva za chilungamo ngati kuti chimalandiridwa monga malipiro (Aroma 3:21-22)
2. Anthu akachititsidwa kuti azikhulupirira zoti kuwomboledwa ndi chipulumutso chathu sitingathe kuzilandira mpaka tsiku la imfa (Yohane 5:13).

B. Chikumbumtima cha uchimo ndicho chotsatira chake.

1. Tanthauzo la chikumbumtima cha uchimo:- Kuziona mu uchimo nthawi zonse, mantha, ndi kusayenera chifukwa cha uchimo.
2. Umakhala wodziwa kwambiri za chibadwidwe kuposa za Mulungu - za uzimu.
 - a. Zizindikiro ziwiri za chikumbu mtima cha uchimo.
 - b. Umataya chikumbumtima cha Mulungu ndi kukhala nacho chikumbumtima cha iwe mwini.

C. Kutanthauzira chilungamo moyenera (2 Akorinto 5:21).

1. Matanthauzo:-
 - a. Mphamvu zoima nazo pamaso pa Mulungu Atate popanda kudzionika ndi kulakwa kapena kudziyoza wekha.
 - b. Kulungamitsidwa - "ngati sindinachimwepo mkale lonse"; kutchulidwa wolungama; kulengeza kwa anthu kukhala a ufulu ku uchimo ndiponso kukhala ovomerezeka kwa Mulungu.
 - c. Chilungamo ndi chomwe timapangidwa, osati timakhala (2 Akorinto 5: 21).
 - d. Chilungamo si chinthu; koma ndi malo oimapo
 - e. Chilungamo chimalandiridwa ndi chikhulupiriro (Aroma 3:22, 5:1).
 - f. Chilungamo ndi mphatso yaulere (Aroma 3:24, 5:14-17).

D. M'mene ungakhalire chilungamo (Aroma 10:10)

II. KUBWEZERETSEDWA KWA CHILUNGAMO

Yesu, Adamu wotsiriza, anabwezera kwa ife zomwe Adamu woyambayo anataya.

A. Zotsatira za chilungamo cha Adamu - asanachimwe (Genesis 1:3-28, 2:15)

1. anali pa ubale wabwino ndi Mulungu.
2. Anali ndi ulamuliro ku zinthu zonse.
3. anali kukwaniritsidwa pa zosoweka zake zonse zomwe anali nazo.
4. Anamva liu la Mulungu ndipo anali pa ubwenzi (chiyanjano) ndi Mulungu.
5. Analibe maganizo odzinyozetsa kapena cholakwa.

6. Sanadziwe kuopa(mantha) kapena kulephera.
7. Iye anadziwa mtendere.
8. Anali ndi chikhulupiriro (chitsimikizo) ndi ulamuliro.

B. Zotsatira za uchimo wa Adamu - atagwa mchinyengo (Genesis 3:6-15).

1. Ubwenzi wake ndi Mulungu unatha.
2. Ulamuliro wake unatha.
3. Anayamba kudziwa kuopa, kulakwa ndi kulephera.
4. Tchimo ndi kudwala(matenda) kunayamba kulamulira.
5. Satana anasanduka Mulungu wa dziko lino (2 Akorinto 4:4).
6. Tchimo linafikira kwa anthu onse (Aroma 5:12).
7. Analawa imfa (kulekana ndi Mulungu) chifukwa tchimo ndi mayi wake wa imfa (Aroma 5:12).

C. Kudzera mchikhulupiriro mu mphatso ya chilungamo, Yesu anabwezeranso kwa ife china chili chonse chomwe Adamu anachitaya (Aroma 5:17).

1. Khristu anali kuunika komwe kunapambana mdima (Yohane 1:5; Machitidwe a Atumwi 10:38).
 - a. Kakhalidwe ka dziko momwe Khristu ankabwera (Mateyu 4:16).
 - b. Kakhalidwe ka omwe alibe Khristu (Aefeso 2:1-2; 4:17-18).
 - c. Yesu anayambitsa njira ya moyo wa tsopano womwe sakanatha kukhala nawo mdierekezi.
2. Khristu amatipanga ife kukhala amodzi ndi Iye (Aefeso 2:13-16)
3. Chilungamo chimabwezeretsa kufatsa, kupuma ndi mtendere ku mizimu yathu (Yesaya 32:17-18, 54:13-14; Aroma 5:1).
 - a. Opanda chilungamo kapena oipa alibe mtendere (Yesaya 57:20-21).
 - b. Mtendere wa Mulungu siufana ndi mtendere wa dziko lino lapansi (Yohane 14:27).
 - c. Umo m'mene ungasungire mtendere wako (Afilipi 4:6-8).
4. Chilungamo chimatipangitsa ife kuiwala maganizo akusowa kwathu.
 - a. Kusowa kwa ndalama.
 - b. Kusowa kwa mphamvu.
 - c. Kusowa kwa chikondi.
5. Chilungamo chimabwezeretsa ufula wathu weniweni.

III. MITUNDU IWIRI YA CHILUNGAMO (Afilipo 3:9).

A. Poyerekeza chilungamo cha Chipangano Chakale ndi Chatsopano.

1. Chilungamo chinali lonjezo kwa onse a Chipangano Chakale popherezera (posunga, kukwaniritsa) lamulo.

2. Lonjezoli linakwaniritsidwa ndi Khristu. Pakali pano tinapangidwa kukhala chilungamo cha Mulungu mwa Khristu (2 Akorinto 5:21).

B. Kuyerekeza Ubale ndi Chiyanjano (1 Yohane 1:9, 3:21).

1. Anyamata ambiri ndi atsikana salandira chikhululukiro koma amayenda ngati antchito osati ana. Kumbukani (osaiwala), tchimo limamusiya munthu wopanda mphamvu mpaka avomereza (atalapa) tchimolo.
2. Ndi ana okha angathe kulimbana ndi umphawi, matenda ndi tchimo.
3. Ndi ana okha omwe angathe kusangalala ndi malonjezo a Mulungu.

IV. KUYENDA MCHILUNGAMO CHAKO

A. Chenjera ndi chinyengo cha Satana (Yohane 10:10; 2 Akorinto 2:11; Chibvumbulutso 12:9).

1. Satana anamchititsa Adamu kuti asachite zoyenera mu chiyanjano chake ndi Mulungu.
 - a. Mulungu anampatsa adamu ulamuliro wosunga (kuyang'anira) munda ndi kugonjetsa dziko lapansi (Genesis 1:28, 2:15).
 - b. Mulungu wakupatsani inu ulamuliro (Marko 16:15; Luka 10:19).
 - c. Monga lye aliri, ndi momwemonso ife tiliri padziko pano (1 Yohane 4:17).
 - d. Wokhulupirira atchedwa Khristu (2 Akorinto 6:14-15).
2. Satana amakunyengani inu ndi:
 - a. Pokupangitsani inu kukhulupirira zomwe sizili zoon.
 - b. Pokupangitsani inu kulephera kuchita pa zomwe mumadziwa (Mateyu 7:24-27; Yakobo 1:22).

B. M'mene tingayendere mchilungamo:-

1. Dziwa kuti pamene wabadwa kachiwiri, umakhala mchigwirizano (chiyanjano) ndi Mulungu (2 Akorinto 5:17).
2. Koma uyenera kuchitapo kanthu ndi thupi lako ndinso maganizo ako (Aroma 12:1-2). Kukonzanso maganizo mwatsopano mwina ndi chomwe chili chosowa chachikulu kwa wokhulupirira - obandwanso mwatsopano.
3. Ungathe kukhala wolungama ndikudziwa kuti ndiwe wolungama komabe osanetsa kapena kugwiritsa ntchito chilungamo chako. Chitsanzo cha ichi tingathe kuchipeza mu fanizo la Mwana Wolowerela (Wotayika). Mwana wamwamuna wamkulu sanachite moyenera ndi momwe iyeyu akanachitira (analili) (Luka 15:25-31). Komabe, ngati muyenda moyenera ndikugwiritsa ntchito chilungamo, sungasunthidwe ndi wina aliyense kapena chinthu china chili chonse.
4. Simukula m'chilungamo koma m'makula m'chidziwitso ndi muvumbulutso la chilungamo chanu.

V. ZIPATSO ZA CHILUNGAMO

A. Mbali ya zochita kapena kuchita chilungamo ndi moyo wanu wa mapemphero (Yakobo 5:16:18).

B. Zipatso za Chilungamo.

1. 2 akorinto 9:10, safotokoza kokha za khalidwe ndi kulankhulana kapena chikhalidwe cha moyo komanso kuchita ntchito za Yesu (Yohane 14:12). Munthu amene adziwa chilungamo chake komanso nkusamachichita chilungamo ali ngati munthu amene ali ndi ndalama zambiri ku Banki koma osamazingwiritsa ntchito ndalama zakezi zothandiza amene agwidwa ndi umphawi ndinso amene akumwalira pa dziko.

VI. M'MENE MULUNGU ANATIPANGIRA IFE KUKHALA OLUNGAMA

A. Chinachitika nchiyani pa mtanda (Yesaya 53:4,5).

1. Iye anagonjetsa tchimo pamene analola tchimo kumugonjetsa (2 Akorinto 5:21).
2. Iye anagonjetsa imfa pamene analola imfa kumugonjetsa.
3. Iye anagonjetsa nthenda pamene analola nthenda kumugonjetsa, (1 Petro 2:24).
4. Iye anagonjetsa Satana pamene analola Satana kumugonjetsa lye.

B. Tinazindikiridwa (kufanizidwa) ndi Khristu mu imfa Yake, kuikidwa kwake m'manda ndi kuuka kwake kwa akufa.

1. Pamene Yesu anagonjetsa Satana ndikumuvula mphamvu zake (Akolose 2:15), m'maganizo a Atate zinali ngati kuti ndi iweyo wachita zonsezi.
 - a. Pamene Khristu anafa, munafa naye pamodzi (Akolose 2:20, 3:3).
 - b. Pamene Khristu anauka, munauka naye limodzi (Aefeso 2:5-6; Akolose 2:13, 3:1).
2. Lero ndinu mbuye wa satana monga momwe Yesu analiri pamene ankauka kwa akufa.
 - a. Satana amaopa chilungamo kwambiri kuposa chinthu china chili chonse.
 - b. Limbani mtima (mukhale okondwera) moyo wanu wa mantha wafika pa mapeto ake - Watha.

KUMVETSETSA ULAMULIRO

"Ndipo pamene zonsezo zagonjetsedwa kwa Iye, pomwepo Mwana yemwe adzagonjetsedwa kwa Iye amene anamgonjetsera zinthu zonse kuti Mulungu akhale zonse mu zonse" (1 Akorinto 15:28).

I. KUGONJERA KU ULAMULIRO, CHOFUNIKIRA KU MOYO WOPAMBANA WA CHIKHRISTU

A. Ulamuliro wapamwamba kwambiri ndiye Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Mulungu Mzimu ndi Mau ake.

1. Awa ndiwo maulamuliro odziwika olunjika m'moyo mwanu.
2. Ulamuliro wosalunjika kapena woperekedwa, umapatsidwa kwa anthu ndi maudindo.

B. Kuukira ku ulamuliro wa Mulungu (wodziwika kapena mosadziwika) ndiko kuukira koonekeratu motsutsana ndi Mulungu Mwini Wake.

1. Adamu ndi Hava (Genesis 2:17-3:19).
2. Lusifala (satana) (Yesaya 14:12-15).
3. Sauli (1 Samueli 15:1-23). Kuukira ndiye monga ngati tchimo la ufiti (ndime 23).
4. Chotsatira chakuukira ulamuliro iwo anataya malo (udindo) wawo.

C. Ndi ulamuliro zimadza udindo ndi kuziwerengera

1. Ntchito yakupereka ulamuliro (mphamvu ndi kuziwerengera) kuimilira m'malo.
2. Pali mbali zitatatu za ulamuliro.
 - a. **Ulamuliro wotheratu:** Kutha kuchita kanthu mopanda kuuza wachikulire.
 - b. **Ulamuliro wosapitirira:** Utha kuchita kanthu monga waonera kuti ndi koyenera pokhapokha ngati wachikulire adzauzidwa pambuyo pake.
 - c. **Wopanda ulamuliro:** Palibe kanthu kangathe kuchitika popanda kuyang'anidwa ndi wachikulire.

II. MAULAMULIRO OKHAZIKITSIDWA NDI MULUNGU (ULAMULIRO WODZIWIKA)

A. Maulamuliro okhazikitsidwa ndi Mulungu m'dziko lapansi (Aroma 13:1, 1 Petro 2:13-14).

1. Chilamulo
2. Olamulira

B. Maulamuliro oikidwa ndi Mulungu m'banja.

1. Mwamuna ndiye ulamuliro wapamwamba koposa m'banja (Genesis 3:16; Aefeso 5:23).
 - a. Mwamuna adzasiya atate ndi amayi ake kutenga chisamaliro cha banja lake latsopano (Genesis 2:24; Aefeso 5:31).
 - b. Abrahamu ndi Loti analekana chifukwa cha kutsenderezeka ndi mavuto opezeka ndi kukula kwa banja (Genesis 13:1-12).

- c. Mwamuna ayenera kukonda mkazi wake monga Khristu anakonda mpingo (Aefeso 5:25).
- 2. Akazi kwa amuna awo. (1 Petro 3:1).
- 3. Ana kwa makolo. (Aefeso 6:1-3).
 - a. Makolo ali ndi mphamvu (udindo) yakuwaphunzitsa ana awo (Genesis 18:19; Miyambo 22:6).
 - b. Tiyenera kuwayang'anira bwino ana athu kuti tiwaphunzitse iwo (Miyambo 19:18; 22:15; 13:24; 23:13-14; 29:17).

C. Maulamuliro oikidwa ndi Mulungu mu Mpingo (Aefeso 1:22-23).

- 1. Ntchito kapena mphanzo za utumiki (Aefeso 4:11).
- 2. Ulamuliro mu mpingo umakhala panso pa mutu wa Mbusa (Machitidwe a Atumwi 20:28)
- 3. Oyang'anira, othandizira azibusa ndi akulu amasankhidwa ndi Mbusa kapena Mtumwi (Machitidwe a Atumwi 4:23; Tito 1:5).
- 4. Otumikira (atumiki) amasankhidwa ndi mpingo (Machitidwe a Atumwi 6:5-6).
- 5. Zofunikira ndi zoyenera za akulu ndi atumiki (1 Timoteo 3).

D. Maulamuliro oikidwa ndi Mulungu pa ntchito: Olembedwa ntchito kwa owalemba (akapolo kwa Mbuye wao) (Aefeso 6:5-7; 1 Timoteo 6:11; Tito 2:9-10).

E. Maulamuliro oikidwa ndi Mulungu m'moyo mwako: Chikumbumtima kapeka Mzimu (Machitidwe a Atumwi 24:15; 1 Timoteo 1:18-19).

- 1. Kuononga dala Chikumbumtima chako kudzalocha (kupsereza) ndi kuumitsa icho (1 Timoteo 4:1,2).
- 2. Mtima wofewa udzatulutsa makhalidwe abwino. Chikumbumtima chofewa ndi cha changu chimakula pakuchita Mau a Mulungu, kugonjera ku ulamuliro wapambamwa, kupemphera mu Mzimu ndi kumvera nthawi ndi nthawi mau a Chikumbumtima chako.
- 3. Chikumbumtima cholochedwa (chopserezedwa) chimayamba ndi maganizo ako (2 Akorinto 10:5).

III. ULAMULIRO WOPEREKEDWA (ULAMULIRO WOSADZIWIKIRA)

A. Mbali (njira) za woyimirira (kutenga malo awina): Chiyani ndiponso nthawi iti muyenera kupereka kwa wina (kuimirira m'malo)?

- 1. Pamene mavuto ali kumangopitirirabe mwa iwo okha.
- 2. Zokambakamba zing'onong'ono zochitidwa mochulukira.
- 3. Mfundo zotenga magawo akulu a nthawi yako.
- 4. Magawo a ntchito yanu mwa zimene simungathe kuchita moyenera panokha.

B. M'mene mungagawire (kupereka)

- 1. Sankhani munthu woyenera pa udindowo.
- 2. Musapereke mopitirira usinkhu wa munthu (mochulutsa). (Mateyu 24:45-47).

3. Tengani nthawi yabwino kuika (kukwaniritsa) maudindo.
4. Perekani maudindo mavuto asanafike.
5. Kumanani nawo oimirira anu nthawi isanafike (mwachutchutchu).
6. Gwirizani momveka bwino.

C. Kufunika kwa kugwirizana.

1. Fotokozani kufunikira kwa kuimirira (kugawira ntchito) m'malo.
2. Gwiritsani ntchito kuimira m'malo kuthandizira olembedwa ntchito kuchita mopyolera ntchito yao.
 - a. Ichi chidzathandizira olembedwa ntchito kuphunzira zambiri.
 - b. Ntchito zoperekedwa, zingapereke chikwaniritso cha ntchito yoposa.
 - c. Kupatsidwa ndi mphoto ya ntchito yabwino.
3. Fotokozani momveka ntchitoyi (Genesis 6:9-22; Yoswa 6:1-5).
4. Pamene mwasindikiza, (mwapereka), funsani oimirira ngati akumvetsa.
5. Onetsetsani zotsatira, osakhala njira za kachitidwe.
6. Funani malangizo (umboni) m'madela omwe ali ovuta kuchokera kwa oimirira ena.
7. Musakhale opeza zifukwa pa ena.
8. Mukhale ndi anthu mwa chikondi, ulemu ndi molemekezana.
9. Musakhale wolemekeza anthu mwa sankho kapena kuonetsa kukondera (Aefeso 6:9; 1 Timoteo 5:21).
10. Perekani malipiro mu nthawi yake (mwa changu) (Akolose 4:1; 1 Timoteo 5:8).

D. Mbali (udindo) ya Woimilira: Mungakhale bwanji opindulitsa kwambiri kwa munthu wa Mulungu amene mukumugwirira ntchito (2 Timoteo 4:11).?

1. Mutumikireni iye, "monga kwa Ambuye" (Akolose 3:23).
2. Zindikira anthu omwe ali pamwamba pa iwe.
3. Khala mu udindo wako osalowerera wa ena. (1 Timoteo 2:12). Pamene thupi lilanda ulamuliro wa Mzimu, umakhala ndi chosayenerera m'moyo mwako. Chimodzimodzi pamene watenga ulamuliro umene suli wako izi zimachitikanso.
 - a. Chita chomwe anakutengera kuti uchite.
 - b. Tsamira ndi kuganizira za ntchito yoposa yabwino yomwe ikuchitika.
 - c. Uzipempherera mavuto omwe uli nao.
 - d. Lankhula kwa okulamulira. Tsimikiza kuti uli ndi mfundo zonse.
4. Zindikira kuyenda kwa bwino kwa ulamuliro mu mpingo kapena utumiki.
5. Peza (pindula) chikhulupiriro (chidaliro) chao.
6. Khala wophunzitsika ndi wotheka kukonzedwa.
7. Usataye (kulumpha) chikhalidwe (Machitidwe a Atumwi 9:5).

8. Usakhale wopereka malangizo pa china chili chonse.